


# NTHAWI YOKOLOLA

 Zikomo inu, M'bale Williams. Mmawa wabwino, abwenzi. Ndi chamwayi kukhala pano mmawa uno. Ndipo kukhala ndi mawu oyambirira monga awa, zimandipangitsabe ine kudzimva kukhala wochepa. Ndipo ndine...ndinali woyamikira kwambiri chifukwa cha mwayi uwu kuti ndibwere, mmawa uno, ku Phoenix.

<sup>2</sup> Ine ndikukumbukira pamene ine ndinabwera koyamba ku Phoenix, ine ndinali pafupifupi usinkhu wa zaka seventini. Ndithudi yakula kuyambira nthawi imeneyo. Kutuluka mmawa uno pamene timabwera mu Phoenix, ife timalephera kusiyantsa pamene ife timasiya Tucson ndi kufika ku Phoenix. Atsala pang'ono kulumikizana pamodzi, malo ambiri aphukira. Malo amene ife tinkakonda kupitako kuno ndi kuthamangitsa abulu aang'ono mchipululu, ndipo tsopano kuli ma motelo ndi masitolo a masenti-teni, ndi zina zotero. Ndipo, ndithudi, izo zikundipangitsa ine kukalamba.

<sup>3</sup> Ndipo kenako ine ndinakhala pansu apa pambali pa m'bale wanga wabwino apa, M'bale Valdez, ndi ine—ine ndinati, “Chabwino, m'bale . . .” Ife tinali kuyankhula, ndipo ine ndinati, “Chabwino, ndithudi, ine ndikukalamba.” Ine ndinati, “Ine ndikuzindikira kuti, ma mailosi anga akuchulukana.” Ine ndinati, “Iwe udikire mpaka udzafike usinkhu wanga,” kapena chinachake chonga icho. Ine ndinali—ndinadabwa kumva kuti iye anali wamkulu pafupifupi zaka thwelofu kundiposa ine. Chotero, ine, ndiye ine ndinamverera bwinoko pamenepo. Ine ndinati, “M'bale Valdez, ine ndikufuna inu . . . Kodi mwakhala mukulalikira Uthenga kwa nthawi yayitali bwanji?”

Iye anati, “Zaka fifite.”

<sup>4</sup> Chabwino, ine ndinali mwana wamng'ono kwambiri pamene iye ankalalikira. Chotero ine ndinati, “Ine ndikanakonda inu mukanangotenga msonkhano mmawa uno, M'bale Valdez.” Ine ndinati, “Ine—ndine mnyamata wachichepere,” Ine ndinati, “Sindimakonda kukhala pano ndi kuyesera kuyankhula,” ine ndinati, “akuluakulu anga.”

<sup>5</sup> Ndipo iye anangoseka, anati, “Inu mukuganiza kuti ndayendetsa kubwera kuno chifukwa chiyani?”

<sup>6</sup> Chotero ndine woyamikira kwambiri chifukwa cha M'bale Valdez. Iye amandiuza ine zokhala ndi nyumba yopumulira kunja kuno. Ndizo—izo ndi zabwino kwenikweni. Ine ndikuyamikira zimenezo. Anandiyitana ine kuti ndibwere kudzacheza nawo nthawi ina. Ndipo iyo ili kunja kuno pafupi ndi New River. Ine sindikudziwa ngati aliyense wa inu akudziwa

kumene iyo ili, kapena ayi. Ndikutsimikiza, ngati Valdez ali kuseri kwake, izo ziri bwino.

<sup>7</sup> Chotero ndiye, nthawi iliyonse ndikabwera ku msonkhano, kawirikawiri ndimakumana ndi winawake amene—amene anachiritsidwa mu misonkhano kapena chinachake. Ndipo pamene ine ndinaima pano pa tebulo mmawa uno, mlongo wofunika wakhala apa, dzina lake Erb, iye amachokera ku Michigan. Mwana wake wamwamuna ndi muwulutsi kuno pa sitieshoni ya Chikhristu iyi. Ndipo iye amandiuza ine za kukhala mu msonkhano kumbuyo uko mu Flint, Michigan. Iye anali ndi khadi la pemphero, ndipo ankayesera kuti apemphereredwe, ndipo iye sanakanwitse kutero. Ndipo iye akudwala kwambiri. Ndipo pomwe pano mmawa uno, ine ndikukhulupirira Mulungu anamuchiza mkaziyo, wayima pomwe pano pambali pa malowa.

<sup>8</sup> Ine ndinati, “Ndi nthawi yotani tsopano! Izo zakhala ziri pafupifupi thwelofu, zaka fortini zapitazo, ndipo tsopano mu mzinda wotchedwa Phoenix, Phoenix ndi winawake umene wamangidwa—wamangidwa kuchokera ku mabwinja.” Ine ndinati, “Chabwino, ndicho chinthu chomwecho chimene chachitika kwa iwe mmawa uno. Mulungu wakumanga iwe, ine ndikukhulupirira, mmawa uno, kuchokera ku a—thanzi labwinja kudzakhala thanzi labwino.”

<sup>9</sup> Ine ndimangomvetsera dzulo usiku, mafoni amabwera, ochuluka kwambiri. Ndine woyandikana nanu tsopano, ndikukhala ku Tucson ndipo mafoni anali ochuluka kwambiri sindikanatha kuwayankha onse, chotero ine ndimangowapempherera iwo pa foni. Ndipo iwo, ndiye, iwo amangoyenera kusiya manambala awo.

<sup>10</sup> Ndipo panali dona, usinkhu wa zaka eyite-seveni, Mkhristu wachikulire, iye anali atasokonezeka malingaliro kwa kanthawi. Iye anali mu msewu, akukuwa, ndipo akuyitana apolisi, kuti winawake wamutengera mwana wake. Usinkhu wa zaka eyite-seveni, mwaona, malingaliro ake anali atamuchokera iye. Ndipo iye anali mkazi wachikulire wokondeka. Ine sindimamudziwa konse iye mmoyo wanga. Ndipo chotero Billy anayimba, ndipo anati, “Mupite mwamsanga kokapemphera,” anati, “mayiyo wadwalika, ndipo iwo akuganiza kuti iye afa.” Anati, “Iye basi . . . iye salinso iyeyo.”

<sup>11</sup> Kenako ine ndinangodula foniyo, ndipo ndinapita mchipinda ndi kukapemphera. Mu mphindi pang’ono, iye anali mtulo. Iye anadzuka, ali bwino bwino, anadya chakudya chamadzulo cha nkhu yathunthu, ndi ayisikrimu yense ndi keke, pambuyo pake. Eya.

<sup>12</sup> Inu mwaona, Mulungu ndi wochita mwayekha. Iye ndi weniweni, Iye akhoza . . . Inu simukuyenera kukhala pamenepo; basi—kungopempha ichi.

13 Ine ndikukhulupirira mtsogoleri wathu pano, mmawa uno, kapena winawake, kapena mwinamwake anali M'bale Valdez mu pemphero lake, anati, "Ife sitimakhala nazo chifukwa sitimapempha. Ife sitimapempha chifukwa ife sitimakhulupirira."

14 Ine ndikuyamikira kuyimba kwa achinyamata awa pano. M'bale Valdez, ife anthu okalamba, timachitira umboni za kuwona mtima kwa mnyamata ameneyo akupereka umboni umenewo, kuti ankamudziwa Yesu.

15 Tsopano ife tikudziwa kuti ife timapeza, nthawi zambiri, makorteti aang'ono awa ndi zoyimba, ine. . . awa ndi mawu a mtumiki wina, M'bale Valdez anati, "Nthawiyina iwo amabwera ochepa thwelofu." Chifukwa, iwo akuwoneka ngati, lero, izo—izo zakhala chiwonetsero mmalo mwa—kupatulika ndi kuwonamtima kumene apentekoste anali nako.

16 Ndipo kuwonamtima kwa anyamata awa, ine—ine ndinayamikira zimenezo. Ambuye akudalitseni inu anyamata. Ndipo ine ndinali. . .

17 Ine sindikhala mochuluka pa televizioni. Monga inu mukudziwira, ine ndimatsutsana nayo iyo kwenikweni. Ndipo kwenikweni ndimakhala malo obwereka ku Tucson mpaka ife titakonzala malo athu, kumene ife tidzakhazikitse nyumba yathu kumeneko, Ambuye akalola. Ndipo dona amene amabweretsa nyumbayo, iye ndi bwenzi labwino la Chikhristu, koma iye anali ndi a—a—televizioni mnyumbamo. Chabwino, ine ndiri ndi ana aang'ono, ndipo inu mukudziwa momwe iwo amakhala, chotero iwo amathamangira kwa iyo. Chotero, mmawa ungapo wapitawo, pamene ine ndinangobwera kumene kuchokera ku ulendo ndi M'bale Stromei. . . Ine sindikudziwa ngati M'bale Stromei ali pano mmawa uno, kapena ayi, iye ndi purezidenti wa gululo ku Tucson. Mwana wanga wamkazi wamng'ono, amene wakhala kumbuyo kuno, anandiyitana ine kuti ndikawonere, anati, "Ife tiyatsa televizioni, ma korteti ena ayimba," kapena chirichonse chimene icho chinali.

18 Chabwino, tsopano, ine ndine wotsutsa wabwino kwambiri, ndipo ine—ine ndikupepa chifukwa cha izo, koma ine—ine—ine sindingakhale chirichonse koma chimene ndinapangidwa. Ngati ine ndingachite chinachake chosiyana ndi mapangidwe anga omwe, ndine wachinyengo. Ndipo ine ndingafune kukhala chimenecho pamaso pa anthu inu. Ine—ine ndikufuna ndingokhala chimene ine ndiri, ndiyeno inu nkungodziwa momwe ife tikuimira. Ndipo ine—ine ndikuganiza kuti ndimatsutsa pang'ono kwambiri.

19 Koma ine ndinangokhala nazo mu mtima mwanga kuti nditsutse izo, chifukwa izo zinkangowoneka kwa ine ngati mtundu wina wa Hollywood utavalidwa, basi zochulukana za zotengeka. Izo sizinawoneke ngati kupatulika kumene

kumayenera. Ndipo iwo ankayimba nyimbo zimenezo mu—mu nthawi ya gwedemula, ndipo atavala mapatapata agolide. Ndipo kodi izo zafika kuti Uthenga wasanduka chiwonetsero? Bwanji, ine, ngati icho ndi chimene chiri, ine—sindikufuna kanthu kochita nazo izo. Ine ndikufuna chinachake chimene chiri chenicheni ndi chapachiyambi, ndipo tikufuna kuchisunga mwanjira imeneyo.

<sup>20</sup> Tsopano, ine—ine ndikukhulupirira kusintha uku kwa ziwiri izi pomwe apa, abale. Kuti, mukundimva ine bwino bwino tsopano?

<sup>21</sup> Tsopano, Loweruka likubwerali mmawa, Ambuye akalola, ine ndidzakhala ndi mwayi waukulu wokayankhula ku chaputalacho, nthawi yanga yoyamba, ku Flagstaff, Arizona. M’bale pano, ndangoyiwala dzina lake, ndi purezidenti. [M’bale akuti, “Chester Earl.”—Mkonzi]. Chester Earl, M’bale Chester Earl. Ndinangopeza mwayi wokumana naye iye mmawa uno, pamene ine ndimangogwirana chanza ndi mlaliki wabwino kuno wochokera ku India, m’bale wa Chimwenye. Ndipo iye ananena kuti Loweruka likubwerali mmawa ine ndikayankhula kumeneko. Inu nonse mukuitanidwa kuti mukakhalepo pa msonkhano uwu. Tikuyembekeza kuti Ambuye akatidalitsako ife.

<sup>22</sup> Ndipo kenako Lolemba lotsatira usiku, ku Tucson, kukakhala phwando. Ambuye andipatsa ine ulemu woti ndidzakayankhule kwa a...pa phwando kumusi uko, tsiku la twente-wani la—la Disembara, ku Tucson. Inu ndithu muli oitanidwa mwachikondi kuti mukakhale nawo usiku wa phwando umenewo.

<sup>23</sup> Ndiyeno monga M’bale Williams analengezera kuti ine ndine woti ndidzabwererenso kuno, kuti ndidzakhale ngati kalambulabwalo pang’ono msonkhanowo usanayambike.

<sup>24</sup> Ndipo, chotero, kodi ine ndikupeza kusamveka pamenepo, M’bale Williams? Apo pali...Mukuti chiyani? Kodi pamenepo ziri bwino tsopano? Ziri bwino. Chabwino.

<sup>25</sup> Ine ndithudi ndikuyembekeza kuti ambiri a inu mungapeze nthawi yobwera ku umodzi, kapena usiku uliwonse ndi usana, wa msonkhanowo. Umene, umene udzayambe pa senventini, pa seveni, Lamlungu madzulo? [Winawake akuti, “Wani-sarte.”—Mkonzi]. Wani-sarte. Wani-sarte, Lamlungu madzulo. Ine ndikufuna kunenanso, ngati Ambuye alola, Ine ndidzakhala ndikupempherera odwala mu—mu—mu misonkhano imeneyo, ndi kuchita zonse zimene ine ndingathe kuti ndikuthandizeni inu.

<sup>26</sup> Ndipo abale otumikira pano, mmawa uno, a dera la Phoenix. Chifukwa chimene ine ndabwera kuno ku holo iyi, ine... Nthawi iliyonse imene ine ndibwera, kawirikawiri ndimawona malo pang’ono, ndi kuthamangira ku matchalitchi, tchalitchi

chirichonse. Kenako ine ndimazipeza izo kukhala zovutirapo, chifukwa matchalitchi ena ali ngati aang'ono. Ndipo ife ndithudi sitimafuna kumusiya m'bale aliyense chifukwa tchalitchi chake ndi chaching'ono, ndiyeno zimapangitsa izo kukhala zovuta, anthu amalephera kuti alowe. Chotero ngati. . . Ine ndinaganiza kuti tingokumana pamalo amodzi ndipo ine ndisamalira izo inemwini, ndipo tidzangokumana pano ndi kudzakhala ndi msonkhano, msonkhano waung'ono chabe wa uvangeri, ndi kupempherera odwala ndi zinthu. Tisanati. . .

<sup>27</sup> Mwinamwake ngati ine ndingapite pa inayi, iyi ili bwinoko apa? [Winawake akuti, "Ayi, iyo, imeneyo ndi tepi."—Mkonzi]. Imeneyo ndi tepi. Chabwino.

<sup>28</sup> Mwinamwake zingakhale a—zabwino pang'ono ngati ndingachite izo mwanjira imeneyo. Ndipo ine ndikufuna abale anga pano, a mipingo, azibusa kuno ku Phoenix, adziwe kuti ndicho chifukwa ife tinachitira izi, kuti tidzabwere kuno ku holo iyi, kuti ife tidzathe kukhala tonse titasonkhana pa malo amodzi. Ndipo iwe sungathe kufikira kwa abale onse, alipo ochuluka kwambiri a iwo. Inu munawawona amene anayima mmawa uno, ndipo mwinamwake iwo si theka la iwo. Chotero iwe sungathe kuwabweretsa iwo onse mmasiku pang'ono amene ife tiri nawo kuno, msonkhano usanachitike.

<sup>29</sup> Ndipo ine ndikutsimikiza kuti tikhala ndi nthawi yabwino pa msonkhanowu. Inu mudzawamvetsera oyankhula abwino. M'bale Cash uyu ndi Cash Hamburg, Hamburg. Mai, ndi angati anamumvapo iye? Iye ndithudi ndi—mkuntho. Eya. Pepani, ine sindimayenera kuti ndinene zimenezo mwanjira imeneyo. Uyo ndi m'bale, koma—koma, mai, ine ndinali ndi iye nthawi ina. Inu mukudziwa, ine sindikuwona momwe inu mumabwerera konse kuti mudzandimve ine, pamene inu mumumva munthu ngati ameneyo. Iye akhoza kulalikira ndipo izo sizimamutengera konse mpweya wake. Ine—ine sindikudziwa momwe iye amachitira izo, ine. . . koma iye ndithudi amapeza zambiri. Ine ndinapita naye mu msonkhano wanga wa ku New York, posachedwapa, ndipo iye ankafuna kunditengera ine—ku chakudya chamadzulo utatha msonkhano. Ndipo ine ndinapita ku maloko, ndipo ine ndinali pafupi kukonzekera kuti ndituluke pamene m'bale. . . Iye, iye amalalikira paliponse chokwera-ndi-chotsika pamene. . . Iye, iye paliponse akuzungulira, kwa aliyense amene anali pamene. Iye ndithudi—khalidwe, mwa iyemwini.

<sup>30</sup> Ndipo ine ndikutsimikiza inu mudzasangalala naye m'bale wochokera ku California, inunso. Dzina lake ndi ndani? Sindingathe kuganizira dzina lake, amene ndi mmodzi mwa oyankhula. Ine—ine ndaiwala dzina lake, inenso. Koma iye ndi a—woyankhula mwamphamvu, ndipo inu musangalala naye. Mwinamwake kudzakhala oyankhula opambana kumeneko monga, inu mukudziwa, M'bale Roberts ndi ambiri a amuna opambana a tsiku lino.

<sup>31</sup> Chotero, ndine wothokoza kuganiza za Lemba limene likubwera mmalingaliro anga pano pa nthawi ino. Ndipo pa nthawi ina Davide ankayang'ana kunjja pa likasa la Ambuye, litakhala mu mahema. Ndipo iye anati...Iye anali atakhala ndi mneneri, Natani, wa tsiku limenero. Ndipo chotero iye anati, "Kodi ndikoyenera kuti ine ndizikhala mnyumba muno, kumakhala mnyumba ya nkungudza, ndipo likasa la pangano la Ambuye wanga kumakhala pansu pa hema?"

<sup>32</sup> Ndipo mneneriyo anati kwa iye, "Chita zonse zimene ziri mu mtima mwako, Davide, chifukwa Mulungu ali ndi iwe." Ndizo zonse zimene iye ankadziwa kuti anene.

<sup>33</sup> Koma usiku umenewo, Ambuye anakumana ndi mneneri, ndipo anati, "Pita, ukamuuze wantchito wanga, Davide, kuti ine ndinamutenga iye ku khola la nkhosa, akutsatira nkhosa zapang'onozo, iwe ukudziwa, ndipo ndinamupangira iye dzina ngati amuna opambana," osati dzina lalikulu kwambiri, osati dzina lalikulu kwambiri, koma ndinamuwerengera iye ndi amuna opambana amene anali pa dziko lapansi pa nthawi imeneyo.

<sup>34</sup> Ndipo ndinaganiza, "Chisomo cha Mulungu, kwa Davide kumeneko!" Ndipo ine ndinaganiza, "Ine ndikhoza kuziwerengera izo, inemwini. Pamene ndapeza mwayi wa tsiku lino limene ife tikukhalamo, masiku otsekera a mbiriyakale ya dziko, ndipo nkuwerengedwa pakati pa amuna oterowo amene abwera pa misonkhano iyi." Ndipo Ambuye akudalitseni inu, mochuluka kwenikweni.

<sup>35</sup> Tsopano, mzanga wabwino, M'bale Valdez, anati, "M'bale Branham, ine ndikuyenera kuti ndizichoka pa, ine ndikukhulupirira, korta isanakwane teni, kapena korta pasiti teni." Anati, "Ine ndikhala cha kumapeto, kuti ndisakusokonezeni—ndisakusokonezeni mukuyankhula." Iye wakhalapo mmisonkhano.

<sup>36</sup> Ndine—Ine ndimakhala ngati wochedwerapo, ndipo ndimayenera kuganiza, inu mukudziwa, pamene ndikuyankhula. Ndipo ndimalemba Malemba anga apa, ndi cholemba, mwinamwake, komano ine ndimayenera kubwera ndi kuganizira chimene Ambuye anandiuza ine kuti ndidzanene, inu mukudziwa, ndimayenera kumuyembekezera Iye. Ndipo ine ndimakhala ngati wochedwerapo, chotero ine ndikuyembekeza kuti sindikusungani inu motalika kwambiri, mmawa uno.

<sup>37</sup> Ine ndinamufunsa M'bale Williams, ine ndinati, "M'bale Williams, kodi ndiri ndi nthawi yochuluka bwanji?" Ine ndinati, "Tsopano, ine ndinali ndi Lemba pano limene ine ndikanakhoza kuyankhulapo limene likananditengera ine pafupifupi maminiti sarte, kapena chinachake, ndi kubalalitsa aliynense ndi kumapita kunyumba." Ndipo ndinati, "Koma ndikufuna kukhala ndi phunziro laling'ono, ngati nkotheke," ndipo pa chimene ine

ndikuganiza icho chikanakhala chinachake kwa inu lero, chinachake chimene inu mukhoza kupita nacho kunyumba, kuti mukachiganizire icho.

<sup>38</sup> Ndipo ine ndithudi sindikanadzuka mmawa uno hafu pasiti firiri, kapena maminiti twente kufika foro, ndi kukonzekera kubwera kuno, kuti ndidzangowonedwa. Ine—ine—sindisamala kuti ndiwonedwe. Ine—ine ndinabwera kuno ndipo ndinadzaphunzira dzulo pa Malemba ena amene ine ndinawalemba, kwa chinachake chimene ine ndinachipempherera moonamtima, ndipo ndinaganiza mwinamwake kuti, kupyolera mu chimenecho, icho chikhoza kumuthandizira winawake. Ine...Ife tiribe nthawi ya ziwonetsero ndi zochitika. Ife—ifite tikuyenera kupita ku zenizeni. Ine ndikukhulupirira kuti Yesu akubwera posachedwapa.

<sup>39</sup> Ndipo tsopano iwo akujambula izi, ndipo mwinamwake winawake akhoza kudzatenga tepiyo. Ndipo ine ndikufuna kuti ndipange neno ili, kuti nthawizina ine ndi...nthawi zambiri ine sindimamvetsetsedwa. Ndipo nthawi zambiri anthu amandiyimbira ine, kumati, “M’bale Branham, kodi uku ndi kuwala kumene inu munkatanthauza?” Ndipo nthawizina ndi ife timanena chinachake, koma iwe umayenera kudziwa, kuchifikira icho ndi mawu amene ine ndimatanthauza ndi icho.

<sup>40</sup> Ndipo ine ndimanena zinthu nthawizina zimene—zimene zimakhala zotsutsana pang’ono mwinamwake ndi chikhulupiriro cha winawake, Ine ndikufuna inu mumvetsetse zimenezo tsopano, winawake, chimene winawake amakhulupirira. Koma ine ndiri ndi a—Uthenga, sindiri... wochokera kwa Ambuye, umene ndimamverera mwanjira imeneyo za izo. Ena akhoza kumverera kuti Iwo ndi wochokera kwa mdierekezi. Ena akhoza kumverera kuti Iwo ndi zamkutu. Koma, kwa ine, ndi Moyo. Ndipo sindikutanthauza kuti ndikhale wosiyana pamene ndikunena zinthu zosiyana, kapena mwinamwake zopweteka pang’ono kapena zocheke, kwa anthu. Ine sindikutanthauza izo mu kuwala kumeneko. Ine—ine, ngati ine ndingatero, ndiye ndine wachinyengo. Ine—ine ndikunena izo mu kuwala kwa kupita patsogolo, kwa Mulungu. Ine ndikunena izo mu kuwala kwa—kwa—kowapangitsa anthu kuti amudziwe bwino Mulungu. Ndi ndikunena izo osati chifukwa chakuti ndi chimene ine ndachipanga, inemwini. Ndi chinachake chimene ndachipeza kuchokera kwa Mulungu.

<sup>41</sup> Ndipo tsopano ngati ndingapezeke ndikuyankhula pa chinachake mu uliwonse wa misonkhano iyi, chimene chikuwapweteka anthu, kapena...Kuti, “Ine sindimakhulupirira Izo mwanjira imeneyo.”

Chabwino, nthawi zambiri ndapangapo neno lamwano ili. Ndipo mkazi wanga wakhala apoyo akundimvetsera ine, iye akudziwa kuti palibe machitidwe ochuluka okhudza ine. Ine—

ine . . . Chimodzimidzi monga mukudya nkhuku, ndipo ukaluma fupa. Tsopano, palibe wokonda nkhuku wabwino amene angataye nkhukuyo chifukwa waluma fupa. Iye amangotaya fupalo, kenako iye amapitirira kumadya nkhukuyo. Chinthu chomwecho pakudya chitumbuwa cha nthudza. Ngati ine ndiluma nthanga, ine—ine—ine sindimataya chitumbuwacho, ndimangotaya nthangayo. Chotero . . .

<sup>42</sup> Ndipo zimene ine ndinganene pano zimene zikhoza kuwoneka ngati, mu iliyonse ya misonkhano yanga, zimene zingawoneke ngati nthanga kwa inu, chabwino, mungoziyika izo pambali, ndipo, nkuti, muziyike zimenezo kwa ine kuti ndi wosadziwa zambiri za izo monga momwe inu mukudziwira. Chotero, ndiye, inu musingopitirira ndi kumadya zimene mukuganiza kuti ndi zolondola. Ndipo ine ndi . . .

<sup>43</sup> Ine ndikudalira tsopano kuti Ambuye adalitsa Mawu Ake. Ndine wokhulupirira wolimba mu Mawu, ndipo Mawu okha. Mawu okha basi, ndipo ndiwo Uthenga umene Ambuye andipatsa ine.

<sup>44</sup> Ife timasiyana, wina ndi mzake. Ine ndazindikira mmawa uno, abale anga, amishonare, alaliki, ndi azibusa, ayima pano, mwinamwake—mwinamwake handirede kapena kupitirira a iwo, ayima pano. Aliyense wa iwo ndi woyenera kwambiri kuyima pano ndi kudzayankhula, kuposa momwe ine ndingachitire. Ndine wotsimikiza za izo. Koma, mwawona, aliyense wa ife, mmodzi sangatenge malo a wina. Wina sangatenge uthenga wa mzake. Mwaona, ife tiri nazo njira zathu zosiyanasiyana.

<sup>45</sup> Mulungu ndi wochita mwayekha. Pamene Iye . . . Ndani, ndani akanamuza Mulungu momwe angapangire zinthu, pachiyambi, pamene kunali Iye yekha basi? Mukuona? Ndipo ngati ife tiri ndi Moyo Wamuyaya, ulipo mtundu umodzi wokha wa Moyo Wamuyaya, ndipo umenewo ndi Mulungu. Chotero ngati ife tiri ndi Moyo Wamuyaya, ife tinali ndi Mulungu nthawi imeneyo, gawo la Mulungu. Ife tinali chikhumbo Chake. Ife tsopano ndi chikhumbo Chake. Ndipo, chifukwa, “Pachiyambi panali Mawu.” Ndipo mawu ndi ganizo lofotokozedwa. Chotero ife tinali maganizo Ake, kenako tinadzafotokozedwa kudzakhala mawu ndi kudzakhala chimene ife tiri. Ndi chifukwa chake maina athu, mwinamwake osati amene tiri nawo tsopano, koma maina athu analembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Mukuona? Ndipo ngati kunalibeko kumeneko nthawi imeneyo, ilo silidzakhalako kumeneko. Mukuona? Ndipo Yesu anabwera kuti adzawombole onsewo, ndiwo, amene maina awo sali pa Bukhu limenero. Mwaona, Iye ankadziwa.

<sup>46</sup> “Wowumba,” monga Aroma 8 amatiuza ife, “ndani



angamuwuze wowumba? Kodi dongo linganene kuti, ‘Ndipangeni ine *motere, motere*?’” Mukuona? Ayi. Mulungu ayenera kuwonetsera zikhumbo Zake zonse. Ndipo chotero Iye akuyenera kupanga chotengera chimodzi chamanyazi, ndipo chinacho chaulemu, kuti awonetsere izo, ndithudi. Tsopano, koma Iye ndi wochita mwayekha, inu mwaona, palibe amene angamuuze Iye choti achite.

<sup>47</sup> Ndipo Iye amatipanga ife mosiyanasiyana. Ngakhale a...pamenepo, ife timauzidwa, mu Baibulo, kuti nyenyezi zimasiyanasiyana ina ndi imzake, nyenyezi imodzi imasiyana ndi imzake. Inu mukudziwa, kulipo kusiyanasiyana Kumwamba, mwa Angelo, Angelo a matupi; alipo Angelo, kuli Akerubi, kuli Aserafi, ndi kwawo—kusiyana kwawo Kumeneko. Ndipo tonse ndife osiyanasiyana. Ndipo Mulungu ali ndi mapiri aakulu, Iye ali ndi zigwa, zidikha, udzu, chipululu, madzi. Mwaona, Iye ndi—Iye ndi wosiyanasiyana, Iye ndi—Iye ndi—Mulungu wa zosiyanasiyana. Ndipo tayang’ana pa anthu Ake pano mmawa uno, ena a ife oyera, ena akuda, ena abulauni, ena achikasu, ena ofiira; mwaona, ndi—ndi anthu Ake. Iye ndi . . . Iye ndi—Iye ndi Mulungu wa zosiyanasiyana, ndipo chotero ine ndikuganiza Iye ali ndi chinthu chomwecho pakati pa atumiki Ake.

<sup>48</sup> Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi yokha, kwa pemphero. Ndipo ine ndikhoza kunena ichi tsopano ife tisanawerenge Mawu. Ndikudziwa kuti ndikangotalikitsa pang’ono, ndipo inu muyenera kuyimirira ndi kumatuluka, Ine ndimvetsa, mwaona, ine ndimvetsa bwino bwino. Tsopano tiyeni tipemphere. Ndipo pamene ife tikupemphera, ndi mitu yathu yoweramitsidwa ku fumbi kumene Mulungu anatitengako ife, alipo winawake pano amene akufuna kuti akumbukiridwe mu pemphero, ingokwezani dzanja lanu. Iye, Iye akudziwa kumene chimene chiri mu mtima mwanu, pansu pa dzanja limenero.

<sup>49</sup> Wokonedwa Atate Akumwamba, ife tikuyandikira kwa Inu mwaulemu, ndi mitu yathu itayang’ana ku fumbi kumene Inu munatitengako ife. Ndiyeno mmalingaliro athu ife tikuganiza kuti Inu munamuza Abrahamu, usiku wina, kodi iye angathe “kuwerenga mchenga umene unali mmphepete mwa nyanja?” Ndipo kenako Inu munamuza iye kuti “ayang’ane nyenyezi,” ndipo kodi angathe “kuziwerenga izo?” Ndithudi, izo zinali zosatheka. Ndipo Inu munamuza iye kuti yake “mbewu idzakhala yosawerengeka, ndipo munga mchenga wa mmphepete mwa nyanja, ndi pa nyenyezi zimene zimawunikira mmiyamba.” Tsopano malingaliro athu, ganizo lathu, maganizo athu mmalingaliro athu, kani, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu ku mchenga kumene ife tinachokerako; ndiye mitima yathu ikuyang’ana Kumwamba, kumene ife tikupitako. Kuchokera ku mchenga kupita ku nyenyezi, pokhala Mbewu ya Abrahamu! Akufa mwa Khristu, ndife Mbewu ya Abrahamu, ndi olandira pamodzi ndi Iye munga mwa lonjezo.

<sup>50</sup> Ndipo ife tabwera kuno mmawa uno kudzayanjana pa zakudya zachirengedwe za moyo, zimene tazitenga, kuti tizichotse izo panjirayo. Ndipo tsopano ife tikukhumba Inu kuti mutipatse ife Manna a Kumwamba amenewo, Chakudya chimenecho chimene chingatipatse ife mphamvu mu Moyo umene uli mwa ife. Pamene magazi akunyamula chakudya ichi tsopano, kuti chikawalimbikitse iwo, kukapanga timakhungu tochuluka, kukatimanga ife amphamvu kwa tsikuli; mulole ife tilandire za Khristu, kuti Iye athe kulowa mmizimu yathu, mmawa uno, kudzera mu Mawu, ndi—ndi kudzatilimbikitsira ife ku ora limene ife tikukhalamo. Chifukwa, tsiku latha ndipo mithunzi yamadzulo ikugwa, Kuwala kwamadzulo kuli pano, ndipo posachedwapa tizimva kuyitanidwa kuti “bwerani Mmwamba,” ndipo ife tikufuna kukhala okonzeka pa ora limenero. Chotero, tithandizeni ife, Atate.

<sup>51</sup> Ndipo palibe munthu woyenera kutsegula Bukhu, kapena kumasula Zisindikizo zake; koma Mwanawankhosa, amene anaphedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi, anabwera kudzatenga Bukhu ndi kumasula Zisindikizo. O Mwanawankhosa wa Mulungu, bwerani mmawa uno, mudzatsegule Bukhulo kwa ife, ndi kutilola ife kuyang’ana mkati ndi Inu, Ambuye, ndi kuwona chimene ife tikuyenera kuchita kuti tikonzekere ora lino. Mudalitse mpingo uliwonse, mudalitse misonkhano ikudzayi, uliwonse wa iwo, ndi msonkhano wathu wawung’ono, kuti tidzalumikizane ndi iyo imene ikubwera. Ndipo pamene ife tizichoka pano lero, mulole tithe kunena monga aja amene ankachokera ku Emau, “Kodi mitima yathu siinantenthe mkati mwathu, pamene Iye amayankhula nafe panjira?” Perekani izi, Atate. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>52</sup> Tsopano kwa inu amene mukufuna kuti mutsegule, kawirikawiri mumakonda kuwerenga kuchokera kuseri kwa mtumiki pamene iye akuwerenga, kuti mupeze pamene iye akuyankhulirapo, ngati inu muli ndi ma Baibulo anu, ndipo mutsegule ku Mateyu Woyera mutu wa 4.

<sup>53</sup> Ndipo tsopano ine ndipereka mutu wanga ndisanayankhule; mochuluka kapena mocheperapo, ndikufuna kuphunzitsa izo chomwecho, ndi kuziyankhula izo pamene ife tikupitirira. Ndipo izi ndazitcha, mwanjira ina, sindikudziwa chifukwa chake, kuti ndikuzitchula izi: *Nthawi Yokolola*.

<sup>54</sup> Ndipo ife titenga kuwerenga kwa Lemba, kuti tikhazikitsirepo lingaliro ili, kuti titengepo kuchokera apa nkhani ya mutuwo. Ife tiwerenga Mateyu Woyera mutu wa 4, gawo la iwo. Izi ziri mu mayesero a Yesu. Iye atadzazidwa ndi Mzimu Woyera, Iye anatsogozedwa kupita mchipululu.

Tsopano pamene Yesu anatsogozedwa ndi Mzimu  
kupita mu chipululu kuti akayesedwe ndi mdierekezi.

*Ndipo pamene iye anasala kudya masiku forte ndi usiku forte, pambuyo pake anamva njala.*

*Ngati iwe uli Mwana wa Mulungu, lamulira kuti miyala iyi ikhale mikate.*

*Koma iye anayankha ndipo anati, Kwalembedwa, Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.*

*Ndipo mdierekezi anamutengera iye ku mzinda woyera, ndipo anakamukhazika iye pamwamba pa nsonga ya kachisi,*

*Ndipo anati kwa iye, Ngati iwe uli Mwana wa Mulungu, udzigwetse wekha pansi: pakuti kwalembedwa, Iye adzalamulira angelo ake za iwe: ndipo mmanja mwawo iwo adzakunyamula iwe, kuti nthawi iliyonse iwe ungamenyetse phazi lako pa mwala.*

*Yesu anati kwa iye, Kwalembedwanso, Iwe usamuyese Ambuye Mulungu wako.*

*Ndipo kenanso, mdierekezi anamutengera iye ku . . . phiri lalitali kwambiri, ndipo anamuwonetsa iye maufumu onse a dziko lapansi, ndi ulemelero wa iwo;*

*Ndipo iye anati kwa iye, Zinthu zonsezi ndikupatsa iwe, ngati iwe unagwade pansi ndi kundipembedza ine.*

*. . . Yesu anati kwa iye, Choka apa, Satana: pakuti kwalembedwa, Inu muzilambira Ambuye Mulungu wanu, ndipo iye yekha inu muzimutumikira.*

<sup>55</sup> Ine ndikufuna kubwerera mmbuyo pang'ono pokha, ku ndime ya 4 kachiwiri.

*Koma iye anayankha ndipo anati kwa iye, Kwalembedwa, Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.*

<sup>56</sup> Tsopano kwa phunziro, ndikufuna kutenga zimenezo, “Mawu aliwonse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Tsopano mugwire zimenezo mu lingaliro pamene ife tikuyankhula.

<sup>57</sup> Yesu ananena nthawi ina, mu Yohane Woyera 6:48, ine ndikukhulupirira uko nkulondola, monga ine ndinazilemba izo mmawa uno, “Ine ndine Mkate wa Moyo.” Izi zinali paphwando la Paskha, pamene Ayuda anka—ankadya zopatulika zawo pokumbukira manna amene ankagwa mchipululu, ndipo—ndipo iwo anali akumwa kuchokera pa kasupe kumeneko kuimira Thanthwe limene linali mchipululu, ndipo iwo anali ndi nthawi yopambana. Ndipo Yesu anafuula mokweza, pakati, ndipo Iye

anati, “Ine ndi Mkate wa Moyo. Makolo anu anadya manna mchipululu, kwa danga la zaka forte, ndipo iwo aliyense, anafa. Koma Ine ndi Mkate umenewo umene umachokera kwa Mulungu kuchokera Kumwamba. Ngati munthu adyako, iye sadzafa ayi.” Ndipo kwa thanthwe, Iye anati, “Ine ndine Thanthwe lija limene linali mchipululu. Ine ndi Thanthwe lija limene makolo anu ankamwapo.”

<sup>58</sup> “Motani?” Iwo anati, “Ndiwe mwamuna wosapitirira usinkhu wa zaka fifite, ndipo ukunena kuti Iwe unamuwona Abrahamu? Tsopano ife tikudziwa kuti Iwe uli ndi mdierekezi ndipo ndiwe wamisala.”

<sup>59</sup> Ndipo Yesu anati, “Abrahamu asanakhalepo, INE NDINE.” Mwaona, “INE NDINE” anali Lawi la Moto limene linali mu chitsamba, chimene chinayankhula ndi Mose. Ndipo ngati inu mungakonze izo mu manauni ake ndi mapronauni, osati “Ine ndinali, Ine ndidzakhala.” “INE NDINE” amakhala nthawi yapano, nthawi zonse.

<sup>60</sup> Ife tikuganiza za izi, kuti Iye akunena, Iyemwini tsopano, kuti, “Ine ndi Mkate wa Moyo uja.” Tsopano zingatheke bwanji kuti munthu uyu akhale Mkate wa Moyo? Ndi chimene ife tikudabwa. “Thupi Langa ndi Mkate,” Iye anatero. Ndipo tsopano zingatheke bwanji kuti munthu uyu akhale Mkate? Izo ndi zachirendo, koma musadabwe nazo izo. Anthu a nthawi Yake anadabwa nazo izo. Iwo sankadziwa momwe munthu uyu akanakhala kwenikweni Mkate, Iyemwini. Ndiponso mu Yohane Woyera 1, zinaperekedwa kwa ife mwanjira iyi, kuti, “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Chotero, Mawu anadzakhala Mkate. Mawu ndi Mkate pano ziyenera kukhala zofanana, chifukwa Yesu ndi Mawu ndipo Iye ali Mkate.

<sup>61</sup> Tsopano Iye akanakhala bwanji Mkate ndi Mawu? Zonse. . . Izo zikanakhala zododometsa, kwa malingaliro achithupithupi. Koma ife tikuyembekeza, mmawa uno, kuti palibe malingaliro achithupithupi pakati pathu, kuti pali malingaliro auzimu pakati pathu, kuti ife tithe kumvetsa chimene Atate akuyesera kutibweretsera ife pano. Kuwona mawu awa ndi odabwitsa, koma, pa nthawi yomweyo, iwo ndi Choonadi cha Malemba, mwaona.

<sup>62</sup> “Tsopano munthu uyu angakhale bwanji Mkate?” Ndi chimene iwo ananena. Ndicho chimene, ine ndikukhulupirira, Josephus, ambiri a inu azambiriyakale. . . monga ine ndakhala ndikuphunzirira izo.

<sup>63</sup> Tsopano ndikulemba bukhu, ndemanga yanga pa mitu inayi yoyambirira ya Chivumbulutso, ndikuyembekeza kuti litulutsidwa posachedwapa. Ilo lidzakhala bukhu lalikulu.

Kenako ndidzakhala ndi kabukhu ka m'badwo uliwonse wa mpingo.

<sup>64</sup> Ndipo ine ndimaphunzira mbiriyakale ya mpingo. Ine . . . zinali ngati mmalingaliro anga, ine ndikukhulupirira anali Josephus, amene, mmodzi wa olemba oyambirira, mulimonse, amene ananena kuti, “Yesu uyu waku Nazareti, Amene ankayendayenda akuchiritsa odwala,” anati, “Ophunzira ake anamukumba Iye ndipo anadya thupi Lake.” Mwaona, iwo ankadya mgonero. Ndipo iwo ankaganiza kuti anakumba thupi Lake ndipo ankadya thupi Lake. Chimene, ife timadya mgonero, kapena kutenga mgonero, mwa chiphiphiritso, cha thupi Lake, chifukwa Iye anali Mawu.

<sup>65</sup> Tsopano, mwaona, izi ndi zododometsa. Ndipo, nthawi yomweyo, pali Malemba. Ndipo Yesu anati, “Malemba onse akuyenera kukwaniritsidwa.” Mukuona? Tsopano, ife tikufuna kuti nthawizonse tizidula malingaliro athu ku chirichonse chosiyana ndi Lemba limenero. Musadzatero konse, konse, nthawi iliyonse, kudzalisiya Lemba limenero pa chifukwa chirichonse, osati Mawu amodzi a Ilo. Muzikhala ndendende ndi Lemba limenero.

<sup>66</sup> Tsopano, Mulungu akuyenera adzawaweruze anthu tsiku lina. Ndipo ngati Iye ati adzawaweruze anthu ndi mpingo, udzakhala mpingo wake uti? Iwo amati, “Mpingo wa Katolika.” Chabwino, ndiye, mpingo wa Katolika wake uti? Mukuona? Chifukwa iyo ndi yosiyana wina kwa umzake, moyipa kuposa momwe iwo aliri ndi ife. Mwaona, iwo ndi osiyana, mmodzi . . . Iwo onse ndi mitundu yosiyanasiyana ya iwo, Achiroma ndi Achiorthodox, ndi Achiyuda ndi, oh, mitundu yambiri yosiyanasiyana ya iwo. Ndipo ndithudi iwo amagwirana pakhosi wina ndi mzake, ndiye ndi wuti wa mipingo ya Katolika imeneyo? Ngati Iye angachite izo ndi mpingo wa Chiprotestanti, mpingo wa Chiprotestanti wake uti? Uliwonse umatsutsana ndi umzake.

<sup>67</sup> Koma Iye adzaweruzza dziko lapansi, ndipo Iye akuyenera kukhala ndi muyezo wina woti adzaweruzire dziko, kapena Iye angakhale wosalungama kutisiya ife kuti tizipita tsopano ndi—ndi kumakhala moyo uno wopanda muyezo woti tiweruzidwe nawo. Ndani angakhale wolondola? Ndi kuti kumene mungadziwe chimene chinali choyenera? Pakuyenera kukhala muyezo.

<sup>68</sup> Ndipo Iye anati, mu Baibulo Lake, kuti Iye adzaweruzza dziko ndi Yesu Khristu. Ndipo timawerenga apa kuti Yesu ndi Mawu. Mu Ahebri 13:8, amati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Chotero, choncho, Iye adzaweruzza mpingo ndi kachitidwe kake kwa Khristu, Amene ali Mawu. “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Osati kuchokera

mkamwa mwa munthu, osati kuchokera ku seminare, osati kuchokera ku—ku mpingo, koma, “kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Munthu akuyenera kukhala moyo ndi Iwo, ndipo Iwo wokha; osati kutanthauzira kwa munthu, koma Mawu Omwewo a Mulungu!

<sup>69</sup> “Chabwino,” inu mukuti, “pali kulakwitsa *Apa*.” Ngati ndi choncho, Mulungu ali ndi choyankhira pa izo. Iye anabweretsa icho kwa ine, mwaona. Ichi ndi chimene ine ndikuyenera kutenga, pomwe pano ndi chimene Iye ananena.

<sup>70</sup> Tsopano, ngati izi ziri ngati zododometsa, ndipo za “munthu pokhala Mkate ndi Mawu,” tiyeni tipite tsopano ndipo tifufuze izi. Tiyeni tifufuze. Chifukwa, Malemba onse ndi owona, ndipo iwo—iwo sangaswedwe konse. Lemba lililonse lidzakwaniritsidwa. Ziribe kanthu momwe izo zikuwoneka zachilendo, Ilo, nthawizonse lidzakwaniritsidwa.

<sup>71</sup> Bwanji ngati—ngati M'bale Williams kapena—kapena ena a abale pano, agogo—a agogo—a agogo athu, onse akanakhoza kuwuka powonekera, mmawa uno, ndipo, nkuti, chabwino, kuwawonetsa iwo televizioni? Ndipo mwinamwake winawake analosera mmbuyo mu tsiku lawo limenero, ndipo anati, “Padzakhala nthawi imene mudzakhoze kumva liwu padziko lapansi.”

<sup>72</sup> Iwo akanati, “Chabwino, musiyeni munthu wachikulire wosaukayo, iye sakuganiza bwino.”

<sup>73</sup> “Ndipo idzakhhalapo nthawi imene mtundu umenewo uzidzayenda mu mlengalenga.” Izo ziri pano pakalipano. “Ndipo azidzayatsa kabatani kakang’onoko, ndipo padziko lonse lapansi mudzizawona anthu akuyenda, ndi zinthu, pa sikrini pomwe.”

<sup>74</sup> “Chabwino,” iwo nkudzati, “munthu wokalamba wosauka!” Mukuona? Koma tsopano ife tiri nazo izo, mchipinda chino mmawa uno.

<sup>75</sup> Ndipo ine ndikufuna kuti ndikudziwitseni inu za izo, ife tisanapite patali, kuti Mulungu ali mchipinda chino. Mlembi wa Mawu awa ali pano. Chotero, ziribe kanthu kuti mwavala chotani, kapena mukukhala bwanji mmoyo, kapena ndi nyumba ya mtundu wANJI imene mukukhalamo, kapena mtundu wa galimoto imene inu mumayendetsa, kapena muli ndi maphunziro ochuluka bwanji, Mulungu amayang’ana pa mtima wanu. Ndipo Iye amayang’ana mu mtima mwanga. Ndipo timaweruzidwa kuchokera mu mtima mwathu, osati ngakhale mawu athu. Mtima wathu umatiweruza. “Kuchokera mumtima kamwa imayankhula.” Ngati izo sichoncho, ndi chinyengo.

<sup>76</sup> Tsopano, mchipinda chino tsopano mukubwera anthu, mawonekedwe a anthu, akudutsa muno, ochokera kuzungulira dziko lonse lapansi, maliwu akuimba, ali mchipinda chino pakali pano. Koma, inu mwaona, inu muli ndi malire, mu

zokhudzira zanu, ku gawo lina la kupenya. Koma tsopano inu mukhoza kutenga zonyezimira, kapena chubu kapena chirichonse chimene chiri mu televizioni, ndi kuchiyatsa icho, ndi china chimene chingathe kupatutsa izo pa za mipweya imeneyo—mafunde a mipweya, ndi kuzipatutsa izo, kuti zikakumane kukalowa mu mpita, ndi kuwanyamula anthu amenewo; wina ku Australia, South Africa, kapena kumeneko, India, kapena kulikonse kumene kungakhale. Inu mukhoza kuyima apa, pa sikrini, ndi kumawona ngakhale mtundu wa zovala zimene iwo avala, mtundu wa mitengo, ndi kusuntha kulikonse kumene iwo akupanga. Mudzangoyatsa televizioni, mudzawone ngati izo siziri chomwecho.

<sup>77</sup> Ndiye, izo zikuyenera kukhala kwinakwake, zobisika ku maso athu, chinthu chomwecho chikudutsa apa tsopano. Izo zinadutsa apa pamene Abrahamu anamva Mulungu akunena kuti, “Yang’ana mmwamba ku nyenyezi.” Izo zinali pano pamene Eliya anakhala pa Phiri la Karimeli. Izo zinali pano pamene Adamu anali kuno, koma iwo angozindikira kumene izo.

<sup>78</sup> Ndipo chomwechonso ali Mulungu pano, ndi Angelo. Ndipo tsikulina zidzakhala zenizeni basi monga momwe televizioni kapena china chirichonse chimakhala, chifukwa Mzimu udzatibweretsa ife ku Moyo wachisavundi umenewo. Ndiye ife tidzamvetsa. Chotero, ndiye, ife tikuyankhula kuchokera mu Mawu Ake. Tsopano, kuti, ife tiyesera . . .

<sup>79</sup> Mulungu, Mulungu Mlengi wamkulu, tiyeni tiyesere kuyankhula pa mawonekedwe a chirengedwe, timutenge Iye mu chirengedwe poyamba, kuti tizibweretsenso izo ku Mawu. Tsopano, chirengedwe chimangoyenda ndi Mawu, chifukwa Mulungu ndi Mlengi wa chirengedwe. Mukawona momwe chirengedwe chimagwirira ntchito, a . . .dziwani kuti ndiyo njirayo. Ichu, ndicho Baibulo langa loyamba, linali loti ndifufuze momwe chirengedwe . . . ndimamupeza Mulungu mu chirengedwe. Ndipo tirigu ndi chopangidwa ndi chirengedwe, mkate, amapanga mkate kuchokera mmenemo, umene umakhutitsa thupi la chirengedwe. Chirengedwe chimasunga zinsinsi zambiri. Ife . . .ndipo iyo ndi nthawi yanga yoyamba kuti ndimupeze Mulungu, inali kuyang’ana chirengedwe. Ine ndinawona kuti pamayenera kukhala chinachake. Ndipo, tsopano, ine ndiribe maphunziro, chotero ine ndimayankhula mochulukana ndi chirengedwe. Ndipo izo ziri . . .Sindikuyesera kuthandizira umbuli. Koma ine ndikuyesera kunena kuti inu simukusowa nkomwe kukhala ndi maphunziro, kuti mumudziwe Mulungu.

<sup>80</sup> Yohane M’batizi, wotsogolera wa Khristu, pamene iye anatuluka mchipululu . . .Ife timaphunzitsidwa kuti anapita mchipululu, pa usinkhu wa zaka naini, ndipo iye anakhala kumeneko chifukwa ntchito yake inali yofunika. Bambo ake anali wansembe. Ndipo mu mzere winawakewo wa unsembe,

kapena chipembedzo, oh, abambo ake anati, “Tsopano, Yohane, iwe ukudziwa iwe ndi woti udzamusonyeze Mesiya. Iwe ukudziwa, M'bale *Wakuti-ndi-pano* akungomupanga mwangwiwo Mesiya!” Chotero Yohane ankayenera kuti achoke kwa izo, iye amapita mchipululu kwa iyemwini, chifukwa zimayenera kukhala kusankha kwa Mulungu, ndipo osati kusankha kwa munthu, nkomwe, amene akanadzakhala Mesiya. Chotero, iye anapita kumeneko pa usinkhu wa pafupifupi zaka naini zakubadwa.

<sup>81</sup> Ndipo, inu mukuzindikira, pamene iye ankatulukako, pa usinkhu wa sarte, maulaliki ake sanali ngati a za waumulungu. Iye sankagwiritsa ntchito mawu ofufuma kwambiri, koma zonse zinali pa chirengedwe. Iye anati kwa amuna a mpingo amenewo a tsiku limenero, iye anati, “Inu kam’badwo ka njoka.” Izo ndi zimene iye ankaziwona mchipululu, njoka. Iye ankadana ndi njoka. Izo zinali chiphe. Mmano ake izo zinali ndi chiphe chakupha, ndipo iye ankanena izi pa mpingo wa tsiku limenero, “Inu mulu wa njoka za chiphe, wakuchenjezani nndani kuti muthawe mkwiyo umene ulinkudza? Musayambe kunena, ‘Ndife a *ichi*,’ ndipo, ‘Ndife—ndife a Jesuites,’ kapena ‘Ndife *akuti-ndi-akuti*,’ kapena, ‘Ife ndi a Methodisti, Baptisti, Presbateria,’ kapena chirichonse chimene icho chiri. Musayambe kunena kuti muli ndi icho, chifukwa, ine ndikukuuzani inu, Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu.” Mukuona?

<sup>82</sup> Komanso, “Nkhwangwa,” ndi imene ankagwiritsa ntchito mchipululu, “iyo idzagona pa muzu wa mtengo. Ndipo mtengo uliwonse umene subereka chipatso chabwino—chipatso, umadulidwa ndi kuponyedwa pamoto.” Mwaona, iye sakanadula mtengo umene umabereka chipatso, chifukwa iye ankakhala moyo ndi chipatso cha mtengowo. Koma, mtengo umene sumabereka chipatso! Oh, inu mukhoza kungotenga Malemba onse, ndi odzozedwa kwambiri, mpaka chirichonse mmenemo chimagwirizana ndi Yesu Khristu. Inu mwaona, “Mtengo uliwonse umene subereka chipatso chabwino umadulidwa ndi kuponyedwa pamoto,” ndi zina zotero. Inu mwaona, iye—iye ankagwiritsa ntchito uthenga wake mu dera la chirengedwe.

<sup>83</sup> Ndipo ife tikufuna kuti tikumane nazo izo tsopano, pokhala kuti ife tapeza kuti Iye anati, “Ine ndine Mkate. Ndipo munthu adzakhala moyo ndi Mawu aliwonse, ndipo Ine ndi Mawu.” Mukuona? Chotero ife tikufuna kubwerera mmbuyo mu chirengedwe. Ine ndimazindikira nthawi zambiri ndimayenera kuchita zimenezo.

<sup>84</sup> Ndipo chirengedwe chimayenda pamlingo wofanana. Mudzatenge nthawi imene mudzawone mbalame zonse zikusonkhana, zikuchoka ndi kupita kumunda ndi kumakadya. Mudzawone ng’ombe zonse zitatuluka, zitamwazikana mmunda, zikudya. Mudzaponyere chingwe chanu, nsomba zidzadyera.



Koma pamene ng'ombe zimenezo . . . Mbalamezo zikawunjikana mmitengo, ndipo ng'ombezo zikawunjikana pa ngodya, inu mukhoza kungochotsa chingwe chanucho. Izo sizidyera, chifukwa chirengedwe chimayenda pamlingo wofanana nthawi zonse.

<sup>85</sup> Ndipo chomwechonso Mawu a Mulungu amayenda mopitirira. Mulungu nthawizonse amachita chirichonse chimene Iye amachita pa mulingo wofanana. Iye anasankha pachiyambi, pamene munthu anataya chiyanjano chake ndi Iye, Iye akanadzamupulumutsa iye ndi magazi okhetsedwa a mmodzi wosalakwa. Ndipo Iye sanasintheo konse njira Yake. Ife tayesetsa kuwaphunzitsa iwo mu izo, kuwapanga iwo chipembedzo mu izo, ndi—ndi kuwapempha kuti alowemo, kuwamenyera iwo mmenemo, kapena kuwafuulira iwo mmenemo. Izo zikukhalabe chimodzimodzi, Magazi okhetsedwa okha ndi pamene Mulungu amakumana ndi wokhulupirira.

<sup>86</sup> Osati, sitingapange Bungwe limodzi la mipingo ya Padziko ndipo aliyense azikumanapo. Izo sizidzagwira ntchito; izo sizinateropo, izo sizidzatero konse. Umo ndi momwe ine ndimatsutsirana ndi kachitidwe kameneko. Mulungu ali nako kachitidwe. Munamva izo zikunenedwa lero, “Mipingo yonse ibwere pamodzi, iyo ikhala Bungwe la mipingo ya Padziko. Ndipo Yesu anapempherera zimenezo, kuti ife ‘tonse tikhale mmodzi.’” Chabwino, tsopano, inu mwaona, amenewo ndi malingaliro achithupithupi, popanda kuwudziwa Mzimu.

<sup>87</sup> Yesu anati, “Kuti iwo akhoze kukhala mmodzi, Atate, monga Inu ndi Ine tiri mmodzi.” Osati kuti munthu wina akhale pamwamba pa chinachake, izo sizidzagwira ntchito nkomwe; chipembedzo chimodzi chikufuna kulanda chimzake, ndipo munthu mmodzi pamwamba pa mzake. Koma kuti inu mudzakhale mmodzi ndi Mulungu, monga Khristu ndi Mulungu anali mmodzi, ndicho chimene pempherolo liri. Kuti, Iye anali Mawu, ndipo Yesu anapemphera kuti ife tithe kukhala Mawu, kumamunyezimiritsa Iye. Ndiro pemphero Lake loti liyankhidwe.

<sup>88</sup> Mukuona momwe Satana amawonongera izo mmalingaliro achithupithupi? Koma limenero silinali pemphero la Yesu, nkomwe, kuti ife tonse tidzisonkhana pamodzi ndipo tonse nkukhala ndi kachikhulupiriro kena ndi zina zotero. Nthawi iliyonse iwo akachita zimenezo, iwo amapita motalikira ndi motalikira kuchoka kwa Mulungu.

<sup>89</sup> Iye amafuna kuti ife tikhale mmodzi ndi Mulungu, ndipo Mulungu ndi Mawu. Munthu aliyense, mu mtima mwake, akuyenera kukhala mmodzi ameneyo ndi Mulungu.

<sup>90</sup> Mulungu podziwa kuti, izi, zinthu zonsezi zinkagwira ntchito monga chonchi. Tsopano umo ndi momwe ife timamupezera Mulungu nthawizina, ndiko kuyang'ana

mu chirengedwe. Nyengo, zimazungulira mozungulira, kumutsimikizira Mulungu. Ndi pamene ndinazipeza izo poyamba, momwe kuti pali moyo umatuluka mu kuphukira, iwo umadzikhala moyo wake, umabereka mbewu, imafa ndipo imapita mu nthaka, imadzabwereranso mu chiwukitsiro, basi kumangozungulira zungulira. Tikhoza kukhala maora pa zimenezo.

<sup>91</sup> Koma tsopano ndi zosiyana bwanji zimenezo ndi monga, m'bale wathu waumishonare kuno, mu India. Ine ndimapeza ambiri kumeneko, ndi kuzungulira dziko, amakhulupirira mu kusintha kwa cholengedwa, kuti, iwo—iwo, kuti iwe umafa kuno ngati munthu ndipo umadzabwereranso ngati mbalame kapena nyama. Mwaona, izo sizimayankhula ndi chirengedwe.

<sup>92</sup> Chirengedwe chimanena kuti mbewu yomweyo imene inalowa mu nthaka, mbewu yomweyo imadzatulukiranso. Mukuona? Yesu yemweyo amene anapita pansu, ndi Yesu yemweyo anadzabwereranso. Aleluya! Ndipo thupi ili, pamene ilo ligwera mu nthaka, ilo silidzabwereranso kudzakhala duwa kapena chinachake, ilo lidzabwereranso kudzakhala mwamuna kapena mkazi. Ife timaziwona izo mu chirengedwe, momwe izo zimakhallira, zimayenera kudutsa mu nyengo yozizira, ndi kukavunda ndi zina zotero, koma moyowo umasungidwa ngati muli moyo uli wonse mmenemo.

<sup>93</sup> Koma ngati, apo, ngati mbewu imeneyo sinamere, iyo sidzawukanso kachiwiri; iyo singawuke, mulibe kanthu mwa iyo koti kawukitse iyo. Ndipo ngati ife titangokhala Mkhristu wamba. . . Pali mipingo iwiri mdziko, mpingo wachithupithupi, mpingo wauzimu, iyo yonse imatchedwa “Akhristu.” Koma mpingo wachirengedwe sungakhoze kuwuka. Iwo ukupanga kuwuka kwake tsopano mu Mgwirizano wa Mdziko, mgwirizano wa mipingo.

<sup>94</sup> Koma Mkhristu amawuka kuti akakumane ndi Khristu chifukwa Iye ndi Mkwatibwi, kupita kukakumana ndi Iye. Pali kusiyana mwa iwo. Chirengedwe chimasunga zinsinsi izi, kwa ife, ndipo tikhoza kuziwona izo pamene ife tikuziyang'ana izo. Ndipo ife tikuwona kuti Chikhristu chimayankhula Choonadi, cha imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiwukitsiro.

<sup>95</sup> Ngati pali mkate wa tirigu umene ife tikudziwa kuti tonse timakhallira nawo moyo, ndipo tikudziwa kuti pali njira imodzi yokha imene tingakhalire moyo, ndi pakudya zinthu zakufa mthupi mwathu. Inu simungakhale moyo mwanjira ina.

<sup>96</sup> Wodya zamasamba anakumana nane, osati kale kwambiri, iye anati, “M'bale Branham, ine ndinali ndi chidaliro chochulukuka mwa inu kufikira nditakumvani inu mukuti inu mumadya nyama yankhumba ndi mazira pa kadzutsa.” Mukuona? Ndipo anati, “Kodi munthu waumulungu angadye bwanji chinthu choterocho?”

Inu mwaona, ine ndinati, “Chabwino, chalakwika ndi chiyani ndi zimenezo?”

<sup>97</sup> Zinthu zonse ndi zodetsedwa, koma zimayeretsedwa ndi Mawu a Mulungu ndi pemphero. Baibulo linati, “Ngati iwe uli mtumiki wabwino wa Yesu Khristu, iwe udzamukumbutsa m’bale za zinthu izi. Mwaona, zinthu zonse zimayeretsedwa, palibe choti chikanidwe, ngati chilandiridwa ndi chiyamiko,” Timoteyo Woyamba :3. Tsopano ife tikupeza kuti zimenezo ndi zoon. Chotero ine ndinati, bola . . .

Ine ndinati, “Chabwino, kodi iwe sumadyaa chinachake chakufa, nawenso?”

“Oh, ayi, bwana!”

<sup>98</sup> Ine ndinati, “Ngati iwe umakhala moyo konse, iwe umayenera kukhala moyo ndi zinthu zakufa. Ngati udyo mkate, tirigu anafa. Ngati udyo masamba, iwo anafa. Chirichonse chimene unachita, ngakhale mkaka, iwe umamwa bakiteriya. Iwe umatero.” Iwe umangokhala moyo kokha ndi zinthu zakufa.

<sup>99</sup> Ndiyeno ngati chinachake chimayenera kuti chife kuti ife tikhale ndi moyo mwathupi, ndi mochuluka bwanji kuti chinachake chimayenera kufa kuti ife tikhale kwa Muyaya! Imfa imachitika, kuti izo zichitike. Mkate! Powona kuti Yesu anati, “Ine ndine Mkate,” ndipo pali mkate wa tirigu ndipo Iye sanali mkate wa mtundu umenewo, chotero pakuyenera kukhala mitundu iwiri ya miyoyo imene imadyetsedwa ndi mkate. Iyo ingatitsogolere ife ku zimenezo. Sizingatheke kuti pakhale . . . Iye siali, Iye sanali tirigu; ndipo Iye sanali Mawu, Iye anali thupi, chotero pakuyenera kukhala mitundu iwiri ya moyo. Ife tikudziwa kuti tirigu amafa kuti ife tikhale moyo mwathupi, monga momwe ndinanenera. Yesu, Mkate wa Mawu, anafa, kuti ife tidzakhale moyo Kwamuyaya. Iye anali Mkate wa Mawu. Tsopano zindikirani, musunge izo mmalingaliro. Tsopano kuti titsimikizire Mawu a Yesu kukhala owona, ife tikuwona mu ichi, mu chirengedwe, momwe izo zimachitikira.

<sup>100</sup> Tsopano tiyeni tipite ku Lemba, kuti tikafufuze kachiwiri, kubwerera ku Lemba mpaka titafika ku mutu wathu waukulu. Mmunda, Mulungu anapereka kwa banja Lake loyamba Mawu a Mulungu kuti azikhalira nawo moyo, Mawu aliwonse a iwo. Banja loyamba limene linaikidwa pano pa dziko lapansi, linapatsidwa Moyo Wamuyaya bola ngati iwo akukhala ndi Mawu a Mulungu.

<sup>101</sup> Limenero linali dongosolo Lake. “Ine ndine Mulungu,” Iye akuti, “Ine sindisintha.” Ilo likadali dongosolo Lake. Ilo silinali konse dongosolo Lake la kachikhulupiro, kapena bungwe, kapena malamulo opangidwa ndi munthu, zimene munthu adzakhale nazo moyo, koma ndi Mawu aliwonse otuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.

<sup>102</sup> Tsopano kubwerera mmbuyo mu Genesis, chimene chiri chiyambi. *Genesis* amatanthauza “chiyambi.” Ife tikupeza kuti Mulungu anapereka kwa banja Lake Moyo Wamuyaya bola ngati iwo akukhala mu Mawu awa ndi kukhala moyo ndi Mawu awa. Koma pamene iwo anaswa icho, cholumikizira chimodzi chokha cha chingwe cha malonjezo, imfa inawakantha iwo, limene linali lonjezo aponso.

<sup>103</sup> Icho ndi chingwe. Inu mukulendewera ku gehena ndi icho, ndipo ndicho chinthu chokhacho chimene chidzakudutsitseni kuti mukafikeko. Pamene wokhulupirira akhala wodzipangitsa kukhulupirira ndi kumakhala moyo pa mawu amodzi amene ali otsutsana ndi Mawu awa, iye amadula chiyanjano chake ndi Mulungu. Cholumikizira chimodzi chaduka! Ndipo, kumbukirani, chikhulupiriro chanu mu Mawu awa chiri ngati chingwe. Chingwe chimakhala champhamvu kwambiri pa malo ake olumikizira ofooka kwambiri. Uko nkulondola. Icho chimakhala champhamvu kwambiri, icho, chifukwa ndizo zonse zimene icho chingagwire. Ndipo ngati pali chinachake mu Mawu chimene chiri chododometsa kwa inu, chinachake chimene inu mwachimva mosiyana, koma iwo anati, “Inu? Oh, izo zinali za atumwi, ndipo zinthu zimenezo zinali za masiku apitawo,” pamene Malemba anati Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, musalole kuti icho chikhale chofooka! Alimbikitseni Iwo ndi kuwagwira Iwo, ndi kukulunga moyo wanu mwa Iwo, chifukwa ndicho chinthu chokhacho chimene chidzakutengereni inu kudutsa malawi a moto. Uko nkulondola.

<sup>104</sup> Pamene chingwe ichi chinaduka, ndi Adamu ndi Eva, banja loyamba, tsopano kumbukirani, iwo sanaphwanye chiganizo, sanaphwanye Mawu atatu; Mawu amodzi! Munthu adzapulumuka gehena ndi Mawu aliwonse, Mawu aliwonse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu. Ndiko kumene kofikira Kwamuyaya kwa munthu kumatsimikiziridwa. Bwanji, iye adzapachikika chifukwa cha chingwe chimenecho, kapena iye adzapachikika chifukwa cha kachikhulupiriro; kapena ngati pali kachikhulupiriro kosakanikira mu unyolowo, apo ndi pamene pali malo ofooka, ndipo inu mwapita. Pamenepo ndi pamene malo ofooka anali ndi Adamu ndi Eva. Malo ofooka aja, “ndithudi,” iye anati, “Mulungu...” Koma ndithudi Mulungu ananena izo! Ndipo ngati Mulungu ananena izo, Mulungu ankanthauza izo. Ndipo Iye nayenso amasunga Mawu Ake ponena kuti, “Tsiku limene mudzadya umenewo, tsiku limenero mudzafa.” Tsiku limene inu mudzaika mwa inu china chirichonse kupatula Mawu osaipitsidwa a Mulungu, mmoyo mwanu, limenero ndi tsiku limene inu mudzalekanitsidwe ndi Mulungu.

<sup>105</sup> Tsopano izi ndi zolimba kwambiri, koma ingomvetserani mwatcheru. Tsopano zindikirani. Mawu amodzi, Mawu amodzi a koyambirira kwa Baibulo, Mulungu ananena kuti, “Mawu

amodzi, anamulekanitsa munthu kuchoka ku Chingwe chake cha Moyo Wamuyaya.”

<sup>106</sup> Izo ziri ngati kumutenga munthu ndi kumupachika iye, ndi mapazi ake... ali ndi manja ake Kumwamba, ndipo inu nkumudula iye pakati pawiri, kuthyola chala chakuphaza, chirichonse chimene inu mukupachikikako. Inu mukulendewera kumusi kwenikweni, ndipo, inu mukadula chingwe chimenecho, paliponse, inu mwapita. Tsopano muzikumbukira zimenezo.

<sup>107</sup> Kumbukirani, Baibulo linati, “Pakamwa pa mboni zitatu, mulole mawu onse akhazikitsidwe.” Ife tifika pa zimenezo, mu maminiti pang’ono, pa mayesero atatu a Yesu; mayesero atatu a atumiki, lero, pamene iwo amagwerapo; mayesero atatu a mpingo, ndi pamene iwo amapangira kugwa kwawo; mayesero atatu a bungwe, pamene ilo limapanga kugwa kwake; ndi mayesero atatu mwa anthu, ndi pamene amapangira kugwa kwawo. Tsopano, zonsezo zimayenda mu zitatu; monga kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera; Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Chirichonse chimakhala changwiwo mu zitatu.

<sup>108</sup> Tsopano zindikirani Mulungu, pachiyambi, chinthu choyamba chomwe Iye anawapatsa ana Ake kuti azikhala nacho moyo, chinali Mawu Ake. Tsopano ife tikupeza kuti izo ndi zoon. Ndiye pakati pa Baibulo, ife tikumva Yesu akubwera ndi kudzanena kuti, “Munthu adzakhala moyo ndi Mawu aliwonse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Ndipo kenako mu Chivumbulutso 22:18, Yesu Iyemwini akuyankhula kachiwiri, anati, “Ine ndikuchitira umboni za zinthu izi. Ngati munthu aliyense adzawonjezera mawu amodzi kwa Awa, kapena kuchotsako Mawu amodzi a Bukhu ili, gawo lake lidzachotsedwa mu Bukhu la Moyo.”

<sup>109</sup> Tsopano, taonani, sikukhala bwino kwathu; icho ndi chinachake chimene chimapita ndi izo. Si kwathu—kukhulupirika kwathu kwa ku tchalitchi; izo zimapita nazo. Koma chinthu chofunikira chake ndi, kukhala ndi Mawu amenewo. Musamadye china chirichonse koma Mawu amenewo. Kumakhala ndi Iwo. Iye ndi Mawu amenewo. Tsopano ife tikufuna kuti tiyang’anitsitse mwacheru tsopano.

<sup>110</sup> Kodi pali kusiyana kotani mu mkate uwu, wa chirengedwe, kukhala ndi moyo? Tsopano, tirigu ndi mkate wa moyo, ngati iyo si mbewu ya haibridi, iyo idza... mukazikwirira izo ndipo izo zidzatuluka kachiwiri. Iku yenera kukhala mbewu yakucha yabwino. Mbewu zowonongeka sizidzawuka. Ife tonse timadziwa zimenezo. M’bale Sothmann, wakhala apa, wolima tirigu wochokera ku Canada, amadziwa kuti simubzala mbewu zowonongeka mu nthaka, kuti muyembekezere mbewu kuchokera mmenemo. Chifukwa, kachilombo kapena—kapena

bakteriya, chimene chiri mu mbewu, chimadya iyo, chimadya moyo wa iyo poyamba.

<sup>111</sup> Kodi inu mumadziwa kuti mphutsi zomwezo zimene zidzakuwonogeni inu, zomwe zidzadye thupi lanu, ziri mmenemo pakali pano? Yobu anati, “Ngakhale nyongolosi ya khungu langa itadzawononga thupi ili!” Kudzakuyikani inu mu bokosi ndi kulisindikiza ilo, mosalowa mpweya; komabe mphutsi, zimene ziri mwa inu, zidzakudyani inu.

<sup>112</sup> Inu mumapeza nsima ndi ufa, ndi zinthu, ndipo mukaziika izo kanthawi pang’ono, izo zimakhala ndi tizirombo mmenemo, mutazitsekera izo. Ndi chiyani chimenecho? Kachiroombo kameneko kali mmenemo, kuyamba ndi kuyamba. Kali mmenemo, kuyamba ndi kuyamba.

<sup>113</sup> Tsopano, mbewu iyi ikuyenera kukhala mbewu yabwino. Iyo ikuyenera kukhala yopanda cholakwika, zolephera, ndi zina zotero, mwa iyo. Ikuyenera kukhala mbewu yosasakanizidwa. Iyo singakhale mbewu ya haibridi—mbewu, chifukwa, iyo ikamera, inu mumaibzalanso iyo, ndipo wanu—tirigu wanu watha, chifukwa mbewu ya haibridi singamelenso. Iyo singamelenso. Inu mumachotsamo moyo mwa iyo pamene muipanga iyo haibridi.

<sup>114</sup> Ndipo ndicho chimene chinachitika kwa mipingo. Iyo yakhala ya haibridi kwa dziko, ndipo ndi chifukwa chake chitsitsimutso chirichonse chikabwera, ndipo inu simungakhale ndi chitsitsimutso china kumbuyo kwake. Bungwe lililonse limene linapangapo bungwe, limafera pomwepo ndipo silimawukanso kachiwiri, chifukwa ilo limapanga bungwe dziko kukhala mu kachitidwe kake, chotero ilo silimateronso nkomwe. Palibepo mbiriyakale imene imawonetsa konse kuti mpingo uliwonse, umene unapangapo bungwe, unawukanso kachiwiri. Iwo umafera pomwepo. Chifukwa chiyani? Inu mumawupanga haibridi iwo.

<sup>115</sup> Musamayike bishopu pa iwo. Muzilola Mzimu Woyera uzikhala pa iwo. Mukuona? Mzimu Woyera unatumizidwa kuti uzichotsa udzu ndi zinthu kunja; osati zimene bishopu akuganiza, kapena oyang’anira, kapena ena otero. Zimatengera Mzimu Woyera kuti usunge mpingo umenewo mu chikhalidwe chake. Iye anali Mawu angwiro amenewo, monga momwe titi tiwonere.

<sup>116</sup> Adamu anali ndi kusankha kwake, Mawu ndi kukhala moyo, kapena kusawakhulupirira Mawu amodzi ndi kufa.

<sup>117</sup> Ife tiri ndi kusankha komweko, chifukwa ife tikuyenera kutero. Ngati Mulungu anamuyika Adamu pa Mawu, ndipo Mawu okha, kenako Iye nkudzatiika ife pa kachikhulupiriro kapena mtundu uliwonse wa kachikhulupiriro, ndiye kuti Mulungu ndi wosalungama mu kuweruza Kwake, sizolondola ku chiyeero Chake kapena kuima payekha Kwake. Koma ndi

zolondola ku kuchita kwa yekha Kwake kuwonetsa kuti Iye akumuyika munthu aliyense pa maziko ofanana. Ndipo Iye ndi Mulungu ndipo samasintha. Chimene Mulungu anachita poyambirira, Iye amachita nthawizonse chinthu chomwecho. Iye samasintha nkomwe Lake—dongosolo Lake. Chinthu chokhacho, Iye amachikulitsa icho, koma Iye samasintha icho nkomwe. Chinthu chomwecho chimapitirirabe.

118 Tsopano, Adamu anali ndi kusankha. Ndipo ngati iye akanagwiritsitsa ku Mawu, iye akanakhala moyo. Ngati iye sanagwiritsitse ku Mawu, iye anafa.

119 Ndipo ife tiri nacho chinthu chomwecho. Ife tikakhala ndi Mawu, ife tikhala moyo. “Munthu adzakhala moyo ndi Mawu aliwonse.” Koma ngati ife sititero, ife tidzafa, ife timafa mwauzimu. Oh, ife tikhoza kumapangabe phokoso, ndithudi, kumakankha pozungulira, ndi kumafuula ndi kumapitirira, koma, izo, izo sindizo—izo sikukhala moyo. Kumeneko sikukhala moyo. Ndine wa misionare. Ine ndawamvapo achikunja akukankha ndi kufuula mochuluka kuposa momwe ife tingachitire, ndi kumadzinenera kuti amadziwa milungu, ndi zinthu monga choncho. Iwo sali moyo. “Iwo ndi akufa akadali moyo.” Baibulo linanena chomwecho. Tsopano ife tikupeza kuti chisankho ichi chinaperekedwa kwa ife.

120 Koma iye analekerera ku mawu amodzi a Satana, kenako iye anafa.

121 Ndipo ngati, chiyambi, chimene Mulungu mu chisomo Chake ndi chifundo akanalambalala zowawa zonse zimene ife tazichita, imfa zonse izi za makanda aang’ono, ndi chirichonse, ndi nkondo, ndi zamkati, ndi kupachikidwa, ndi zinthu zimene ife takhala nazo; ngati Iye akanazilambalala izo, kuchita mwayekha Kwake kwa Mawu Ake kukanamulola Iye kuti alambalale izo, Iye akanakhala wopanda chirungamo ngati Iye akanati azilambalale izo kumeneko. Kodi inu mukumvetsa zimenezo? Iye sangakhoze kuzilambalala izo. Iye sanazilambalale izo kwa Adamu, kuyamba ndi kuyamba. Ndipo Iye sadzazilambalala izo kwa inu kapena ine, kuyamba ndi kuyamba. Ife tikuyenera kubwera ku chinthu chimenecho, Mawu okha. “Mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo anga akhale owona,” Iye anatero.

122 Tsopano tikungoyembekezera tsiku limene tikukhalamo, nthawi yokolola.

123 Kenako Mulungu, Adamu atagwa (atayesedwa ndi Mawu, ndipo anagwa), Mulungu anapitiriza, mu chirengedwe Chake, kuyesera kuti apeze munthu amene akanadzakhala Mawu aliwonse. Tsopano taonani. Iye anayesetsa kuti amupeze munthu, ndiko, kukhala Mawu a m’badwo wake. Tsopano, inu mwaona, Mulungu anamwaza Mawu Ake, chifukwa Iye akanatero.

<sup>124</sup> Iye ali, Iye ndi wopandamalire, ndipo Iye ndi—Iye ndi wopezeka paliponse. Wamphamvuzonse, chotero Iye amadziwa zinthu zonse. Iye sangakhale paliponse. Pakukhala wamphamvuzonse, wodziwa zinthu zonse, ndiye Iye akhoza kupezeka paliponse. Chifukwa, umo ndi momwe Iye amatikonzera ife, mwa kudziwidwiratu, osati chifukwa Iye anafuna kuti munthu *uyu* apulumutsidwe ndipo *uyu* atayike. Koma Iye anadziwa amene akanadzatayika ndi amene akanadzapulumutsidwa. Mukuona? Chotero, mwa kudziwiratu Kwake, Iye akhoza kukonzeratu. Ndipo Iye amapanga chirichonse kugwira ntchito kwa ulemelero Wake. Ndi chimene zikhumbo Zake zikuchita, kuwonetsera ku ulemelero Wake. Chotengera chimodzi chaulemu ndi chimodzi chamanyazi, koma ndi Mulungu amene amapanga izo. “Osati iye amene afuna kapena iye amene athamanga, koma Mulungu amene amawonetsa chifundo.” Mukuona?

<sup>125</sup> “Palibe munthu angadze kwa Ine,” anatero Yesu, “pokhapokhapo Atate Anga atamukoka iye. Ndipo onse amene Atate anali nawo,” nthawi yakale, “anaperekedwa kwa Ine, adzaza kwa Ine, ku Mawu.” Iwo angathe bwanji kubwera pokhapokha ngati iwo anali, onsewo, iwo anazodzedweratu kuti adzabwera? “Onse amene anamulandira Iye, kwa iwo Iye anawapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu.” Mwaona, chifukwa maina awo anali pa Bukhu, Iye anabwera kuti adzawombole chimene chinali pa Bukhu.

<sup>126</sup> Mu Chivumbulutso, ife tikupeza kuti, pamene Zisindikizo zinatsegulidwa, apo panali Bukhu. Ndipo Iye amene anakhala pa Mpandowachifumu, Mulungu, anali nalo Ilo mu dzanja Lake lamanja. Ndipo kunalibe kalikonse, kunalibe aliyense, Kumwamba kapena pa dziko lapansi, kapena kulikonseko, anali woyenera kubwera kudzatenga Bukhulo, kapena ngakhale kuti ayang’ane pa Ilo. Yohane analira kwambiri . . . chifukwa Bukhu lonse la chiwombolo linali pamene.

<sup>127</sup> Panali pa msonkhano usiku wina, m’bale wamng’ono wa Assembly of God uja ndi mlongo anaimba nyimbo ija, “Ine ndikudabwa ngati Yohane anandiwona ine pamene iye anawona mafuko onse atasonkhana. Kodi iye anandiwona ine?” Ndithudi, iye anatero, ngati dzina lanu linali pa Bukhu limenelo. Ndipo pamene . . .

<sup>128</sup> Dzina la Yohane linali pa ilo, nayenso, ndipo iye analira chifukwa panalibe aliyense amene akanakhoza kuligwira Ilo. Ndipo kenako mmodzi wa akuluakulu anabwera ndipo anati, “Usalire ayi, Yohane, pakuti Mkango wa fuko la Yuda walakika.”

<sup>129</sup> Ndipo Yohane anali kuyang’ana pozungulira kuti apeze a—mkango, ndipo kuchokera kuseri kwa katani kunadzabwera Mwanawankhosa, Mwanawankhosa amene anali ataphedwa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Kenako iye



anawona Mwanawankhosa wamagazi akutuluka, ndipo Iye anabwera ndipo anadzatenga Bukhu kuchokera ku dzanja lamanja la Iye, ndipo anaitana chirichonse chimene chinali pa Bukhu limenero. Ilo ndi Bukhu lathunthu la chiwombolo. Ndipo *ili* ndi Ilo. Bukhu la chiwombolo, Iye anawaombola onse amene anali mu Bukhu limenero, osati kunjwa kwa Bukhulo. Chirichonse chimene chinali ndi chiyambi chiri ndi mapeto. Koma ngati inu muli ndi Moyo Wamuyaya, inu simunachite kuyamba ndipo inu simungathe kutha, chifukwa ndinu ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, zikhumbo za maganizo Ake ndi Mawu Ake. Inu mulibe mathero a Moyo, ngati dzina lanu liri pa Bukhu limenero. Mwanawankhosa anabwera kuti adzaliwombole Ilo. Osati onse amene amadzinenera kuti “Akhristu,” osati onse amene amayesetsa kukhala abwino ndi oyera; koma iwo amene maina awo analembedwa mmenemo, Iye anawawombola iwo, ndipo iwo okha, amene maina awo anali pa Bukhulo.

<sup>130</sup> Tsopano ife tikupeza kuti Satana anamupangitsa Adamu kugwa, mwa mawu amodzi amenewo. Ndipo Mulungu anapitirizabe tsopano, mu chirengedwe Chake, kuyesetsa kuti amupeze munthu mmodzi amene akanati adzakhale moyo mwa Mawu aliwonse. Munthu wake woyamba analephera. Ndipo munthu uyu akanadzakhala moyo nthawi yake, m’badwo wake umene iye akukhalamo.

<sup>131</sup> Tsopano, mwaona, ilipo mibadwo yosiyanasiyana imene Mulungu analosera kuchokera pachiyambi, imene ikanadzachitika mpaka mmusi. Ndi chifukwa chake Iye amakhoza kunena mapeto kuchokera kuchiyambi, ndi chifukwa chakuti Iye ankadziwa zinthu zonse. Iye anapanga zinthu zonse mwa Yesu Khristu, ndi kwa Iye, ndi mwa zonkondweretsa Zake Zomwe. Zindikirani mwatcheru tsopano. Musaphonye ichi.

<sup>132</sup> Bwanji ngati Mose akanabwera akubweretsa uthenga wa Nowa? Izo sizikanagwira ntchito. Sizikanatheka. Ayi.

<sup>133</sup> Bwanji ngati Yesu akanabwera akubweretsa uthenga wa Mose? Izo sizikanagwira ntchito.

<sup>134</sup> Bwanji ngati ife titabwera, kumayesetsa kubweretsa uthenga wa Methodisti, uthenga wa Baptisti, kapena uthenga wa Chipentekoste? Izo sizikanagwira ntchito. Iwo anali bwino; nditsimikizira zimenezo mu miniti, mwa Mawu. Iwo anali bwino mu m’badwo wawo. M’badwo umenewo unapita. Ife tikuyenera kupeza chimene chimene limanena za lero. Tsiku lino, ndi chimene munthu akuyenera kukhala nacho moyo kwa m’badwo wake.

Iye anayesetsa kuti apeze munthu amene akanadzakhala Mawu athunthu.

<sup>135</sup> Chinthu choyamba chimene Iye anachita, Iye anamuyesa Nowa. Nowa anamulephera Iye; analedzera, iye analephera.

<sup>136</sup> Mose, mbambande yamphamvu ija ya Mulungu, Iye anamuyesa iye ndipo iye analephera. Iye anadzilemekeza yekha, ndipo sanaloledwe kupita ku dziko lolonjezedwa.

<sup>137</sup> Kenako panadza Davide, kuti Iye akanati adzanyezimiritse Zake—Zake... Zaka chikwi zazikulu, mwa Davide, ndipo Iye anali woti adzawonetsere chimene Mfumu Yake inali. Ndipo Mulungu analumbirira pa Davide, iye adzauka... adzawukitsa Mwana Wake kuti adzakhale pa mpando wake wachifumu. Ndipo Davide anali munthu wolimba mtima, mpaka, “iye anali munthu wapamtima Pomwe pa Mulungu.” Ndipo Davide ankachita bwino. Iye anawakantha Afilisti onse ndi kugwetsera pansi maguwa, ndipo anakhala ndi Mawu. Ndipo, potsiriza, mkazi wokongola anamutembenuza iye, ndipo iye anaswa lamulo, anataya Mawu, anachita chigololo. Mukuona? Munthu wa pa mtima Wake Womwe, mwaona, komabe Davide anamulephera Iye.

<sup>138</sup> Mose anamulephera Iye, ena onsewo anamulephera Iye, koma miyoyo yawo yonse inali chinyezimiritso chabe cha Mmodzi amene anali nkudza.

<sup>139</sup> Mu Bukhu la Chivumbulutso, pamene ine ndikulemba, munthu mmodzi amene akumasulira kapena kukonza... Galamala yanga ndi yoipa kwambiri, ine ndiri ndi—sokolala wabwino woti akonze izo, kuyika manauni olondola ndi mapronauni pamodzi. Chimene, sindikudziwa kusiyana pakati pa nauni ndi pronauuni. Koma, koma iye amatero, ndipo iye akuziyika izo zonse... Ine ndikudziwa, chinthu chokhacho chimene ine ndikuchidziwa, Mulungu amapereka Ichu kwa ine ndipo ine ndimangochilemba Ichu, mwaona. Ndipo, iwo, iwo akuyenera kuziyika izo kuti ngati izo zipita ku masukulu ndi zinthu, iwo—iwo amadziwa kuti akhoza kuwerenga izo mochulukana mmene iwo akuzimvetsera. Ndipo kenako wolembayo anati kwa ine, galamala, munthu amene akukonza galamalayo, anati kwa ine, iye anati, “Koma, M’bale Branham, ife tikupeza mu m’badwo wa mpingo wa Pergamo... Kutu, Yesu ananena apa, ‘iye amene agonjetsa, Ine ndidzampatsa iye Nyenyezi ya Mmawa.’ Kumupatsa iye Nyenyezi ya Mmawa?” Iye anati, “Tsopano iye akanakhoza bwanji kupeza Nyenyezi ya Mmawa, pamene Yesu anati, Iyemwini, kuti Iye ndi Nyenyezi ya Mmawa?”

<sup>140</sup> Mwaona, mbewu zonsezo za Abrahamu zimawonetseredwa ndi nyenyezi. Izo ndizosiyana wina ndi mzake, ndipo ife tidzasiyana wina ndi mzake. Ndipo Yesu ndi Nyenyezi ya Mmawa ija, yowala kwambiri mwa zonse. Koma ife tikumupeza Iye, mu Chivumbulutso 1, ali ndi nyenyezi seveni mdzanja Lake. Iye akutanthauzira izo, ndipo anati, “Nyenyezi seveni izi ndi angelo seveni ku mipingo seveni, kapena mibadwo ya mpingo seveni imene ikudza.”

141 Kenako iye anati, “Zikanakhala bwanji ndiye, ngati iwo anali ndi Nyenyezi ya Mmawa?”

142 Ine ndinati, “Nyenyezi zimene zinali mdzanja Lake zinali kokha nyenyezi zonyezimiritsa kuchokera ku Nyenyezi ya Mmawa, mwaona, pakuti mtumiki wa tsiku limenero anali ndi Mawu.” Ndipo Iye ndi Mawu; iye anangokhala ndi gawo la tsiku limenero. Ndipo anthu amene ali okonzeka kuti achoke ku machitidwe a chidziko ndi zinthu za mdziko, ndi kumayenda ndi Iye, amawona chinyezimiritso cha Nyenyezi ya Mmawa kupyolera mwa mtumiki wa m’badwo umenewo. Monga Iye anachitira kudzera mwa Nowa ndi kudzera mwa Mose, ndi ena otero, pamene Iye ankanyezimiritsa Chipangano Chakale, potsiriza iwo onse anadzafika kwa Mmodzi. Ndipo chomwechonso izo zidzatero pa mapeto a mibadwo ya mpingo, izo zonse zidzabwerera kwa Yesu, kuti Iye ndi Mawu.

143 Ife monga Akhristu tikungonyezimiritsa Iye. Mwezi umangonyezimiritsa dzuwa, pamene ilo palibe. Ndipo wokhulupirira amangonyezimiritsa Mwana wa Mulungu, mmalo mwa Mwana wa Mulungu. Ndi Kuwala kwa Baibulo, Malemba, akutsimikiziridwa mmiyoyo yathu, Mawu amene amapanga Kuwala mu mdima. Ndinu makandulo amene amakhala pamwamba pa phiri. Amenewo si dzuwa; ndi kandulo. Kandulo imangotenga malo a dzuwa, imangowonetsera kuwala kwa mlingo winawake. Ndife ana a Mulungu, ndife ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, mwa Mzimu wokha ndi gawo. Iye anali ndi Iwo wopanda gawo. Ndife nyenyezi imene ikuwala, tonse pamodzi timapanga Kuwala kwa dziko, koma Iye ndi Mwana wathunthu amene amanyezimiritsa Kuwala ku nyenyezi iliyonse. Aleluya! Ine ndikumukhulupirira Iye. Mulungu thandizani kusakhulupirira kwanga!

144 Potsiriza, wangwiwo Uyu anafika. Tsopano, Iye anafika kuti adzayesedwe mu mfundo iliyonse monga momwe ife tiliri. Baibulo linati Iye anali. Iye anayesedwa ngati Nowa. Iye anayesedwa ngati Mose. Iye anayesedwa monga ena onse a iwo. Ngati ife tikanakhala ndi nthawi yoti tiziphwanye zimenezo ndi kukuwonetsani inu, koma ife tiribe, chifukwa ine sindikufuna kuti nditenge nthawi yanu yochulukika. Koma, kuti tiphwanye izo ndi kukuwonetsani inu, Iye anayesedwa mwanjira yomweyo.

145 Satana samasintha njomba zake, ngakhalenso Mulungu, amangosintha mibadwo. Koma chimene... Satana analowa kumbuyo uko, ku banja loyamba la Mulungu, pa dziko lapansi. Ndi izi apa m’bale, mlongo. Musalephere kumvetisa ichi. Kodi Satana analipeza bwanji banja loyambalo? Iye sakanaliphwanyana ilo mwanjira ina iliyonse koma powaswa Mawu amenewo, pakuti iwo anatchingiridwa kuseri kwa Mawu amenewo. Ngati akanangopeza mpata umodzi!

146 Umo ndi momwe wawupezera mpingo uliwonse mu m’badwo

uliwonse, wamupezera wokhulupirira aliyense, amangokokera mpata umenewo kunja. “Chabwino, ine—ine ndimakhulupirira kuti Baibulo ndi lolondola, koma ine sindimakhulupirira izo.” Oh, apo iye akanapita. Zoipa kwambiri, koma apo iye anapita.

“Mawu aliwonse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu!”

<sup>147</sup> Tsopano mwacheru muyike malire izi tsopano. Tsopano Iye potsiriza, Mmodzi uyu amene akanatero, anafika ndipo ankayenera kuti ayasedwe chimodzimodzi basi monga ena onsewo anayesedwa. Tsopano zindikirani momwe mokantha Satana amapangira kumenya kulikonse, mofanana basi nthawi iliyonse. Tsopano iye anayesera kumupatsa Iye mkate wachibadwa, monga momwe iye anachitira kwa Eva. “Ngati mudzadya *ichi*, kutenga *ichi*,” kapena chinachake chimzake, iye ali nacho.

<sup>148</sup> Ndipo ndi chimene iye amachita kwa bungwe lirilonse, ndi chimene iye amachita kwa munthu aliyense, iye amayesetsa kukupatsani inu zinthu zachirengedwe zimene inu mukhoza kuziyang’ana. Ndipo izo zimakutengerani kutali! “Chabwino, tayang’anani pa mpingo wawukulu uwu! Bwanji, iwo ali ndi mamillioni ochuluka kwambiri mmenemo! Mpingo wathu ndi mpingo waukulu kwambiri mu mzindawu. Chabwino, athu, ife tiri ndi ameya amabwera ku mpingo wathu. Onani zonsezo! Abusa athu ali ndi a—digiri ya D.D., L.D., Ph.D! Izo, chabwino, izo, chabwino, iye akuyenera kukhala munthu wanzeru.” Wansembe wa Chikatolika akhoza kubwera ndi kudzamuveka iye, nthawi iliyonse, ndi madigirii ake. Iye ali ndi mabukhu sikisite chakuti ena osamvetseka omwe akuyenera kuwadziwa kwambiri monga inu mukudziwira Baibulo, kuti apeze digiri yake kuti akhale wansembe, chotero musayesere kufanizitsa maphunziro.

<sup>149</sup> Zimenezo ziri ngati dziko, nthawizonse limayesera kufananiza. Musamafananizitse ndi zinthu za mdziko. Musamafananizitse ndi mipingo. Muzifananizitsa ndi Baibulo! Icho ndi chimene ife tikuchita lero. Ndiro limene liri vuto ndi ife mipingo ya Chipentekoste. Ndiro limene liri vuto ndi makorteti athu ndi zoimba, ndi zina zotero, monga ife tiri nazo, ife tikuyesetsa kuti tizichita monga Hollywood. Zonyezimira za Hollywood; Uthenga umawala. Pali kusiyana kwakukulu pakati pa kunyezimira ndi kuwala. Mukuona? Hollywood amanyezimira ndi zovala, ndi ma Ricky ndi ma Ricketta, ndi ma ricochet. Koma Mulungu modzichepetsa amawala mu kudzichepetsa kwa wokhulupirira, ziribe kanthu atakhala mbuli bwanji. Iye amawala modzichepetsa, osati kunyezimira mu Hollywood.

<sup>150</sup> Zindikirani, iye anayesera njomba yake yakale pa Yesu, chinthu chomwecho iye anachita kwa Mose, chinthu chomwecho

iyе anachita kwa ena onsewo. Iye anayesera izo. Iye adzayesera izo pa inu, kuti akupangitseni inu kuvomera chinachake chachikulu chimene chikuwoneka chonyezimira.

<sup>151</sup> Zimandikumbutsa ine pamene ine ndinkakonda kusaka kanyimbi, akanyimbi. Ine ndimakhoza kuwapezera a... Abambo, adadi anga, ankagwiritsa ntchito fodya. Ine sindikudziwa ngati inu nonse munayamba mwadziwapo chimodzi cha zidindo zakale izo zimene zinkakhala pa thumba la fodya. Ine ndinkatenga izo, kutenga chipika ndi kubowola bowo mu icho, kuzungulira mtsinje kumene kanyimbi anali akuthamanga. Ndipo kenako ine ndimabowola bowo mmenemo, ndi kumata chidindo cha fodya ichi pamene. Ndipo kenako nkukhoma misomali ina, yokhota mkati monga *chonchi*. Ndipo kanyimbi nthawizonse amafikira kwa chinachake chonyezimira. Ndipo chotero pamene mwezi utuluka, ndipo iye amathamangira kumeneko, iye ankayang'ana kumbuyo uko, iye anakankhira dzanja lake mmenemo kuti atenge icho. Ndipo iye samamasula icho.

<sup>152</sup> Iye ali ngati mamembala ena a mpingo. Ngakhale iye akudziwa kuti wagwidwa, iye sangamasule icho. “Ngati ine nditero, iwo andichotsa ine mu bungwe.” Imeneyo ndi imfa yake basi, ndizo zonse. Chabwino. Zindikirani. Pamenepo iye wagwiritsitsa pa icho, iye samachimasula icho.

<sup>153</sup> Tsopano Satana anayesa njomba zake zomwezo pa Yesu, zimene iye anaziyesa pa ena onsewo. Iye anayesera kuti amupangitse Iye kudya chinachake pambali pa Mkate wa Mawu wolonjezedwawo. Chifukwa, Yesu anati, “Kwalembedwa, ‘Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha.’” Mukuona? Iye anayesera kumupangitsa Iye kumumvera iye. Ngakhale izo zinkawoneka zabwino kwambiri, zinkawoneka ngati Iye akanakhoza kudzidyetsa Yekha, ndipo Iye akanatha kuchita izo. Inu mwa... .

<sup>154</sup> Inu mukhoza kuchita mwanjira iliyonse imene inu mukufuna kutero, inunso. Inu mukhoza kuwatenga Iwo kapena kuwasiya Iwo, aliyense amene inu mukumufuna kutero. Tsopano ngati kanyimbi ameneyo akanakhala ndi nzeru zokwanira basi kuti, oh, kutsekanso dzanja lake, iye akanakhoza kulitulutsa ilo kachiwiri; koma iye sangachite izo, iye amangodzigwira yekha pamene. Ndipo umo ndi momwe Akhristu ambiri a dzina chabe amachitira, nawonso. Iwo samafuna kuti amve kalikonse za Iwo, samafuna kubwera ndi kudzawamva Iwo. Iwo sakufuna kanthu za Iwo. Pitirirani ndipo mugwiritsitse kwa icho ndiye, mwaona, inu mupeza chimene chimachitika.

<sup>155</sup> Tsopano zindikirani, iwo ankayesera kuti amupangitse Iye kudya chinachake pambali pa Mkate wa Moyo umene munthu aliyense akuyenera kukhala nawo moyo. Koma Yesu anakhala ndi Mawu a Atate. Oh, iye sanamumenye Eva pamene. . .

iyе sanamumenye Mose, iye sanamumenye aliyense wa iwo. Iye anamumenya Mmodzi amene ankati anezimiritse Mawu aliwonse. Mwaona, Iye, ndi chifukwa chake, Iye anali Mawu. Koma Yesu anakhala ndi Mawu, anakana chiphunzitso chake cha zaumulungu zaku seminare, inde, bwana, kuwala kwake kwatsopano, chomuchitikira chake chochuluka. Iye sanathe kukankhira izo pa Yesu monga iye anakankhira izo pa Eva, kuti amuwonetse iye, “Oh, ndithudi, Mulungu . . .”

<sup>156</sup> “Oh, ndithudi, Mulungu angakhale mu izi ngati ife tingakhale pamodzi ndi kupanga Bungwe la mpingo la Dziko lonse. Ndithudi, Mulungu angakhale. Iye amafuna umodzi ndipo amafuna ubale.” Ndi Iyemwini, osati ndi dziko; ubale ndi Iyemwini, kupembedza kwa Iyemwini. Ndicho chimene Iye anafera, kuti inu muzimupembedza Iye. Monga kale, ngati sangathe kupeza . . .

Tsopano ife tikupeza kuti iye analephera. Yesu anabwerera kwa iye, ndi PAKUTI ATERO AMBUYE.

<sup>157</sup> Tsopano pamene iye awona kuti wokhulupirira . . . Penyani wokhulupirira akubwera mu magulu omwewa tsopano, aliyense wa inu. Pamene iye awona (iye) inu mukhala ndi Baibulo, “Eya, ine ndimakhulupirira Baibulo. Ine sindikujowina kachikhulupiriro ndi chinthu kunja uko. Ine ndikhala ndi Baibulo.” Ndipo, monga kale, ngati sangakupangitseni kuti mukhulupirire, ku—kukhala moyo Choonadi chenicheni ndi kukhulupirira Mawu, ine ndikufuna kuti inu muzindikire chimene iye anachita kwa Yesu, nthawi yachiwiri, ngati iye sanakupezeni inu. Nenani, “Ine sindidzajowina kachikhulupiriro. Ine sindidzatero. Ine, ine ndinabadwa mfulu, ine ndidzakhala ndi Iwo. Ine ndichita *ichi, icho, kapena chinacho.*” Mwaona, “kujowina mpingo,” ndipo “mubwere kudzajowina,” ndi chinachake china; iye sangakupangitseni inu kuti muchite zimenezo, ndiye iye adzachita chinachake kwa inu. Oh, m’bale, penyani ichi.

<sup>158</sup> Ngati iye satero, ndiye iye adzakutumizani inu ku seminare yake yomwe, kuti mukaphunzitsidwe ndi afioloje ake omwe, mwaona, kumene Satana ndi wotanthauzira. “Oh, masiku a zozizwitsa anapita. Anthu aja kumusi uko, ine ndiri . . . chabwino, limenero ndi gulu la ampatuko. Iwo, iwo sali, mwaona.” Iye adzakutumizani kumeneko.

<sup>159</sup> Oh, inu mukhoza kunena, “Dikirani miniti, M’bale Branham! Miniti yokha tsopano!” Eya, tiyeni tidikire miniti yokha, mwaona. Inu mukuti tsopano, “Kodi inu simukuyenera kutero? Kodi ife sitikuyenera kutero?” Ayi, bwana. Ayi, bwana.

<sup>160</sup> Koma Yesu anati, “Pamene Iye Mzimu wa Choonadi udzabwera, mwaona, Iye adzabweretsa zinthu izi zimene ine ndakuphunzitsani, ku chikumbutso chanu, Mawu. Ndipo adzakuwonetsaninso zinthu zimene ziri nkudza.” Apo pali

Mpingo weniweni wodzazidwa ndi Mzimu tsopano, umakhala ndi Mawu, umanyezimiritsa Mawu, Mulungu pa dziko lapansi. Mukuona? Iye samasowa wa zaumulungu aliyense, chifukwa Mawu Ake alibe kutanthauzira kwamseri. Iye amatanthauzira Mawu Ake Omwe, powatsimikizira Iwo ndi kuwatsimikizira Iwo, Iwo ndi Choonadi.

<sup>161</sup> Pamene mpingo wa Methodisti unakuuzani inu kuti simungalandire Mzimu Woyera monga iwo anachitira pa Tsiku la Pentekoste, kodi inu munaperekapo tcheru chirichonse kwa icho? Ndithudi ayi. Inu munapitirira limodzi ndipo munalandira Mzimu Woyera, mulimonse. Mukuona? Chifukwa . . .

<sup>162</sup> Ine ndimakambirana za—utatu ndi a—mtumiki wa Baptisti, usiku wina, ndipo ine ndinamuza iye kuti anali maneno chabe. Ndipo chotero ife tinadzapeza kuti, iye anati, mtumiki wina wamng’ono uko wochokera ku seminare, iye anati, “Koma, Bambo Branham, inu mukuyesetsa kuwapangitsa anthu kukhulupirira chipembedzo cha utumwi.”

Ine ndinati, “Ndithudi, chimodzi chokha chimene chiripo.”

Ndipo iye anati, “Bwana, kodi munapita ku sukulu yanji?”

<sup>163</sup> Ine ndinati, “Pa mawondo anga, m’bale wanga. Osati kuti . . . Mwaona, ndi kumene ndimapezako, osati fioloje, koma pamawondo.” Ine ndinati, “Apo ndi pamene ndinamupeza Iye.”

<sup>164</sup> Ndipo iye anati, “Bambo Branham, ubatizo wa Mzimu Woyera, monga iwo anawupezera pa Tsiku la Pentekoste, inu mukuyesera kunena kuti izo ndi lero?”

<sup>165</sup> Ine ndinati, “Baibulo linatero, bwana, kuti . . . kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Ine ndinati, “Ameneyo anali Yesu Khristu amene anabwera pa Tsiku la Pentekoste.” Oh, eya.

<sup>166</sup> Ayi, Mmodzi yemweyo! “Katsala kanthawi pang’ono, Ine ndidzawapempha Atate, Iye adzakutumizirani inu mthonthozi wina, amene ali Mzimu Woyera. Kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine, Ine kenanso; komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka ku chitsiriziro, mathero a dziko.”

<sup>167</sup> Ine ndinati, “Eya, ndi Iye amene anabwera pa Tsiku la Pentekoste. Inde, bwana. Iye anabwera, anadzakhala mwa iwo, zindikirani, mmawonekedwe a umunthu wa Mzimu Woyera, Yesu Khristu mu umunthu wa Mzimu Woyera, monga ife timamvetsera Umulungu.”

<sup>168</sup> Tsopano zindikirani, Satana sankasowa fioloje yake, fioloje. Ndipo mwamuna uyu ananena kwa ine, anati, “Bambo Branham,” iye anati, “Ndikupatsani inu kuti mumvetse, ndine wochokera ku sukulu inayake, ndipo ife tinaphunzitsidwa.”

Ine ndinati, “Ndimamvetsera programu yanu, nthawi zonse.” Mukuona?

Iye anati, “Ife tinaphunzitsidwa kumeneko.” Anati, “Ubatizo wawo wa Mzimu Woyera unali wa ophunzira okha.”

<sup>169</sup> Ine ndinati, “Baibulo linati panali ‘handirede ndi twente’ mchipinda chapamwamba.” Ndipo ine ndinati, “Tsopano ndani akulondola, iwe kapena Mawu?”

<sup>170</sup> Ndipo ine ndinati, “Ndiyeno, aponso, pamene Filipino anapita kumusi ndi kukalalikira kwa Asamaria, ndipo iye anawabatiza iwo mu Dzina la Yesu Khristu, koma Mzimu Woyera unali usanabwere pa iwo apobe, chifukwa Petro anali ndi mafungulo. Chotero iye anapita ku Yerusalemu ndipo anakamutenga Petro, amene anabwera ndipo anayika manja pa iwo, ndipo Mzimu Woyera unadza pa iwo. Baibulo linati, ‘Mzimu Woyera!’”

<sup>171</sup> Ine ndinati, “Kenako Petro, ndi masomphenya, ndi mafungulo, anapita ku nyumba ya Korneliyo, Machitidwe 10, forte-naini. . . ‘Ndipo pamene Iye anali chiyankhulire mawu awa, Mzimu Woyera unagwa pa iwo. Pakuti iwo anawamva iwo akuyankhula mu malirime, ndi—ndi—ndi kunenera, akumukweza Mulungu. Kenako Petro anati, kodi ife tingaletse madzi, kuti awa asabatizidwe, powona kuti iwo analandira Mzimu Woyera monga ife tinachitira pachiyambi? Ndipo anawalamulira iwo kuti abatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu.’

<sup>172</sup> “Ife tikupeza, zaka sarte zitatha, Paulo akudutsa ku madera akumtunda kwa Efeso, anawapeza anthu ena Achibaptisti amene anali ndi chitsitsimutso chachikulu. Zinthu zazikulu zinkachitika. Iwo akufuula, akuyamika Ambuye. Ndipo Paulo anakachezera ku tchalitchi kumene anthu pafupifupi twente anasonkhana, kumene Aquila ndi Priscilla anali pa msonkhano; kumene Apollo, woimira milandu wotembenuzidwa, akutsimikizira mwa Baibulo kuti Yesu anali Khristu. Ndipo iwo anali ndi chisangalalo chachikulu, ndi msonkhano waukulu. Paulo akudutsa, iye anabwera pafupi iye ata. . . Ambuye atamutulutsa iye mu ndende; chifukwa chotulutsa mzimu, mdierekezi mwa wam’bwebwe. Ndipo kenako iye anabwera kudutsa kumeneko, mu ntchito ya Ambuye, ndipo iye anapita kuti akamve msonkhanowo. Ndipo iye anati, ‘Munthu uyu ndi munthu wamkulu, chabwino, koma,’ anati, ‘kodi munalandira Mzimu Woyera kuyambira pamene munakhulupirira?’ Iye ankakhulupirira kuti inu munalandira Iwo pamene inu munakhulupirira. Koma iye anati, ‘Kodi munalandira Mzimu Woyera kuchokera pamene munakhulupirira?’ Iye anati, ‘Ife sitikudziwa ngati kuli Mzimu Woyera uliwonse.’

<sup>173</sup> “Anati, ‘Ndiye munabatizidwa ndi chiyani?’ Limenero linali funso. Iye anati, ‘Ife tinabatizidwa, munthu yemweyo amene anamubatiza Yesu: Yohane. Ife tinabatizidwa mu ubatizo wa Yohane.’ Mukuona? Iye anati, ‘Yohane ankabatiza ku kulapa, osati ku chikhululukiro cha machimo.’ Yohane. . . chifukwa



Mwanawankhosa anali asanaphedwe apobe. Iye anati, ‘Yohane ankabatiza kuloza ku kulapa, powona kuti mukhulupirire pa Iye amene anali nkudza, pa Yesu Khristu.’ ‘Ndipo pamene iwo anamva izi, anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo Paulo anaika manja ake pa iwo, ndipo Mzimu Woyera unadza pa iwo, ndipo iwo ananenera ndi kuyankhula mmalirime,’ zaka sarte mtsogolo.”

Ndipo ine ndinati, “Komanso, kodi mumakhulupirira Baibulo?”

Iye anati, “Ndithudi.”

<sup>174</sup> Ine ndinati, “Petro, pa Tsiku la Pentekoste, pamene izi zonse zinamveka kunjā, ndipo iwo onse anali akufuula ndi kuyamika Mulungu, iwo anati, ‘Amuna ndi abale, tingachite chiyani kuti tipulumuke?’ Petro anati, ‘Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera, pakuti lonjezo liri kwa inu ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo amene ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.’ Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu amenewo sadzalephera konse!”

<sup>175</sup> Inu achipentekoste simunapereke chidwi kwa Amethodisti, Abaptisti, kapena Apresbateria. Inu munkadziwa kuti Iwo unali wa m’badwo uliwonse, ndipo inu munakakamizika kulowa mu Iwo. Ndithudi. Tsopano, musasiye kukanikiza pomwe apo, muzingopitirira kukanikiza, mwaona.

<sup>176</sup> Pamenepo ndi pamene Amethodisti analakwitsira, iwo anakakamizira kulowa mu kuyeretsewa koma anayima. Achilutera anakanikizira ku kulungamitsidwa ndipo anayima. Mwaona, kenako iwo anapanga bungwe iwo, apo iwo unafa. Amenewo ndi mathero ake. Ndizo zonse za iwo.

<sup>177</sup> Penyani tsopano pamene ife tikufulumira kuti timalizitse. “Pamene Mzimu wa Choonadi udza, Iye adzakuphunzitsani inu zinthu zonse, chirichonse chimene ndinakuphunzitsani inu,” oh, mai, “poyika chikumbutso chonse kwa inu, zimene ndanena kwa inu, kubweretsa kwa inu, chikumbutso chonse. Ndipo Iye adzakuwonetsani inu zinthu zimene ziri nkudza. Iye adzatsimikizira Mawu aliwonse, kutsimikizira Mawu ndi zizindikiro zikutsatira.” Chirichonse chimene Iye analonjeza, chimene Mulungu analonjeza mu Baibulo, ngati mudzamasuke ku kachikhulupiriro kalikonse ndi china chirichonse, ndi kugwiritsa ku Mawu, Mulungu ndi wokakamizika kuti asamalire Mawu Ake. Ndipo chotero pamene iwo anachita izi, Mawu amadzitsimikizira Okha.

<sup>178</sup> Iye samasowa wina kuti anene, “Chabwino, masiku a zozizwitsa anapita.”

<sup>179</sup> Ndi ndani munthu ameneyo kuti andiuze ine masiku a zozizwitsa anapita, pamene ine nthawiyina ndinali munthu

wakhungu? Aleluya. Nthawi ina ndinkagona pamene adokotala anandipatsa ine kuti ndikhala moyo maminiti atatu, ndipo ine ndiri moyo lero. Iwo angandiuze bwanji kusiyanana kulikonse? Poyamba membala wofunda wa mpingo, tsopano wodzazidwa ndi Mzimu Woyera. Mulungu samasowa wotanthauzira aliyense. Mzimu Iwowokha, umene uli Mawu, umawatanthauzira Iwo kukhala Choonadi. Ngati munthu angayesere kuimirira ndi kuwatenga Iwo. Iye ndi wodzitanthauzira Yekha. Mudzamuyesere Iye nthawi ina, ndipo mudzapeze ngati izo siziri zolondola. Musadzakhale ndi chidwi kwa chimene wina ananena. Muzichita zimene Mulungu anati muzichita.

<sup>180</sup> “Chabwino,” inu mukuti, “Ndimachita *ichi*.” Chabwino, nanga bwanji enawo, Mawu aliwonse? Mawu amodzi amadula chingwe.

<sup>181</sup> Pamenepo ndi pamene mipingo nthawizonse imalephera, pa chingwe chimenecho. Iwo amawupanga iwo bungwe ndi kuchibweretsa chinthucho pamodzi, ndi kupanga chipembedzo chachikulu. Amuna awa amasonkhana pamodzi, Atate Woyera *Akuti-ndi-akuti* ndi Dokotala Bishopu *Wakuti-ndi-wakuti*. Ndipo chinthu choyamba chimene muli nacho ndi chiyani? Ndi inu apo. Inu mufera pomwepo. Iye titsimikizira izo mwa chiregedwe ndi mwa Mawu, ngati Ambuye alola, mu maminiti pang’ono. Chabwino.

<sup>182</sup> “Kubweretsa ku chikumbutso.” Iye amatsimikizira Mawu aliwonse, ndipo ife timakhala moyo ndi Iwo. Aleluya! Kukhala moyo ndi Iwo! “Munthu adzakhala moyo ndi Mawu aliwonse, Mawu aliwonse otsimikiziridwa.” Yesu anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Zidzawatsatira iwo amene akhulupirira!” Gwiritsitsani Iwo; Mulungu amawatsimikizira Iwo, kuti Iwo ndi Choonadi.

<sup>183</sup> Kumene, maseminare ndi azafioleje, odzozedwa ndi Satana, amati, “Inu simungawadalire Iwo. Izo ndi za atumwi. Masikuwo anapita. Kulibeko chinthu choterocho. Izo zinali za atumwi okha, kuti atsimikizire Uthenga pamenepo. Iye tiri ndi anthu ophunzira lero.”

<sup>184</sup> Iwo anali ndi kuphunzira kwabwinoko nthawi imeneyo kuposa amene tiri nawo lero. Ndiwuzeni ine mpingo uliwonse umene ungate kubwera ndi zimenezo, Sanhedrin imeneyo, pamene agogo-agogo-agogo-agogo-agogo awo ankayenera kukhala ansembe, kumbuyo kwawo. Mawu amodzi okhota pamenepo, mu mpukutu umenewo, kapena, bwanji, iwo—iwo akanawagenda miyala chifukwa cha izo. Iwo ankayenera kukhala ndendende. Koma iwo anaphonya kuwona Njere yeniyeni ya Mawu pamene Iwo anabwera, Moyo. Ndi chifukwa chake iwo anatsutsidwa ndi kutchidwa “antchito a Satana.”

<sup>185</sup> Mwaona, izo sizimanyezimiritsa Mawu a Mulungu, pamene wophunzira waku seminare akuuzani inu, “Mzimu Woyera si wa

lero. Ndipo zinthu izi, zinthu zonsezo za machiritso Auzimuzo, ndi za tsiku lina.” Mwaona, si kunyezimira kochokera kwa Mulungu, ndi kunyezimira kochokera ku a—kachikhulupiriro. Ndi chinyezimiritso cha chiphunzitso chimene chiri kunja kwa Baibulo.

<sup>186</sup> Ahebri 13:8 anati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Yohane Woyera 14:12, anati, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndizichita iyenso adzazichita.” Tsopano inu muwachotsa bwanji Mawu amenewo kuchokera pamenepo, inu muwonjezera bwanji chinachake mmalo Ake? Inu mumadula chingwe cha Moyo. Munthu amakhala moyo ndi Mkate wokha, Mkate, Kwamuyaya iye amakhala moyo ndi Mkate umenewo. Mwathupi, iye amakhala moyo ndi mkate uwu. Pamenepo pali mikate iwiriyo. Mzimu Woyera, Mzimu Woyera uli mwa inu, umati “ameni” kwa Mawu aliwonse a Mulungu, ngati umenewo uli Mzimu Woyera. Tsopano ine ndikufuna ndikufunsemi inu chinachake. Tsopano ili ndi gawo lotsina.

<sup>187</sup> Amayi anakonda kundipatsa ine mafuta a nsasi ndiri mwana. Ndipo ine—ine sindikutha kupirira nalo fungo la zinthuzo, panobe. Mukuona? Ife tinaleredwa osauka, ndipo amayi ankawiritisa zikopa za nyama ndi kumakazipereka izo. Ife tinkakazitenga izo uko ku...kwa mlongo wina wakale wotchedwa Goodwin, amene anali ndi bekare kumusi kumeneko, ndipo iye ankaphika nyama ndi zinthu, ndipo ankaperekera izo. Ife timatenga ufa, ndi kutenga mafuta amenewo ndi zinthu ndi kupanga nsima yathu. Ndipo ife timakhala ndi kudya moipa, nzosadabwitsa ife timakhala onyentchera ndi zina zotero, mliri. Koma amayi ndiye, Loweruka lirilonse usiku... Ife—ife sitinkapeza chakudya choyenera, chotero ankatipangitsa tonse kumwa mlingo waukulu wa mafuta a nsasi. Ndipo ine—ndimangogwira mphuno yanga ndikukuwa, ine ndinati, “Amayi, izi zimandidwalitsa ine kwambiri.” Iye anati, “Ngati izo sizikudwalitsa iwe, izo sizikuchitira iwe ubwino uliwonse.” Chotero, chotero mwinamwake izo zigwira ntchito mwanjira iyi. Tsopano bwanji...

<sup>188</sup> Ine ndikufunsemi inu chinachake. Zingathe bwanji mwamuna kapena mkazi amene amadzinenera kuti ndi wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, umene uli Mawu (nkulondola uko?), ndipo iwe ungakhale bwanji thupi la Mzimu Woyera umenewo, wakupangani inu kukhala gawo la Iye, kuti unyezimiritse Uthenga wa m’badwo wanu, ndi kukana Mawu amene Iye anawalemba?

<sup>189</sup> Ine sindikusamala kuti ndinu wabwino bwanji. Bwanji, ine ndikhoza kukutengerani inu ku Afrika, kwa—kwa Akafula kumeneko, ndi kukuwonetsani inu moyo umene Mkristu sangaukhudze. Ngakhale iwo atagwidwa mu chigololo; ngati mmodzi wa akaziwo, iye asanakwatiwe, mtsikana, amayenera

kuti akapimidwe kaye unamwali wake. Ngati iye apezeka wolakwa, iye amayenera kuti atchule mwamuna amene anachita izo, ndipo awiri onsewo amaphedwa limodzi. Bwanji ngati zimenezo zitachitikira mu United States, ndi ndani angati akakwirire mitembo yonseyo, mukuona? Chotero, chotero ndi zimenezotu, mwaona. Ndipo iwo ndi achikunja, muwone chikhaliidwewo. Mwaona, chotero inu simungayese izo ndi zimenezo. M'bale wathu wa ku India pano akhoza kukuuzani inu tsopano, Achimuhamadi mwinamwake amakhala moyo wabwinoko kuposa momwe ife timaganizira.

<sup>190</sup> Koma icho ndi chiyani? Ndi Mawu amene amapima. Afarisi amenewo anali odzichepetsa kawiri kumuposa Yesu. Iye amapita mozungulira akuphwasula mipingo yawo, ndi kuwaponyera iwo panja, ndi kuwamenyera iwo kunja, ndi chirichonse monga choncho.

<sup>191</sup> Ndipo wansembe wachikulire waumulungu uyu, inu mukudziwa, bwanji, amene anali... Ngati ine ndikanakhala kuti ndiri ndi msonkhano womutsutsa Iye, mmawa uno; ine ndikanati, ndani anabwera kwa inu pamene inu munkadwala, anakupempherani inu? “Wansembe wokalamba waumulungu uja.” Ndani anawabwereka abambo ndalama zimenezo pamene mbewu zake sizinachite bwino? “Wansembe wakale waumulungu uja.” Ndani anakuperekani inu kwa Mulungu, kwa moyo wa utumiki? “Wansembe wokalamba waumulungu uja.” Anali ndani ameneyo, pamene munali mu ndende, anabwera kudzakuwonani inu? “Wansembe wokalamba waumulungu uja.” Ndipo chigawenga chaching'ono ichi chotchedwa Yesu, kodi Iye akuchita chiyani? Anawatcha abusa anu “njoka”! Mukuona? Mwaona, izo siziri mwa zipatso.

<sup>192</sup> Ndi mwa Mawu. “Munthu sadzakhala moyo ndi chipatso chokha, koma ndi Mawu aliwonse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.”

<sup>193</sup> Ndipo Iye anali Mawu amenewo. Iwo angolephera kuti awawone Iwo. Ndicho chimene Iye ankayenera kuti achite. Iwo samakhoza kuchiwona icho, chifukwa iwo sanadzozedwe kuti adzachiwone icho. Anati, “Simungabwere kwa Ine.” Tayang'anani pa Ayuda osauka amenewo, maso awo anachititsidwa khungu. Ndithudi, Iye anachita izo. Iye anawachititsa iwo khungu, Iyemwini.

<sup>194</sup> Taganizani momwe zingakhalire kuchititsidwa khungu. Inu kulibwino muzimuthokoza Mulungu chifukwa cha kupenya kumene muli nako pa Malemba. Tsopano zindikirani.

<sup>195</sup> Tsopano, Iye, Iye anali Mawu awa. Tsopano, zitachitika izi, Iye anayesedwa. Kuyesedwa kwa Yesu. Tsopano ife tikudutsa mu izi.

<sup>196</sup> Mwaona, izo sizimanyezimiritsa Mawu pamene aliyense amati, “Chabwino, Izo zinali za m'badwo wina,” chifukwa

Baibulo linanena kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Momwe Mzimu Woyera mwa inu unganenere kuti ndinu odzazidwa ndi Mzimu Woyera?

<sup>197</sup> Tsopano kodi ndingakupwetekeni inu pang'ono? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Kodi ziri bwino? Kwezani manja anu. Inu simundikwiwira ine? ["Ayi."] Ngati mutero, mukuyenera kutero.

<sup>198</sup> Akazi inu mungathe bwanji, ndi tsitsi lodula, kundiuza ine kuti mwadzazidwa ndi Mzimu Woyera? Mawu amodzi! "Oh, ine ndinayankhula mmalirime." Izo sizimapanga kusiyana kulikonse. Ine ndawonapo asing'anga akuyankhula mmalirime, nkutanthauzira, kufuula mu mzimu, kuvina mu mzimu.

<sup>199</sup> Mwamuna ungadzitche bwanji wekha mutu wa nyumba, ndipo nkumulola mkazi wako azivala zazifupi ndi kumapitirira momwe iye aliri, kudziticha wekha Akhristu?

<sup>200</sup> Azibusu inu mungadzakumane naye bwanji ndi Mulungu ndi chinthu chonga chimenecho, wopanda kuimirira ndi kutsutsa izo? Simungathe kuwapangitsa iwo kuti achite zimenezo. Koma iwe ukafika polalikira monga choncho, iwe sudzakhala mu seminare motalika kwambiri kapena ndi gulu. Mukuyenera kupeza mgwirizano kuchokera kwinakwake. Ife tifika ku zimenezo, mu mphindi chabe, Ambuye akalola. Mukuona?

<sup>201</sup> Koma ndi zimenezotu apo. Musati, ine sindikutanthauza kuti ndikupwetekeni inu. Ndimakukondani inu. Ndicho chifukwa chake. Ngati—ngati mutakhala kuti mukuyandama motsika mtsinje, ndipo ine nkukuwonani inu kuti mukumira, ine ndingakhale munthu woyipa, kumati, "Chabwino, ukhale munthu wabwino, wokonedwa." Inu kulibwino uwachenjeze iwo. Uko nkulondola. Kuwawuza iwo!

<sup>202</sup> Monga ine ndinanena usiku wina, ngati ndine Mkhristu, ine ndiyenera kuti ndizindikiritsidwe ndi khalidwe lililonse la Baibulo. Ine ndinkayenera kuyima ndi Nowa ndi kulalikira ndi iye, mmasikuwo, ndi kuwachenjeza anthu. Uko nkulondola. Ine ndinkayenera kuyima pa Phiri la Karimeli, ndekha, ndi Eliya. Ine ndinkayenera kuyima pa Kalvare, ndi kupachikidwa kwa inemwini ndi maganizo anga omwe, ndi Iye. Komano kenanso, ine ndinawuka ndi Iye pa Isitala, wopambana pa zinthu zonse. Zachithupithupi zonse za umunthu wa mdziko, zinakwezedwa pamwamba pa izo, mwa Iye.

<sup>203</sup> Zindikirani, izo sizimanyezimiritsa Mawu ndiye, ayi, izo sizimawatsimikizira Iwo. Tsopano, koma ngati inu mumakhulupirira Mawu, Mulungu adzawatsimikizira Iwo, Iyemwini, monga Iye anachitira apa mwa Yesu.

<sup>204</sup> Mawu Mkate nthawizonse amatanthauza kudiyetsedwa. "Ndipo munthu sadzakhala moyo ndi mkate, monga mkate uwu, wokha, koma ndi Mawu onse." Chotero umenewo ndiwo Mkate wa Mawu, musunge zimenezo mmalingaliro, uwu

ndi Mkate umene mpingo kudutsa mu m'badwo uliwonse wadyapo, wakhala uli Manna obisika kwa wogonjetsa yekha. Chivumbulutso chinanena chomwecho. Tsopano ndiribe nthawi yoti ndiphwanye chinthu chonsechi, chifukwa mwinamwake ndatsala ndi mphindi sarte zina. Koma, taonani, pamene woyera—pamene manna oyera anagwa kuchokera Kumwamba, amene anali choyimira cha Mzimu Woyera. Inu muvomereza pa zimenezo.

<sup>205</sup> Mulungu anamuza Mose kuti apite akatenge mbiya yodzaza ndi iwo, ndi kukawayika iwo mmalo Oyeretsetsa. Chifukwa, ngati iwo sawayika iwo mmalo Oyeretsetsa, iwo ankavunda. Nkulondola uko? Mphutsi zimalowa mwa iwo. Tsopano Iye anati, “Koma muziwayika iwo mmalo Oyeretsetsa, mu mbiya iyi, kuti m'badwo uliwonse;” ukubwera, utatha unsembe umenewo, pamene munthu akupita kuti akakhale wansembe, kuti akatumikire Mawu, chinthu choyamba chimene iye amayamba kuchita, iye akati wadzozedwa, ndi kukalowa ndi kukatenga manna apachiyambi amenewo odzaza dzanja ndi kuwadya iwo.

<sup>206</sup> Uko kunali kuyimira Kuwala kuja mdzanja Lake, mu m'badwo wa mpingo watsopano, kunyezimiritsa Kuwala Kwake, Manna; ndipo amakhala munthu yekhayo amene wagonjetsa mwangwiwo, munthu amene amakhala pansu kwenikweni ndi kutaya china chirichonse cha pambali pa Mawu. Ndipo Mawu ndi Manna amenewo. Oh, mai, ndi Yesu! “Munthu adzakhala moyo ndi Mawu aliwonse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Amenewo ndi Manna obisika a mgonjetsi, oh, amene ankaikidwa uliwonse—uliwonse, pa unsembe uliwonse motsatira iwo.

<sup>207</sup> Masukulu azaumulungu, kalekale, asinthanitsa Chinthu chodala ichi ndi nyansi za mphodza. Ndiko kulondola ndendende. Inde, bwana.

<sup>208</sup> Monga Esau anachitira. Tsopano, Esau, mwamakhalidwe, anali munthu wabwinoko kuposa Yakobo, koma iye analibe ulemu kwa ukulu wa kuyamba kubadwa kwake umene unali Mawu. Ndi angati akudziwa zimenezo, maufulu oyamba kubadwa anali Mawu, lonjezo, mwana wamkulu? Koma iye anali munthu wabwino, munthu wamakhalidwe, monga, oh, monga Mkristu mwadzina lero, munthu wabwino. Iye sananame. Iye sanabe. Iye anali wabwino kwa abambo ake. Iye anachita zinthu zonsezi. Koma, inu mwaona, ukulu woyamba kubadwa wake, iye ananena kuti iye sankasamala za izo. “Kodi izo zimapanga kusiyana kotani? Ndine M'israeli, mulimonse. Mwaona, ine—ine ndi wa iye, mulimonse.” Koma unali ufulu wake woyamba kubadwa umene unkawerengedwa, mwaona. Cha thupi chake chinali chabwino, koma chauzimu chake chonse chinali cholakwika.

209 Chomwechonso izo ziri lero, mphodza, kusakaniza mpingo ndi dziko pamodzi, zina za chirichonse; maphwando a bingo, zovina, mitundu yonse yomangopitirira, mu mpingo; akazi atsitsi lalifupi, ovala zazifupi.

Chabwino, inu mukuti, “M’bale Branham, chinthu chaching’onocho ndi chiyani?”

210 Amenewo ndi amodzi mwa Mawu, pakuti Baibulo linati ndi kulakwa kuti mkazi azimeta tsitsi lake. Uko nkulondola. Ngati iye atero, iye adzalowamo bwanji mmenemo? Mukuona? Mungofunsa, mlaliki aliyense akuuzani kuti Mawu amanena zimenezo. Mwaona, “iye amanyozetsa mutu wake,” amamunyozeza mwamuna wake. Iye ayenera kusudzulidwa. Ndiko kulondola ndendende. “Pakuti iye amene adzadula tsitsi lake, muloleni iye ametedwe, ametedwe.” Mwaona, izo zikuwonetsera kupyolera mu izo. Osati kungodulidwa, Mulungu sakufuna izo mwanjira imeneyo. Ameneyo ndi Bambo Wapakati uja. Musapusitsike ndi izo. Kulibwino mulidule ilo lonse kapena mulisiye ilo lizikula, icho ndi chimene Mulungu ananena. Mtumiki aliyense wa Uthenga amadziwa kuti izo ndi Choonadi, kaya inu munena izo kapena ayi. Koma ndicho Choonadi. Mukuona? Chabwino, ndi ubwino wanji, ngati inu muti muchite zina zonse, ndi kuzisiya izo?

211 Chiyani? Muli kanthu kakang’ono chabe ka kachitidwe ka chidziko mwa inu, kuyesera kuchita pang’ono pokha monga mipingo ina. Ndizo ndendende pamene Israeli anadzalowera mu vuto. Apo ndi pamene iwo amafera. Apo ndi pamene Adamu anadzalowera mu vuto. Apo ndi pamene ena onsewo anadzalowera mu vuto. Mawu amodzi okha, ndizo zonse zimene zimatengera, mfundo imodzi yokha. Mphodza, zosakanikirana ndi dziko! Ena a mdziko, ena a Hollywood, ena a mpingo, ena azaumulungu, ndipo inu muli ndi chiyani?

212 Zindikirani, ngati Satana alephera apa, ndiye iye adzayesera njira yake yachiwiri kuti akupangitseni inu—musakhulupirire Mawu, iye adza . . . ndi—ndi kupita ku seminare. Iye adzayesa yotsatira, njirayo. Tsopano apa ndi pamene inu mumafunikira kukhala wosamala kwenikweni, ndi kungokhala kwa mphindi faivi zina pa gawo ili, ngati mungathe. Kenako iye amakupatsani inu mwayi wa chاوزimu. Ine ndibwerera ku zonsezi, basi ndisanatseke. Iye amapanga . . . Mwaona, ngati iye sangakuyeseni inu kuti muchoke pa Mawu, “Ayi, ndikhala ndi Mawu,” ndiye iye adzakupatsani inu mwayi wa chاوزimu.

213 Iye anati, “Ine ndikuuza iwe chiyani. Iwe ukwere pamwamba apa ndipo ulumphe kuchoka pa kachisi, ndi kubweretsanso. Mwaona, uwawonetse anthu kuti Iwe ukhoza kuchita chinachake chاوزimu.”

214 Mnyamata, iye anawapezeketsa iwo pamenepo. Tsopano penyani ichi, ichi ndi chimenecho. Mupenye pamene mudzafika

kumapeto, kumene yesero ili linachokerako. Mwinamwake iye akhoza kukulolani ena a inu kuyankhula mmalirime, kumaganiza kuti muli nawo Iwo. Mukuona? Kapena iye akhoza kukulolani inu kunenera, ngakhale izo zisakhale ndi Mawu. Ine ndawawonapo anthu akuimirira ndi kunenera, zinali zosiyana ndi Mawu monga Kummawa kuliri ndi Kumadzulo. Mukuona? Ndi Mawu amene inu mukukhala nawo moyo. Mphatso zauzimu zimenezoz, Satana akhoza kungozipereka izo modzaza manja. Ndithudi. Izo sizitanthauza kanthu kamodzi.

<sup>215</sup> Kodi Yesu sanati, “Ambiri azadza kwa Ine tsiku limenero, ndipo adzati, ‘Ambuye, kodi ine sindinalosere mu Dzina Lanu? Mu Dzina Lanu ndatulutsa ziwanda. Ndinachita ntchito zamphamvu. Ndakhala munthu wamkulu mu bungwe. Ndachitapo zinthu zonsezi, zinthu izi?’” Iye adzati, “Chokani kwa Ine, inu akuchita kusaeruzika.”

<sup>216</sup> Kodi kusaeruzika ndi chiyani? Ndi chinachake chimene iwe umadziwa kuti ndi cholondola, ndipo iwe nkuchivomereza icho ndipo osachichita icho, mu mtima mwako. Pamene iwe ukudziwa kuti Baibulo ilo limaphunzitsa chinthu chinachake, ndipo iwe osachichita icho, ndiko kusaeruzika. Ndipo Davide anati, “Ngati ndibisa kusaeruzika mu mtima mwanga, Mulungu sadzamva konse pemphero langa.” Ndi Choonadi chimenecho? Kodi limenero ndi Baibulo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Tsopano, ndithudi inu simungakwiye ndi Ilo, mwaona. Yesu ananena kuti, “Ambiri adzaza kwa Ine tsiku limenero, ndipo adzati, ‘Ine ndachita zinthu zonsezi,’ ndipo Ine ndidzati, ‘Chokani, inu akuchita kusaeruzika.’”

<sup>217</sup> Chimodzimodzi monga anachitira Adamu. Adamu anati, “Ambuye, ine ndachita *ichi*, ine ndachita *icho*.” Koma Mawu amodzi, mwaona, Mawu amodzi anachita izo. Ndizo zonse zimene zimatengera, kusamvera Mawu amodzi okha.

<sup>218</sup> Inde, mwinamwake kulosera mosiyana ndi Mawu. Koma tsopano, nthawi imene iye ali ndi mphatso yauzimu iyi, iye amatengera kwambiri ndi phokoso, ndi kukongola kwake. “Ulemelero kwa Mulungu, ine ndinapempherera *Wakuti-ndi-wakuti*, iwo anaimirira ndipo anayenda! Aleluya, ine ndikhoza kuyankhula mmalirime! Ndipo winawake nkutanthauzira iwo, ndi zenizeni, zooni.”

<sup>219</sup> Paulo anati, “Ine ndikhoza kuyankhula mmalirime monga anthu ndi Angelo, ndipo komabe nkusakhala kanthu. Ndikhoza kukhala ndi chikhulupiriro chosuntha mapiri, ndipo komabe sindiri kanthu.” Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, “Uko nkulondola.”—Mkonzi].

<sup>220</sup> Koma, mwaona, iye adzakupatsani inu zimenezoz. Oh, anthu Achipentekoste, ine ndimakukondani inu, kapena ine sibwenzi ndikukhala ndi inu. Pamenepo ndi pamene inu munalepherera, mwaona. Muzipenya Mawu, osati mphatso.



Muzipenya woperekayo, muziwona kumene—muziwona kumene iyo ikuchokera, mwaona. Iye yense ndi wotengeka, akuvina mu mzimu, mnyamata... [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]... chinthu chokhacho. Iye ali ndi anthu ochuluka omuzungulira iye, ndipo aliyense akumuyitana iye, kuno ndi uko, ndipo iye akuiwala Mawu.

<sup>221</sup> Oh, ndiwe wotchuka kwambiri pokhapokha ngati iwe ukukhala kutali ndi Mawu amenewo. Koma iwe ukalowa mu Mawu amenewo, nthawi imodzi, uwone yemwe angagwirizane nawe pamenepo. Mukuona? Uwone chimene chingatuluke pamenepo. Tifika ku izi, mu gawo lina la chirengedwe, mkamphindi. Mwaona, mudzawone yemwe—yemwe adzakufuneni inu pamenepo, palibe amene angatero. “Oh, kuchotsa manja pa Iwo!” Monga gulu linalake linasonkhana pamodzi kuno masabata angapo apitawo ndipo anandimanga ine, mtumiki aliyense amene amabwera ku mzindawu, a full Gospel, amakhoza kundibweretsa ine ku mzinda kuno kuti ndidzapempherera odwala awo, amakhala kuti achotsedwa kwathunthu ku chiyanjanocho. Chabwino, chifukwa ine ndimapempherera odwala. Zabwino. “Samawamva Iwo,” akunenedwa. Ndipo ndi amenewo Mawu akutsimikiziridwa.

<sup>222</sup> Ndicho chinthu chomwecho chimene iwo anachita ndi Ambuye wathu. Ndicho chinthu chomwecho chimene iwo amachita ndi munthu aliyense, mu m’badwo uliwonse. Ndicho chimene iwo anachita ndi Luther, Wesley, ndi onse. Ndicho chimene iwo anachita ndi inu, pachiyambi, tsopano inu munabwerera mu matope omwewo amene inu munatulukamo. Zindikirani kachitidweko, nthawizonse zakhala chimodzimodzi. Izo sizinalepherepo konse, Satana amachita chinthu chomwecho.

<sup>223</sup> Tsopano iye watengeka kwambiri ndi phokoso la kukongola, ndi zina zotero, mpaka, mai, iye samapereka nkomwe chidwi ku Mawu. “Oh, m’bale, M’bale *Wakuti-ndi-wakuti* ananena *zakuti-ndi-zakuti*, ndipo ine ndikuyenera kupita cha kuno. Ine...” Mwaona, iye wangotengeka kwambiri, iye samawazindikira Iwo nkomwe. Kaya ndi Mawu kapena si Mawu, sizipanga kusiyana kulikonse. “Ena onsewo anati izo zinali bwino, chotero Iwo samapanga kusiyana kulikonse.” Chipembedzo chimati, “Mnyamata, iwe uli nacho icho, usalole aliyense kuti akuuze iwe!” Iwe uli nacho chiyani? Mukuona? Zindikirani.

<sup>224</sup> Satana anayamba wakhalapo, ngakhale pamenepo, penyani mu malo amodzi awa apa, iye anawakutira Mawu. Ngakhale pa chazimu ichi chimene iye anayesa kuti amupangitse Yesu kuti achite, chazimu, mwaona, pokhala nacho chazimu, nanga bwanji ngati Yesu akanamumvera iye? Mukuona? Iye anati, “Tsopano dikirani. Inu mukufuna kukhala ndi Mawu, sichoncho Inu? Inu mukufuna kukhala ndi Mawu?” Anati, “Kwalembedwa, Iye adzawalamulira Angelo Ake zokhuza

izi. Nthawi iliyonse imene Inu mupondetsa phazi Lanu pamwala, Iwo adzakunyamulirani Inu mmwamba.” Koma Iye samapondetsa phazi Lake pamwala uliwonse. Mukuona? Penyani. Bwanji ngati akanati akhalebe nazo izo? Iye... Kodi inu munazindikira, ine sindinanene kuti iye anabwereza Mawu; iye anawakutira Iwo, anawakutira Iwo, monga kuyika zotsekemera pa keke, anawaphimba Iwo, anawakongoretisa Iwo, mwaona, Iwo sanali mu malo Ake oyenera.

<sup>225</sup> Ndicho chimene iwo amayesera kunena lero, kuyesera kuti awakongoretse Iwo, koma inu simungazipangitse izo kuyenda ndi Malemba onse. Izo zikuyenera kukhala chirichonse, “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Mwaona, ziribe kanthu ndi Mawu ochuluka bwanji amene mungayese kuwakutira, izo sizipanga. . .

<sup>226</sup> Iwo akuyenera kunenedwa momwe Iye anawanenera Iwo. Ndiye, ngati Iwo anenedwa molondola, Iye adzawatsimikizira Iwo kuti zikhale chomwecho mmoyo wanu. “Umo ndi momwe anthu onse amadziwira kuti ndinu makalata olembedwa owerengedwa ndi Mulungu.” *Kalata* yolembedwa ndi ili “Baibulo.” Nkulondola uko? Kalata ndi Baibulo. Ndipo inu ndi Baibulo lolembedwa likunyezimiritsa Mawu Ake, munthu wangwirowa uja kenanso, mwa Mulungu.

Koma Yesu anati, “Kwalembedwa, aponso.” Mukuona?

<sup>227</sup> Koma zindikirani Eva pa mlingo womweyo, anatengeka ndi kumvetsa kwake kwauzimu, iye anali ndi chomuchitikira cha maphunziro azaumulungu. Maphunziro ake anali apamwamba kupa wazaumulungu aliyense mu dzikolo pa nthawi imeneyo. Mwaona, iye anatengeka kwambiri, iye sankazidziwa zimenezo. Iye ankadziwa kuti anali ndi chinachake chimene Adamu analibe. Mwinamwake iye akhoza kumulamulira iye pakali pano, chifukwa iye ankadziwa zochulukuka za izo, Adamu wake. Onani chimene ma Adamu awo akuchita lero. Iye ankadziwa zabwino ndi zoyipa, maphunziro abwino a Choonadi. Uko nkulondola. Iye anali ndi maphunziro abwino a Choonadi, amene iye sankawadziwa kale, ndipo icho chinali Choonadi cha Mulungu. Koma iye anali wakufa, pa kuswa Mawu. Eya, iye anapeza maphunziro ake, bwino bwino.

<sup>228</sup> Chomwechonso seminare inakupatsani inu chokuchitikirani cha maphunziro azaumulungu, mwakuti mukhoza kubwereza khalidwe lirilonse la Chipangano Chakale kapena Chatsopano. Koma muzikhala osamala zimene mukuchita, ngati izo sizikuswa Mawu amenewo pamenepo, ngati mukungoti, “Chabwino, ndi za iwowo.” Ayi, ndi za inu, aliyense amene angafune! Mukuona? Mukuona? Samalani. “Oh, izo zinali za mpingo kalekalelo.” Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse! Iye anali ndi maphunziro abwino, koma iye analinso wakufa mu tchimo ndi nkulakwa.

229 Tsopano kachitidwe kachitatu ka Satana. Ife tifika kwa zimenezozo mwamsanga chifukwa sitikufuna kuti titenge nthawi yochulukirapo kuposa momwe tingathere, mwinamwake maminiti ena fifitini, twente, ngati inu mukufuna kuti mupite motalika chomwecho. Taonani kachitidwe kake kachitatu ndiye, kake, kapena yesero lake lachitatu. Ngati enawo analephera, ili silitero, mwaona. Iye tsopano akukupatsani inu udindo mu mpingo, monga anachitira ndi Yesu. “Ine ndikupatsa Iwe dzikoli. Iwe ukhale mfumu, ine ndidzakupanga Iwe. Iwo onse ndi anga, chotero ine ndikulipereka ilo kwa Iwe.”

230 Ndani angamupange munthu kukhala mtumiki? Ndani angamupatse munthu mphatso mwa kusanjika manja pa iye? “Mulungu anakhazikitsa mu mpingo!” Mukuona? Onani momwe iwo amapotozera Mawu. Monga Eva tsopano, ndi kudziwa kwake kwatsopano, chidziwitso, iye anali ndi Adamu woti amubalalitse. Iye anakhoza kuchita zimene iye ankafuna kuchita, mwaona, mwamsanga pamene iye anamupangitsa Adamu kuti avomereze izo.

231 Ndipo, koma pamene iye anabwera kwa Yesu, Iye sanavomereze izo. Iye anati, “Pita kumbuyo kwanga, Satana.” Mwa kuyankhula kwina, ndiloleni ine ndisabwereze izo molakwika, koma ndingowonjezera ichi kwa izo. “Kwalembedwa, munthu aliyense adzakhala moyo ndi Mawu aliwonse a Mulungu; osati ndi malingaliro anu, ‘Ine ndikupanga iwe kukhala woyang’anira wamkulu, mkulu, kapena—kapena dikoni, kapena ine ndikulola iwe uziyimba limba, mlongo.’ Mwaona, malingaliro onsewa, ‘Ndiwe munthu wotchuka kwambiri, ndipo ife tikufuna luso lako mu mpingo wathu.’” Mwaona, bwerani ku Mawu!

232 Iye akanakhoza kumulamulira iye, kapena kumuphunzitsa iye, chimodzimodzi ngati mbewu ya lero. Umo ndi momwe iwo amachitira izo lero, kuti akhale D.D., wamkulu wa boma, woyang’anira, woyang’anira chigawo, kapena chinachake chonga icho.

233 Ndi zosiyana bwanji ndi Yesu! Iye anakhala ndi Mawu. Tsopano, maminiti pang’ono otsatirawa, ine ndikufuna kutsimikizira zinthu zonsezi zooni, mwaona, mwa ziwiri zonse chirengedwe ndi Mawu, kuzibweretsa izi pamodzi. Izi zikutsimikizira kuti Iye anali Mawu atasandulika thupi, a Mkate. Iye anali Mawu atasandulika thupi. Pakuti Iye ankanyezimiritsa chiyani? Mawu okha.

234 Ngati ndinu kalata yolembedwa, mumangonyezimiritsa Mawu okha; osati zimene seminare ikunena, zimene wina akunena, zimene Abiti Jones akuganiza za Iwo, chimene Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti* akuganiza za Iwo, koma zimene Mulungu ananena za Iwo. “Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo Anga akhale Choonadi! Aliyense

amene adzaphwanya lochepetsetsa la malamulo awa, ndi kuwaphunzitsa anthu chomwecho! Aliyense amene ati adzachotse Mawu amodzi kuchokera mu Bukhu ili, kapena kuwonjezera mawu amodzi kwa Iwo! Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu aliwonse otuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Kukhala moyo Kwamuyaya mwa Mawu amenewo!

<sup>235</sup> Monga momwe mumayenera kukhala ndi zinthu zakufa kumeneko kuti mukhale moyo, inu mukuyenera kukhala ndi Khristu kuti mukhale moyo pano kapena inu mufa. Ndipo Khristu ndi chiyani? “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi anadzakhala pakati pathu.”

<sup>236</sup> Ndipo inu ndi kalata yolembedwa yomweyo, ina ya m’badwo umodzi ndipo ina ya umzake, ya Kuwala kwa ora limenero; koma iwo amalephera kuti ayiwone iyo. Inu mumanyezimiritsa Iko kokha.

<sup>237</sup> Ena okhazikika, ngakhale mmodzi, analephera pa mfundo imodzi; koma Iye sanatero. Ndipo monga ine ndinanena, mu Chivumbulutso 22:18, Iye anati, “Aliyense amene ati adzawonjezere kwa Awa!”

<sup>238</sup> Tsopano penyani mwatcheru kwenikweni tsopano. Mateyu 24:24 ndi zokhudza, momwe iwo. . . “Pafupifupi, mmasiku otsiriza ano,” Yesu anati, “osankhidwa kumene akanadzanyengedwa ndi chinthu ichi.” Penyani mizimu. “Mmasiku otsiriza,” tsopano Lemba limenero likuyenera kukwaniritsidwa. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Tsopano, chimenecho chinali, “Mmasiku otsiriza, osankhidwa omwe, okonzedweratu, osankhidwira kwa iwo, akanadzanyengedwa. . .” Ndizo zangwiro kwambiri, ndi Zamalemba kwambiri, ndipo zikuwoneka zokongola komanso zomveka, mwakuti iwe sungawone chilema mwa izo, mulimonse, osankhidwa okha ndi amene adzathawe izo. Tsopano icho ndi chimene Yesu ananena. Kodi inu mukukhulupirira izo? [“Ameni.”] “Akanatha kunyenga osankhidwa omwe ngati kukanakhala kotheka.”

<sup>239</sup> “Bwanji, ndi Malemba mwanngwi, inu mukhoza kuziwona izo mu diso lachibadwa.” Koma, inu mwaona, izo si zimenezo. Yesu. . . Afarisi amenewo anali ndi Lemba limenero mwanngwiro basi monga Ilo likanakhalira, koma mwa kutanthauzira kwawo komwe.

<sup>240</sup> Kodi iwo anadziwa bwanji kuti Iye samalakwitsa? Chifukwa Mulungu anatsimikizira Mawu aliwonse amene Iye analonjeza kwa Iye mu m’badwo umenewo. Ndi chifukwa chake iwo ankadziwa kuti Iye anali Mesiya. Mukuona?

<sup>241</sup> Tsopano zindikirani, “ngati kukanakhala kotheka,” mmasiku ano. Mawu amodzi okha, Mawu amodzi akufunikira.

Ndizo zonse zimene Satana ankayenera kukhala nazo kwa Adamu, kungomutengera Iye pa Mawu amodzi. Ndizo zonse zimene iye akuyenera kukhala nazo lero, kungotembenuza chinthu chimodzi. Ndizo zonse, ndizo zonse zimene iye amafunikira. Tsopano, inu mukudziwa kuti ndicho Choonadi. Kuwonjezera amodzi, kapena kuchotsapo amodzi, ndi kulephera kwathunthu. Gawo lirilonse, “Mawu aliwonse a Mulungu!” Taganizani tsopano za kutanthauzira kwa maseminare, aliyense wosiyana ndi mzake.

242 Pakuyenera kukhala pali Choonadi penapake, ndipo *ichi* ndi Chimenecho, Baibulo. Tsopano Yesu anati. . .

243 Inu mukuti, “Chabwino, M’bale Branham, iwo ali ndi kupembedza kokongola kwambiri.”

244 Yesu anati, “Pachabe iwo amandipembedza Ine, kuphunzitsa chiphunzitso fioloje ya munthu, osati Mawu,” munthu, kumvetsa kwake komwe kwa Mawu kukutanthauziridwa.

245 Monga ine ndimanenera, Mulungu samasowa wotanthauzira. Iye amatanthauzira Mawu aliwonse Iyemwini. Mwaona, inu simumasowa winawake kuti atanthauzire Iwo kwa inu, Mulungu amatanthauzira izo kwa inu pamene inu muli wololera kuwalandira Iwo. Mwaona, umenewo ndi Moyo, umenewo ndi Moyo Pawokha.

246 Yesu anati, “Pachabe iwo amandipembedza Ine.” Iwo amapembedza Mulungu kwenikweni. Kaini kwenikweni ankapembedza Mulungu, pachiyambi. “Koma pachabe iwo amandipembedza Ine.” *Pachabe* ndi chiyani? “Sizipanga ubwino uliwonse.”

247 Iwo akhoza kunena kuti, “Chabwino, ine ndimachita *ichi*. Ine ndimavina mu mzimu. Ine, ine ndimayankhula mmalirime. Ine, ine ndimanenera. Ine ndimalalikirira Uthenga.” Koma kulephera kulilola tsitsi lanu kuti likule, kulephera pa chinthu chimodzi, ndipo onani chimene chimachitika, Mzimu udzakusiyani inu pomwepo. Ndi chimene chinachitika kwa mipingo yathu, inalephera.

248 “Pachabe, kundipembedza Ine. Oh, ndi kupembedza kokongola. Koma pachabe iwo amandipembedza Ine, kuphunzitsa chiphunzitso malamulo a anthu.”

249 Afarisi amenewo anali a zaumulungu ophunzira. Inu musayerekeze kunena kuti tiri ndi chirichonse lero chofanizira ndi iwo. Ayi, ndithudi. Iwo ankadziwa mawu amodzi, mawu aliwonse, basi momwe iwo analembedwera, koma pachabe iwo ankapembedza. Taganizani za izo, “pachabe,” masukulu abwino kwambiri, ndi maseminare, ndi aphunzitsi, ndi anyamata, ndi chirichonse monga choncho, koma otayika!

250 Chimodzimodzi monga chipululu, Iye anati, “Iwo onse ankadya manna kuchokera ku thanthwe Lauzimu limenelo

mchipululu, iwo onse ankamwa kuchokera ku Thanthwe limenero, ine ndikutanthauza, ndipo iwo onse ankadya manna kuchokera mmenemo.” Ndipo Yesu anati, “Ndipo iwo ali, aliyenseyo, anafa.” *Imfa* imatanthauza “Kulekanitsidwa kwamuyaya.” Chifukwa chiyani? Chifukwa iwo analephera kukhulupirira lonjezo la Mulungu.

<sup>251</sup> Oh, ine sindikonda kukusungani inu monga chonchi, koma ine ndikuyenera kungonena zimenezo. Onani, ine sinditenga miniti pa izi. Aliyense wa anthu amenewo anatulukuka pansa pa Lawi la Moto, iwo anatulukuka mchipululu, akukhulupirira Mulungu, akuguba mtsogolo. Koma pamene iwo anabwera kudawona cholepheretsacho, pamene a—pamene khumiwo anabwerera ndi kudzati, “Ife sitingathe kulitenga dzikolo. Oh, mai, iwo ndi zimphona kumeneko. Iwo ndi *ichi*, *icho*, ndi *chinacho*. Iwo basi. . . Ife sitingachite izo. Ndi zosatheka.”

<sup>252</sup> Koma kodi Kalebu ndi Yoswa anachita chiyani? Iwo anawatontholetsa anthuwo. Iwo anati, “Ife ndi okhoza kwambiri kulitenga ilo.” Chifukwa chiyani? Anthu amenewo ankayang’ana zimene iwo ankaziwona, mwaona, ankayang’ana pa zimene iwo ankaziwona. Koma Kalebu ndi Yoswa ankayang’ana pa lonjezo la Mulungu. Mulungu anati, “Ine ndakupatsani inu dziko limenero. Pitani mukalitenge ilo!”

<sup>253</sup> Tsopano Ahebri wa 6, ngati ine ndingabwereze iyo, “Pakuti sikotheka kwa iwo amene anawunikiridwapo kale, ndipo analawa za Mzimu Woyera, mphamvu ya dziko limene liri nkudza, ngati iwo adzagwa kenanso, kukana, kuchokapo.”

<sup>254</sup> Monga anthu amenewo anabwera uko ndi kudya mphesa zochokera ku dziko lina, anayima pamenepo; ndipo pamene zinafika potsatira Mawu, kupitirira, iwo anati, “Sitingathe kuchita izo.” Ndipo iwo anafera mchipululu.

<sup>255</sup> Ndi pamene ife tiri. Ife tinalawa Mawu abwino a Mulungu. Koma, lonjezo lathunthu, “Ayi, ayi, ife sitingachite izo, mwaona, chifukwa Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti* kapena winawake amati ife sitingachite izo. Izo ndi za atumwi. Limenero linali tsiku lina.” Pamenepo inu mumafa.

<sup>256</sup> Mwaona, Malemba onse amalumikizana pamodzi, Mawu aliwonse a Iwo amalumikizana pamodzi. Ndipo izo sizingaperekedwe ndi lingaliro lirilonse lopangidwa ndi munthu, kachitidwe, kapena chirichonse. Izo zimaumulidwa kokha ndi Mzimu Woyera. Yesu anati, “Atate, Ine ndikukuthokozani Inu kuti Inu munabisa zinthu izi kwa anzeru ndi aluntha, ndipo mwaziululira izo kwa makanda amene angaphunzire.”

<sup>257</sup> Mwamsanga tsopano tiyeni tipite ku ganizo lotsatira ili ngati tingathe. “Pachabe iwo amandipembedza Ine.” Afarisi amenewo, ophunzira, oh, amakhaliidwe abwino; koma kumatchedwa, ndi Yesu, “adierekezi.” Azaumulungu ophunzira amenewo, Yesu anati, “Inu ndi adierekezi, ndipo ntchito za atate

wanu inu mudzazichita.” Anati, “Inu mumakongoletsa manda a aneneri, koma makolo anu mmbuyo mu nthawi yomweyo. . . Aneneri amenewo anabwera kudzaphwasula machitidwe achipembedzo awo.” Icho ndi chimene iwo anachita.

<sup>258</sup> Aneneri! Kodi Mawu amabwera kuti, kwa wazaumulungu kapena mneneri? [Osonkhana akuti, “Mneneri.”—Mkonzi]. Osati kwa azaumulungu ndi sukulu. Iwo amabwera kwa mneneri, nthawizonse. Mulungu samasintha konse kachitidwe Kake, zosatheka. Nthawizonse wakhala, nthawizonse! Osati kwa gulu; kwa munthu payekha! Osati kwa gulu; mmodzi, inde, bwana, mneneri. Ndipo iwo anati. . .

<sup>259</sup> Yesu anati, “Inu mumakongoletsa manda a aneneri, ndipo makolo anu anawaikamo iwo mmenemo.” Ndipo iwo akuchita chinthu chomwecho pansa pa khungu la seminare ya Satana. Mukuona?

<sup>260</sup> Ndipo tsopano, Pentekosite, chotsani mphuno zanu ku Bungwe la mipingo ya Mdziko limenero. Tsopano, inu atumiki pano, inu mumalembera ku likulu, kwa—kwa anthu awa. Tsopano, inu simudzasowa kulembera kwa—kwa a Assemblies ndi ambiri a iwo, chifukwa iwo anachiyika kale chinthucho, iwo sakufuna kanthu kochita ndi icho. Ndipo inu abale Achibaptisti, nanunso, muchotse mutu wanu pamenepo. Kodi inu simukuwona kuti icho ndi ndendende chilemba cha chirompo chimene chikubwera? Inu mukudziwa amene ati azimeze izo zonse, ngati inu mukudziwa chirichonse chokhudza Malemba. Ngati Mawu akudzinyezimiritsa Okha mwa inu, chokaniko kwa chinthu chimenecho. Chipembedzo chanu chidzathamangira ku zimenezo. Ndipo inu mudzasowa kuti muchite zimenezo kapena kuchichotsa chipembedzo chanucho. Inu simungakhale chipembedzo ndi kukhala pamenepo, chifukwa inu mukuyenera kulowa kapena kukhala kunjira.

<sup>261</sup> Ndiye, inu simulinso bungwe, ndiye mwadziwonetsera nokha. Ndendende. Mulungu akudalitseni inu, ngati inu mungachite zimenezo. Ndizovuta kunena kuti ndi angati angachite zimenezo. Koma ena adzatero, sindikukaikira. Inde, bwana.

<sup>262</sup> Ananyengedwa, ndipo Yesu anawatcha iwo “adierekezi.” Tsopano, koma pamene Yesu anali atayima pamenepo, (chiyani) yesero lililonse, Iye analidzudzula ilo ndi Mawu, ndipo anayima pamenepo ndi Mawu. Mulungu anamutsimikizira Iye.

<sup>263</sup> Monga uko, usiku wina, ine ndinalalikira za Michelangelo. Ndi angati anakhalapo ku Forest Lawn ndipo anawona chowumba cha Mose kumeneko, cha Michelangelo? Icho chinali chokhudza, pamene ine ndinapita kumeneko nthawi yoyamba ndi kukachiwona icho. Michelangelo anakhala pafupifupi moyo wake wonse, akuchipanga. Mmalingaliro ake, iye anali ndi chimene—chimene Mose ankayenera kumawonekera. Ndipo

ieye—ieye ankafuna ku—kumukonza iye asanamwalire. Ndipo iye anakhala zaka ndi zaka, akuchisema, kukhapa *apa*, ndi kudzaswa *apa*, ndi kudzapukuta *apa*. Mpaka, potsiriza tsiku lina pamene iye anali atachimaliza icho, patapita zaka zambiri, iye anali atayima pamenepo ali ndi kansalu mdzanja lake, monga *chonchi*. Iye anaimirira mmbuyo ndipo anayang'ana pa icho, masomphenya amene anali mmaganizo mwake, pakuti kuyambira pamene iye anayamba kumva za Mose, izo zikuyenera kuwoneka monga choncho. Apo icho chinali, chinawalira pamaso pake. Iye anadzedwa kwambiri ndi ntchito yake yomwe, iye anatenga hamala ndikuchimenya icho pa mwendo, ndipo anafuula, “Yankhula, Mose!” Iye ankaganiza kuti anali Mose amene amayenera kuyankhula, ndipo iye anali wofanana kwambiri ndi chimene chinali mmaganizo mwake. Ndipo chilema chimenecho pa mwendopo chikadalipobe pamenepo. Ndi chonse chosema changwiro kupatula chibanthu chimene chinachotsedwa pa mwendopo, mwendo wakumanja. Mukachiwone icho mu Forest Lawn, pamene mukupita pakhomo, chojambula cha icho. Mose wa Michelangelo, mbambande yake, imene, imene inasindikiza moyo wake.

<sup>264</sup> Mulungu ndi Wosema wamkulu, kulondola, Iye anamupanga munthu mu chifaniziro Chake, kuti amunyezimiritse Iye, ndipo Iye ndi Mawu. Ndipo kodi Iye anachita chiyani? Iye anamuyesa Adamu; iye analephera, Mose analephera, ena onsewo analephera. Koma apa pali Mmodzi wangwiro, aleluya, (icho chinali chiyani?) palibe choposera Mulungu Mwiniwake mu thupi, Mawu ananyezimiritsidwa mwa Iye, anabweretsa chidzalo cha Umulungu mu thupi; osati mneneri, komabe Iye anali mneneri; osati munthu, komabe Iye anali munthu.

<sup>265</sup> Ayuda, musayese kumunena Iye ngati wanu. Iye sanali Myuda kapena Wamitundu. Iye anali Mulungu. Mukuona? Inu mumakhala chimene magazi anu ali, mwaona, ndipo, ndithudi, ndinu mnofu. Ndipo Maria, ndithudi, Maria analibe pakati ndi Mzimu Woyera ukumupatsa iye kugirigisha. Mulungu Atate analenga nyongolosi, kapena—kapena dzira mwa Maria, ndi khungu la Magazi mwa iye, aponso, ndipo awo ndipo a Magazi a Mulungu.

<sup>266</sup> Magazi amachokera kwa mwamuna. Chotero izo sizinali. . . Magazi amoyo ndi magazi zimayenera kubwera kuchokera kwa abambo, chifukwa khanda silingathe nkomwe kutenga matenda a amayi ake, monga TB. Iye akhoza kutenga izo kuchokera mu mpweya wa mayi, koma osati kuyamwira izo, ine ndikutanthauza, koma akhoza kupuma izo ndi—ndi kuzitengera izo. Koma iye sangathe kuzitenga izo kuchokera kwa amayi, chifukwa iye, iwo alibe izo, iye si magazi a amayi ake.

<sup>267</sup> Tsopano, koma Yesu sanali magazi a Myuda kapena Wamitundu, Iye anali Magazi olenga mwa Yehova



Mwiniwake. Iye anali Magazi a Mulungu. Baibulo linati, “Ife tinapulumsidwa ndi Magazi a Mulungu.” Osati magazi a Myuda kapena magazi a Wamitundu, izo zonse zikanakhala kugonana, koma awa anali Magazi a Mulungu.

<sup>268</sup> Zindikirani tsopano pamene Iye anamuwona Mmodzi wangwiroyo, Iye anamukantha Iye, anamuvulaza Iye. Yesaya anati, “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, anatunduzidwa chifukwa cha kusaeruzika kwathu.” Kodi Iye anali chiyani? Iye anali Mawu angwirowo amenewo, onyezimiritsidwira Mkate, umene munthu aliyense ati adzakhale nawo moyo. Iye anali tirigu ameneyo wa Mawu a Mulungu amene akanakhoza kuperedwa ndi kuikidwa mu Mauthenga anayi, Mabuku sikisite-sikisi. Ndipo munthu adzakhala moyo ndi Iwo, ndipo Iwo okha, ndi Mawu aliwonse a Iwo. Amen. Imeneyo inali mbambande ya Michelangelo. Ndipo pamene Mulungu ankadziwona Yekha akunyezimiritsidwa mwa Munthu, Iye anali ndi Munthu wangwirowo ameneyo atalengedwa mu chifanizo Chake Chomwe. Oh, mai, ndi Munthu wotani! Iye ankayenera kutifera tonsefe. Iye tikhoha kukhala pamenepo, koma sititero. Iye ankayenera kutifera tonsefe. Ndipo Iye anafa, Mmodzi wangwiroyo; kuti ife, opanda ungwirofe, tidzakhale angwirowo mwa Iye, potenga nawo Mawu aliwonse a Baibulo Lake. Tsopano, ndiye Iye anamuukitsa Iye kachiwiri, kwa kulungamitsidwa kwathu, kuti ife tidzakhale ndi ufulu, monga Yesu wowukitsidwayo, kuti Iye ali pano tsopano kuti adzatumikire kwa ife, Mawu aliwonse a Mulungu, amene ife tikuyenera kukhalira nawo moyo.

<sup>269</sup> Tsopano, mwamsanga tsopano, kenako ife tikutseka. Tsopano, mkwatibwi wachiwiri wa Eva.

<sup>270</sup> Tsopano, mkwati woyamba, Adamu; ankayenera kubweretsedwa kupyolera mu mndandanda wautali wa aneneri, ndi zina zotero, ndiye anatuluka wangwirowo, ndipo kenako ankayenera kuti afe kuti akhale Mkate wa ena onsewo.

<sup>271</sup> Tsopano nanga bwanji Eva? Iye akuyenera kuchita chinthu chomwecho. Koma pamene Yesu anabwera... Kumbukirani, Eva anali mkaziyo. Mpingo nthawizonse ndi mkazi woyimiridwa mu Baibulo, chifukwa iye ndi mkwatibwi. Tsopano penyani chimene iye anachita. Iye anayesa kumunyengerera Iye ku chiphunzitsa chake. Bola ngati iye akanamalalikira basi chimene iwo ankaganiza, Iye anali Munthu wamkulu.

<sup>272</sup> Koma tsiku lina iye anayamba kuyankhula, ndipo anati, “Ine ndi Atate ndife mmodzi.”

<sup>273</sup> “Oh, Iwe ukudzipanga Wekha wofanana ndi Mulungu, mwaona. Oh, mai! Iye sitikufuna kukhala ndi kanthu kochita ndi Munthu ameneyo, panonso.”

<sup>274</sup> Ndi zinthu zina zonsezi Iye anayamba kunena, “Pokhapokha inu mutadya Thupi la Mwana wa munthu.” Kodi inu mukuganiza

kuti dokotala akanaganiza chiyani, atakhala pamenepo? Kodi inu mukuganiza kuti munthu aliyense akanatani, kuganiza kwa wamba chabe? “Mukuyenera kudya Thupi Langa ndi kumwa Magazi Anga.”

<sup>275</sup> Iwo anati, “Munthu uyu ndi mthakati, osati mtumiki. Khalani kutali ndi Munthu ameneyo, Iye ndi wopenga. Khalani kutali ndi Iye.”

<sup>276</sup> Koma icho chinali Choonadi. Mwaona, icho chinali Choonadi. “Pokhapokha inu mutalidya Ilo, inu mudzawonongeke. Inu nonse mudzafa, ngati inu simulidya Ilo.”

<sup>277</sup> Ndicho chinthu chomwecho lero. Mkate ndi vinyo ndi chizindikiro chabe, musalole chinthu chachirengedwecho chikugwetseni. Inu mukuyenera kudya Khristu, amene ali Mawu amene inu mumakhala naye moyo, “Mawu aliwonse amene atuluka,” Baibulo lonse kuchokera ku Genesis mpaka Chivumbulutso.

<sup>278</sup> Tsopano, Eva wachiwiri, muwoneni iye. Iye analengedwa mwatsopano, monga Iye anali, pa Tsiku la Pentekoste, wodzazidwa ndi Mzimu, ndi wodyetsedwa Mawu. Amen. Tsopano ine ndikuyamba kukhala wachipembedzo. Ndikumverera bwino. Mpingo woyamba uja, Eva woyamba uja, amene anali woti adzakhale Mkwatibwi wa Khristu. Ndi angati anganene “ameni” kwa zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Iye anali woti adzakhale Mkwatibwi wa Khristu. Iye anabadwira pa Pentekoste, osati ku Nicaea, Roma; osati ku London, England; kapena osati mu United States; osati mu Germany ndi Luther, osati mu England ndi Wesley, osati mu United States ndi Achipentekoste, otchedwa chomwecho. Iye anabadwa pa Tsiku la Pentekoste. Iye anali wodzazidwa ndi Mzimu. Ndipo Iye anali wodzazidwa Mzimu, ndipo wodyetsedwa Mawu, “Mawu aliwonse amene ankatuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.” Ngakhale kwa Yudas. . . Ndipo, oh, iwo ankangoyenera kutenga chirichonse, basi Mawu ndi Mawu, chomera chenicheni chophuka pa dziko la Mulungu, kumuyimira Iye, mtengo wina wa Mkwatibwi.

<sup>279</sup> Mawu Ake a lonjezo anamunyezimiritsa Iye mwa Iye. Iwo ankayenera kumuzindikira Petro ndi iwo. Iwo anali asanapite ku seminare, ndipo iwo ankadziwa zimenezo. Iwo anali asanapite ku sukulu ya Baibulo iliyonse, seminare ina ya zaumulungu. Iwo analibe maphunziro, chifukwa iwo sankatha kulemba dzina lawo lomwe. Baibulo linati, “Iwo anali mbuli ndi osaphunzira.” Koma chinachitika ndi chiyani? Iwo ankayenera kuzindikira kuti iwo amakhala ndi Yesu, pakuti apo Iye anali mwa iwo, akunyezimiritsa lonjezo Lake. Aleluya! Ulemelero kwa Mulungu! Ndi chimene ife tikuchisowa mu m’badwo uno. Mawu

Ake anamunyezimiritsa Iye mwa iye, mpingo. Iye anali wamoyo ndi Mawu aliwonse amene ankatuluka mkamwa mwa Mulungu.

<sup>280</sup> Koma ndiye, monga Eva, iye anakumana ndi kugwa kwake, pa Mawu, ku Nicaea, Roma, kumene bungwe loyamba linayamba lapangidwapo bungwe, mpingo wa Chikhristu wa dziko lonse. Kodi muli wophunzira Baibulo muno? Kodi alipo. . . Kodi alipo wazaumulungu muno amene akudziwa kuti izo ndi zoonza? Bungwe loyamba linali ku Nicaea, Roma. Mulungu analibe konse bungwe, sadzakhala nalo konse limodzi. Ilo limalamulidwa ndi munthu. Uko ndi kumene iwo onse. . .

<sup>281</sup> Ndine Mkhristu. “Kodi ndiwe wa mpingo uti?” Ulipo umodzi wokha. Ine ndakhala ndiri Branham, zaka fifite-faivi, ndipo ine sindinajowine konse m’banjali, ine ndinabadwa choncho. Umo ndi momwe inu mumabadwira mu Ufumu wa Mulungu, ndipo ndinu chinyezimiro cha Mawu Ake.

<sup>282</sup> Zindikirani, Eva anakumana ndi wake. Ndipo chomwechonso Eva wachiwiri anakumana nawo wake ku Nicaea, Roma, anapereka kwa iwo chipembedzo, kachikhulupiriro, navomereza miyambo mmalo mwa Mawu; anachotsa mafano achikunja monga Jupiter ndi ena otero, ndi kuyikapo Paulo ndi Barnaba. Ndipo—ndipo anagwetsera pansi mulungu wa dzuwa ndi mwezi, Ashitoret, mulungu wa mwezi, ndi kokulumunya kozungulira pa iwo, ndipo anamupanga iye kukhala mayi wa mulungu wa dzuwa amene ali Jupiter. Ndipo anasintha tsiku la kubadwa kwa Yesu kuchokera mu Epulo, kumene chirengedwe chonse, kumene Iye anabadwira pansi pa mwana wankhosa wamphongo, chifukwa Iye anali mwana wankhosa wamphongo, ndipo anasintha zimenezo kudzakhala tsiku lobadwa la mulungu wa dzuwa mu dzuwa mmenemo, kumene ilo limapanga tsiku limodzi. . . Pangokhala pafupifupi kusiyana kwa miniti imodzi yokha pa tsiku pamene ilo likudutsa pa tsiku la twente-faivi la Disembara, tsiku lobadwa la mulungu wa dzuwa, osati Mwana wa Mulungu. Ndipo aliyense wa ife amasewera Santa Claus, ndi kukongoletsa mitengo, chikunja, ndi zinthu monga zimenezo, ndipo kenako nkumadzitcha tokha Akhristu? Kodi vuto ndi chiyani ndi mpingo wa Chikhristu?

<sup>283</sup> Kodi padzawuka winawake pakati pathu, amene angalalikire Mawu ndi kunena Choonadi, ndipo Mulungu nkumaziwonetsera izo ndi kumazitsimikizira kwa anthu kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? Ife sitikusowa seminare. Ife sitikusowa wazaumulungu. Ife tikusowa mneneri. Uko nkulondola. Mulungu analonjeza zimenezo, nayenso.

<sup>284</sup> Kenako Eva anakumana ndi kulephera kwake, chomwechonso mpingo; anapereka njira ku chipembedzo, malamulo a munthu, kuti azilamulidwa ndi munthu, osati kulamulidwanso ndi Mzimu. Iye anapita kutali ndi Mawu, ndipo anavomereza miyambo. Ndani anganene “ameni”? [Osonkhana

akuti, “Ameni!”—Mkonzi]. Ndithudi. Koma kodi inu mukudziwa ife Achiprotestanti timavomereza miyambo yambiri imene iwo ali nayo, pamene ife tiwonjezera chinachake ku Mawu awa kapena kuchotsa chinachake kwa Iwo? Satana anamupeza iye, ndi kachitidwe kake komweko kakale kamene anamuchitira Eva, kulekerera. Pamenepo ndi pamene iye anapeza izo, ananena chinachake chosiyana ndi Mawu, kachikhulupiriro kapena chipembedzo.

<sup>285</sup> Choyambirira chinapitirira mu nthaka, mu kufera, zoperera za Roma zinapera tirigu uja kuchokera pa Pentekoste, kudzakhala fumbi, ndi kuwawotcha iwo pa nkhuhi ndi kuwadyetsa iwo kwa mikango. Iwo analowa mmenemo monga tirigu winayo anachitira, ndiko kulondola, koma Iye anayamba kumuwukitsanso iye kachiwiri mu kukonzanso, yemweyo, nthawi yachiwiri.

<sup>286</sup> Monga Iye anachitira ndi Adamu Wachiwiri. Adamu atagwa, Iye anayamba kudzutsa Adamu Wachiwiri. Ndipo Adamu Wachiwiri anagwa, ndiye Iwo anatengedwera mmwamba. Adamu woyamba anagwa mu tchimo lake ndipo anakhala pamenepo. Adamu Wachiwiri anagwa, kuti adzawombole munthu ku tchimo, ndipo anatengedwera mmwamba.

<sup>287</sup> Tsopano, mpingo woyamba unagwa pa Nicaea, Roma, choyamba, mwa Mawu amodzi a Choonadi kuchokera mu Baibulo, pamene mpingo wa Chiroma unali utawonjezera miyambo yawo ndi tizikhulupiriro. Apo panadza wansembe wamng’ono dzina lake Martin Luther, amene anati, “Uwu si mgonero, ili si thupi la Khristu. Ndi kokulumunya. Ndipo, munthu, ‘wolungama adzakhala moyo ndi chikhulupiriro.’” Ndipo anaponyera chinthucho pansu, ndipo anatsutsa izo. Apo pakubwera nyenyezi yanu woyamba ikunyezimira utatha m’badwo wa Tiyatira. Inde, bwana, wolungamitsidwa ndi chikhulupiriro! Iye, Wosema wamkulu, anakhazikika kuti apange Mkwatibwi wa mbambande amene adzanyezimiritse Mawu Ake.

<sup>288</sup> Koma kodi Achilutera anachita chiyani pambuyo pa imfa ya Luther? Iwo anakumana ndi Satana, ndipo anapanga chipembedzo kuchokera mwa izo, ndipo anafa. Iye sanachite china chirichonse zitachitika zimenezo, iye anali atathedwa, anadzangokhala khamu lalikulu la anthu. Chabwino.

<sup>289</sup> Kenako Mulungu anamunyamula iye kachiwiri, mmasiku a John Wesley, ndi Choonadi china choti achinyezimiritse. Kodi iye anachita chiyani? Iye anati, “Kuyeretsedwa ndi ntchito yachiwiri ya chisomo.” Ndipo kodi Mulungu anachita chiyani? Iye anadalitsa icho. Ndipo anawutsutsa mpingo wa Anglican, ndi mpingo wa Zwingli, ndi ena onse a iwo, ndi azamalamulo onse, ndi onse a Kalvini, kapena a—Achikalvini, kani, ndipo anatsutsa izo. Ndipo—ndipo anati, “Olungama adzakhala moyo

ndi chikhulupiro,’ anatero Luther. Ndipo ntchito yachiwiri ya chisomo ndi kuyeretsedwa.” Ndipo ndicho Choonadi. Uko nkulondola. Mukuona?

<sup>290</sup> Ndiye kodi iye anachita chiyani? Chinthu chomwecho, itachitika imfa ya Wesley, ndi Asbury ndi iwo, chinthu chomwecho chimene Luther anachita, kupanga bungwe, kufa. Yang’anani pa izo tsopano.

<sup>291</sup> Ndinapita kumeneko, kuno osati kale kwambiri, kuti ndikamupempherere mkazi mchipatala, akupita ku opreshoni. Ine ndinakalowa kumeneko. Iye anati, “M’bale Branham, ine ndinakuimbirani inu. Inu simukundidziwa ine,” iye anati, “koma kodi inu mungandipempherere ine? Ine ndikuyenera kukhala ndi opreshoni mmawa.”

Ine ndinati, “Ndithudi, mlongo.”

<sup>292</sup> Panali mwamuna wina, mkazi, ndi mnyamata, atakhala pamenepo, pafupifupi mnyamata wa usinkhu wa zaka eyitini, ndipo iwo anali akundi yang’ana ine mwatcheru kwenikweni. Ndipo ine ndinapotoloka ndipo ndinati, “Mungandikhululukire ine, ine nditero . . .”

Iye anati, “Kokani katani imeneyo!”

Ine ndinati, “Kodi inu si Mkhristu?”

Iye anati, “Ndife Amethodisti!”

<sup>293</sup> Ine ndinati, “Icho si chimene ine ndinafunsa. Ine ndinakufunsani inu . . . Ngati ndinu a Methodisti basi, ine ndikoka kataniyo. Ngati ndinu Mkhristu, inu simukusowa kuti katani ikokedwe.” Chotero, eya, uko nkulondola.

<sup>294</sup> Chotero, pali kusiyana kochuluka kukhala wa Methodisti, kapena wa Baptisti, kapena wa Presbateria, ndipo kenako nkukhala Mkhristu; osati pokhala wa Campbellite, koma kukhala Mkhristu, mwaona. Kodi iye anachita chiyani? Chinthu chomwecho.

<sup>295</sup> Ndiye chinachitika ndi chiyani? Mulungu ananyamula gulu laling’ono kumusi kuno Kummwera, munthu wamng’ono wachikuda wokhala ndi diso lopingasa. Ndipo, Iye, kodi iye anachita chiyani? Iye anatsanulira kubwezeretsedwa kwa mphatso, ndipo iyo inakhala Pentekoste. Ndipo ambiri a inu a nthawi zakale monga M’bale Valdez wakhala kumbuyo uko, wanzeru wokalamba, anali kulalikirira pamene ine ndinali wa usinkhu wa zaka faivi. Iye akukumbukira Pentekosite yoyambirira. Mnyamata, usamayankhule bungwe kwa anyamata amenewo, iwo anali atatuluka kuchokera mu chinthu choyipa chimenecho. Ndipo iwo anali ndi Uthenga wa Mulungu.

<sup>296</sup> Koma kodi iwo anachita chiyani? Chinthu chomwecho chimene ena anachita, anachipanga bungwe icho. Tsopano iwo ali ndi pafupifupi mabungwe sarte kapena forte osiyanasiyana, aumodzi, auwiri, autatu. Mpaka, chifundo,

ubwino, ine sindinamvepo zoterozo mmoyo wanga! Kodi inu munachita chiyani? Inu munafera pomwepo. Ndiwo utali womwe mungapiteko. Bungwe lanu silingavomereze Izi. Inu, mwasankha munthu wanu, “Munthu uyu, ngati iye sakhulupirira nafe, musakhale naye mmenemo. Chiyanjano chathu sichingakhale nazo izo.” Oh!

<sup>297</sup> Taonani, ndikufulumira, pakuyenera kubwera Mbewu yoona. Pakungoyenera kukhala, chifukwa Iye akudzera Mkwatibwi wopanda banga kapena khwinya. Iye akudzera zimenezo, Mkwatibwi wotsimikiziridwa ndi Mawu. Oh, iye adzakhala gulu laling’ono kwambiri chomwecho. Yesu anati, “Monga momwe zinaliri mmasiku a Nowa, mmene miyoyo eyiti inapulumutsidwa,” (nkulondola uko?) “chomwechonso zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu.” Ndi angati? Ine sindikudziwa.

<sup>298</sup> Koma, mwaona, Mkwatibwi adzapangidwa ndi onse mmusi kudutsa, amene anali ndi Mawu mu m’badwo wawo. Si gulu lomaliza lokhali basi, Mulungu adzachotsa chinthu chonsecho pano. Oh, ayi.

<sup>299</sup> Ilo lidzakhala—lidzakhala laling’ono kwambiri, zidzakhala zodzidzimutsa. Iwo adzakhala akusowa, inu simudzadziwa nkomwe kuti iwo apita. Bwanji ngati Iye atatenga faivi handirede mmasiku otsiriza ano? Inu simungadziwe izo nkomwe izo. Atatenga faivi handirede mmasiku pang’ono, masiku awiri kapena atatu? Pali anthu ambiri amene amasowa padziko lapansi, samadziwa kumene iwo ali, sitimamva kalikonse za iwo. Kudza kwachinsinsi kwa Ambuye Yesu, Iye adzachotsedwapo.

<sup>300</sup> Ndipo ena onsewo adzakhala akupitirira kumalalikirira, chimodzimodzi monga momwe zinaliri mmasiku a Nowa, “Ulemelero kwa Mulungu, ife tiri nawo Iwo, aleluya,” ndipo anasindikizidwa mpaka ku imfa yawo. Ndicho chimene Baibulo limanena, ndipo Ilo silingalephere.

<sup>301</sup> Monga Nowa, Mose, Davide, ananyezimiritsa kudza kwa Mkwati wangwiro ameneyu; chomwechonso Luther, Wesley, ndi Pentekoste, ananyezimiritsa kudza kwa Mkwatibwi wangwiro.

<sup>302</sup> Zindikirani, nthawi iliyonse imene iye anawonetsera, iye anachita chiyani? Nthawi iliyonse, mpingo uwu, monga Eva anachitira, iye anakakamiza ma Adamu ake kuti akhulupirire kuwala kwake kwatsopano, kachitidwe kake, ndipo pamenepo anafa ndi iko. “Ife tidza, chabwino, gulu lathu lidzakhala pamodzi, mwaona, oh, madalitso athu atsopano a chimene ife tinachepeza, zina zotero.”

<sup>303</sup> Kodi zonsezi zinachita chiyani kwa Eva? Ife tangotsala ndi kanthawi pang’ono tsopano. Kodi zonsezi zinachita chiyani kwa Eva, mwa mpingo woyambirira, mkwatibwi woyambirira kwa Adamu woyamba? Kodi izo zinachita chiyani kwa iye? Tsopano

mvetserani mwatcheru, inu mutsutsana nacho Ichi. Koma izo zinabala “mbewu ya serpenti.” Ndendende.

<sup>304</sup> Mwana wake woyamba sanali mwana wa Adamu. Ngati izo zinali, iye anali ndi maufulu akubadwa nawo. Baibulo, mu Yuda, linanena kuti Adamu . . .kuti, “Enoki anali wachiseveni kuchokera kwa Adamu.” Nkulondola uko? Ndipo iye akuyamba, “Adamu anabala mwana wake, Seti.” Nanga bwanji Kaini, amene anali ndi ukulu wakubadwa? Iye sanali mwana wa Adamu. Seti, ndipo Seti anabala; Yaredi, ndi kumapitirira mmusi kwa Adamu, chimene mmusi mpaka . . . “amene anali wachiseveni kuchokera kwa Adamu.” Ndiye ngati Kaini anali mwana wake, mulibemo malo amodzi mu Baibulo, ngakhale mu Luka pamene iye akulozeranso kwa iwo kachiwiri, iye sakunena konse za Kaini kukhala mwana wa Adamu. Ndipo, ngati iye sanali, iye anali mwana wa ndani? Ndipo ngati iye anali mwana wa Adamu, iye anali mwana wake woyamba, amene anali ndi ukulu wakubadwa wonse. Oh!

<sup>305</sup> Ndi umenewo mpingo wachithupithupi uja (kodi inu simukuwuwona iwo?) umene unavomereza chinachake, chinali chigololo mmalo mwa Mawu. Anthu Achipentekoste, akudalitseni inu. Chabwino, kodi iye anabala chiyani kwa Eva? Mbewu ya serpenti. Kodi izo zachita chiyani mmasiku otsiriza ano, mwa chipembedzo? Zabala mbewu ya serpenti, kachiwiri, kukana Mawu. Kodi iye anapereka chiyani? Zipatso ndi zinthu, osati Magazi.

<sup>306</sup> Mwa vumbulutso la Mawu, Mawu a Mulungu Iwo asanalembedwe nkomwe, “Abele mwa chikhulupiriro anapereka kwa Mulungu nsembe yopambana yoposa ya Kaini, amene anachitira umboni kuti anali wolungama,” Mawu akudzinyezimiritisa Okha kudzera mwa iye, mwa chopereka chake.

<sup>307</sup> Oh, Kaini anapita ndipo anakatenga zipatso za mmunda, iye ankaganiza kuti Eva anadya apulo. Maseminare ambiri a zaumulungu azisintha zimenezo tsopano kukhala aprikoti. Icho chinali chigololo. Ndipo aliyense akudziwa zimenezo, amene amalidziwa Baibulo. Ndithudi, icho chinali.

<sup>308</sup> Zindikirani, mbewu ya serpenti inapangidwa ndi kuchoka koyamba kwa Eva woyamba ku Mawu. Eva wachiwiri anachita chinthu chomwecho ku Nicaea, Roma. Ndipo iye ali ndi chiyani? Gulu la ana achipembedzo. Uko nkulondola. Oh, amakhaliwe abwino; ndithudi, abwino. Koma nanga bwanji zimenezo? Akufa, kupyolera mu tizikhulupiriro tawo.

<sup>309</sup> Momwemonso tsopano. Vumbulutso la Kaini la Mawu linachita chinthu chomwecho chimene awa achita. Chiyani? Anamulonjeza iye. Pamapeto a nthawi, ndi chiyani chikumulonjeza Eva uyu tsopano? Mvetserani mwatcheru tsopano, ndikutseka. Ndi chiyani chikumulonjeza Eva uyu

pa nthawi yotsiriza? Chuma, Laodikaya, dzina lalikulu, munthu wamkulu, wolemera. “Koma akufa, ndi amaliseche, ndipo osadziwa izo.” Ndicho chimene m’badwo wa mpingo unatheramo.

<sup>310</sup> Koma iye amawakana Mawu. Kuti apange Mateyu 24:24 kukhala weniweni kwa iye, iye amayesera kulowamo ndi phokoso lambiri, ndi zochuluka za *ichi*, ndi mayimidwe ochuluka a gulu, ndi zinthu monga izi, kuyesetsa kuti aziti, “Chabwino, ife tiri ndi mphamvu! Ulemelero kwa Mulungu, alaluya, ife tiri ndi mphamvu!” Kukhala nawo mawonekedwe aumlungu, koma kumakana Mphamvu yake, zapafupi kwambiri mwakuti akanadzanyenga osankhidwa omwe... Munthu angavine bwanji mu Mzimu ndi kuyankhula mmalirime, ndipo nkukana Mawu a Mulungu kukhala Choonadi, ndi kukhala Mzimu Woyera? Izo sizingachitike basi.

<sup>311</sup> “Mawu aliwonse!” Mulungu amanena chinthu chimodzi, ndicho ndendende basi chimene Iye akutanthauza. Musawatanthauzire Iwo mwanjira ina. Baibulo limanena, kuti, “Iwo alibe kutanthauzira kwamseri.” Muzinena izo momwe Iye anawanenera Iwo.

<sup>312</sup> Zindikirani, mphamvu yabodza. Ndizo ndendende zimene Satana ankafuna kupereka kwa Yesu, kukwera pamenepo ndi kukamupangitsa Iye adziwonetsere Yekha. Anthu amachita zimenezo, ngakhale a World Council, onse a iwo. “Ndani angathe kuchita nkondo ndi iye,” iye anati, Baibulo, “chifanizo ichi cha chirombo chimene chiti chidzawuke?” Ngati ife tikanakhala ndi nthawi, tikanalowa mmenemo (koma ife tiribe) mu izo. Zindikirani Yesu, Adamu wachiwiri wa Mawu, mu tsiku lake, penyani mmasiku a mpingo uwu tsopano umene uti udzakhale wapafupi kwambiri. M’badwo wa mpingo wotsiriza ndi Laodikaya. Ndi angati anganene “ameni” kwa izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Kodi iye akuchita chiyani? Kodi iye akulowa chotani mu gawo laulemelero? Wofunda, wopanda Mulungu. Ndipo iye anachita chiyani?

<sup>313</sup> Tsopano, Adamu anamuwona Eva mwadala... kapena osati mwadala, koma ananyengedwa mosadziwa, ndipo Adamu anatulukana ndi Eva kuti akamuwombole iye. Nkulondola uko? Baibulo linati, “Adamu sananyengedwe.” Ndicho chifukwa Ilo limawaletsa akazi kulalikira Uthenga. Mukuona? Adamu sanali mu kulakwa, komabe Eva anali. Chotero ndi chifukwa chake iye sakuyenera kuphunzitsa, mwaona, kapena kulanda ulamuliro uliwonse pa mwamuna, kapena zina zotero. Ndicho—ndicho chimene Mawu amanena.

<sup>314</sup> Inu mukuti, “Chabwino, ichi...!” Ine sindikusamala chimene *ichi* chimachita ndi *icho* chimachita. Ndi chimene Mawu amanena, m’bale, mlongo. Ine ndikuyesetsa kuti ndizifikitse izo kwa inu, mwaona, ndi chimene Mawu amanena.



Ife timakhala moyo mwa Mawu, osati umboni wina, kapena chinachake chachithupithupi, kapena chokuchitikira china. Izo ziribe kanthu kochita nazo izo. Chochitika chamtundu uliwonse sichingagwire ntchito, ngati icho chiwakana Mawu. “Ambiri adzadza kwa Ine ndipo adzati, ‘Ine ndinanenera, ndinatulutsa ziwanda. Ine ndinayankhula mmalirime. Ine ndinachita zinthu zonsezi, ndinalalikira Uthenga, ndi Dokotala wa Zaumulungu.’ Anati, ‘Inu akuchita kusaeruzika, Ine sindinakudziweni inu nkomwe.’” Kumadziwa kuti Mawu amanena Zimenezo, ndipo kenako nkunyengerera chifukwa cha bungwe lina kapena chinachake, kachitidwe kena. Oh, bwenzi langa, ndiloleni ine ndikuchenjezeni inu, monga m’bale wokondedwa amene amakukondani inu. Mvetserani mwatcheru.

<sup>315</sup> Tsopano, Adamu woyamba anatuluka ndi Eva, chifukwa iye ananyengedwa. Koma, pakhala pali winawake kuno mu Laodikaya uyu, iye ankadziwa mosiyana. Inde, bwana. Chifukwa iye anamuchotsa Iye pakama pake, chipinda chake, sh-...Iye anali panja, akugogoda, akuyesetsa kuti abwerere mkati. Komabe iye anali atapeza chikhaliidwe, iye anali atayikidwa pamwamba. Iye anali, oh, mai, “sankasowa kanthu,” iye anati, koma sanadziwe kuti iye anali wamaliseche, womvetsa chisoni. Umenewo ndi mpingo umene umanyenga osankhidwa omwe ngati kukanakhala kotheka. Zindikirani, iye anali ndi mphamvu, mphamvu yabodza. Iye anatenga gawo la Mawu, sanatenga ena onse a Iwo.

<sup>316</sup> Kodi bodza lalikulu kwambiri limene linayamba lanenedwapo ndi liti? Ilo linali ndi nainte naini peresenti ya Choonadi mwa ilo. Ngati wina ananena “William Branham, pa tsiku ili, anali uko ku Houston, Texas, ataledzera momwe iye akanathera.” Limenero ndi bodza. Mukuona? “Oh,” kunena, “ayi, iye anali ku Phoenix, Arizona. Iye anali akulalikira kwa amuna azamalonda Achikristu, iye analalikira pa phunziro linalake, anthu ochulukana anali kumeneko, iwo anamvetsera mpaka pafupifupi hafu pasti teni. Ndipo, pa hafu pasti teni, inu mukudziwa chimene iye anachita? Anafikira pansu ndipo anakatenga chakumwa choledzeretsa, ndipo anamwa icho.” Tsopano limenelo ndi bodza. Zina zonsezo zinali zooni. Mwaona, izo zikuyenera kuwoneka ndendende basi monga Choonadi, kuti zikhale zonyenga.

<sup>317</sup> Umo ndi momwe anthu amachitira lero. Iwo amakhala ndi zochulukana za Choonadi, iwo amanyenga osankhidwa omwe... Koma, Mawu amodzi, ndizo zonse zimene zimatengera. Ndipo ine ndatsimikizira zimenezo mwa Baibulo.

<sup>318</sup> Zindikirani, Iye sanatuluke konse ndi iye. Iye anamutulutsa Iye kunja, Mawu, anamukana Iye. Tsopano awa ndi mawonekedwe omvetsa chisoni, pamene ife tidzafika kumapeto.

<sup>319</sup> Chimodzimodzi monga momwe zinaliri ku Babulo,

munthu sangasiye chirichonse chimene iye akuyesetsa kuti achikwaniritse yekha. Iye sangasiye basi. Monga mmasiku a Nowa, zinalibe kanthu kuti Nowa analalikira ndi kuchenjeza mochuluka chotani, sizinachite ubwino mpang'ono pomwe. Mmasiku amene Ahabu, iye akuyenera kupanga mkate wake wake kuti adzitumize yekha ku gehena. Ndizo ndendende. Iye akuyenera kupanga mkate wake wake kuti adule cholumikiziracho, kuti chidzamtumize yekha ku gehena. Chimodzimodzi monga Ahabu ndi Yezebeli. Iwo, koma, chinthu chake ndi chakuti, iwo sankaganiza kuti iwo akuchimwa. Iwo ankaganiza kuti amachita zolondola.

<sup>320</sup> Inu mukudziwa, Yesu anati, “Zidzafika podzachitika kuti iwo mpaka adzakuphani inu, poganiza kuti akumuchitira Mulungu ntchito.” Dikirani mpaka bukhu langa latsopanoli litatuluka. Iwo anawombera pa anthu ena, usiku wina, chifukwa chonena kuti kunali kulakwa kuyanjanitsa mpingo wa Roma Katolika ndi Achiprotestanti. Zipolopolo zitatu zinadutsa mu nyumbayo, ya mzanga wa ine, zinangowaphonya iwo pang'ono. Dikirani mpaka bukhu ili liyambe kuzungulira. Samaganiza kuti iwo akuchimwa; iwo amaganiza kuti akuchita chinthu choyenera. Iwo amaganiza kuti iwo—iwo akuchita izo kwa cholinga cha Mulungu, osadziwa izo.

<sup>321</sup> Ayuda anamupha Yesu, akuganiza kuti iwo ankachita chinthu choyenera, chifukwa chiphunzitso chawo cha mpingo chinati Iye ankalakwitsa. Oh, ananena kwa iwo Iye... “Iwo anapachika Mkate womwewo umene iwo ankayenera kuti azikhalira nawo moyo.”

<sup>322</sup> Tsopano, ndiye, “Onse amene anamulandira Iye kuti akhale Moyo wawo, Moyo Wamuyaya, iwo amakhala moyo mwa Iye, ndipo Iye anawapatsa iwo mphamvu kuti akhale gawo la Iye, ana a Mulungu.” Nkulondola uko?

<sup>323</sup> Iwo amakonda mphonda zakuthengo, imfa mu mphodza, yochokera ku sukulu ya zaumulungu zawo. Iwo sakumufuna Yesu, Mkate wa Moyo. Iwo sakumufuna Iye. Iwo anamuchotsa Iye mu mpingo wawo. Iwo akuyenera kuchita zimenezo. Sindisamala zimene iwo akuchita.

<sup>324</sup> Inu mukuti, “Inu mukuganiza kuti musintha izo, M'bale Branham?” Ayi, bwana. Koma ine ndikuyankhula kwa Osankhidwa.

<sup>325</sup> Iwo anamutulutsa Iye kunja. Chifukwa chiyani? Iwo anatenga mphodza zawo, zosakanizidwa ndi dziko, malingaliro ena a chinachake, ndipo anazisakaniza izo pamodzi, ndipo anapanga mphodza ya seminare ya zaumulungu. Ndipo iwo anakana chakudya cha mneneri Eliya kuti chichize izo.

<sup>326</sup> Kodi iwo anachita zimenezo mu tsiku limenero? Eliya anali ndi chakudya china. Ufa umenewo unali Khristu, nsembe yaufa, zonse zoperedwa mofanana. Choperera chirichonse

chinkayenera kukhala chofanana, kuti apere izo. Ndipo iye anaponyera izo mmenemo, ndipo izo zinachiritsa matenda awo, kapena imfa yawo mu mphika.

<sup>327</sup> Koma lero iwo ali ndi imfa mu m'mphika, ndipo sakufuna Chakudya cha Eliya, Khristu, Mkate, Mawu. "Ayi, bwana! Ndi mpatuko!" Iwo sakuwafuna Iwo. Pitirirani ndi kumadya izo, ndipo inu mudzafa motsimikiza basi monga dziko. Muli chiphe mumphikamo. Iwo sangavomereze Chakudya ichi (ayi, bwana) mu miphika yawo ya zaumulungu. Iwo sangachite basi zimenezo. Tsopano iwo adzakuchotsani inu mu izo, iwo sakufuna kanthu kochita ndi izo.

<sup>328</sup> Tsopano Eva wachiwiri, njere ya mkate, anali Pentekoste, anachita monga woyamba, mkate Adamu, anapita mu imfa pansa pa zoperera za Chiroma, pansa pa chizunzo, kufera.

<sup>329</sup> Koma mlongo wake amene anadzakhala hule, (kodi icho ndi chimene Baibulo limanena?) uko nkulondola, kodi iye anachita chiyani? Iye anapitirira mpaka ku dziko ndipo anabala ana. Ndani anganene "ameni" kwa zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chivumbulutso 17, "Hule ndi ana ake aakazi," osati mwamuna; akazi, mipingo. Achipembedzo, nchiyani chinamupanga iye kukhala hule? Iye anakana Mawu ndipo anatenga chipembedzo, iye anadzakhala hule. Kodi ana ake anachita chiyani? Iwo anali timahule, chimene chiri chinthu chomwecho. Anachita chinthu chomwecho, anakana Mawu ndipo anawatengera ku chipembedzo. "Ana ake," ana aakazi, mipingo, yang'anani pa iwo.

<sup>330</sup> Tsopano ndiloleni ine ndinene ichi, mu uneneri. Kodi inu mumvetsa? Mkangano waukulu wa m'banja watsala pang'ono kutha. Onse akubwerera pamodzi. Amayi okalamba atenganso ana awo. Iwo onse ndi ofanana, mulimonse. Iwo akufuna kukhala mmodzi. Ndi nthawi yoti Mpingo ndi Mulungu, Mpingo ndi Mawu, zikhale mmodzi, pomwe pano, chifukwa icho ndi chimene Iye akubwerera; osati gulu "limodzi" monga choncho. Ayi, bwana.

<sup>331</sup> Njere ya tirigu ikuyenera kukhala. Tsopano yang'anani chirengedwe, ndipo tikutsekera pa lingaliro ili. Penyani chirengedwe. Munthu amabzala tirigu.

<sup>332</sup> Iwo analemba bukhu, ine ndikuganiza inu nonse munaliwerenga ilo, mwinamwake ena a inu azaumulungu, lotchedwa *Mulungu Wachete*. Ndikuganiza kuti mukhoza kulipeza ilo—mmabukhu anu, a—a kumene mumagulitsa mabukhu, masitolo ogulitsa mabukhu. *Mulungu Wachete*, ananena momwe...Munthu wachikunja, anati, "Kodi mungayembekezere bwanji kuti kuli Mulungu, amene akanakhala pamenepo mu Mibadwo Yamdima ndi kumawawona ana aang'ono akuphedwa, ndi moto; akazi, tsitsi lawo lalitali litagwera pansa mu phula, ndi kumawotchedwa; kumangirira

ng'ombe pa dzanja limodzi, ndi ina pa winawo, ndi kuwakhazula iwo pakati, chifukwa iwo samapsyopsyona mtanda; ndi zinthu zonsezo monga choncho?" Anati, "Mulungu akanatha bwanji, ngati akanakhalapo mmodzi, kukhala pamenepo ndi kumawawona ana aang'ono amenewo akuwotchedwa?" Mwaona, ndiwo malingaliro achirengedwe, achithupithupi. Mukuona?

<sup>333</sup> Penyani, kodi inu mukudziwa kuti tirigu, pamene iye alowa mu nthaka, iye amayenera kukhala mmenemo ndi kuvunda? Ndicho chimene mpingo wa pentekoste umenewo un kayenera kuchita, kukhala pamenepo ndi kulowa pansu, ndi kufa. Iwo un kayenera kuvunda, kuti ubale Moyo kachiwiri. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Tsopano penyani, ndipo tsopano awa ndi malingaliro anga otsekera. Tsopano kuti ndimalizitse zonsezo, tiyeni titenge chirengedwe. Ndi angati a inu mumakhulupirira kuti Mulungu amagwira ntchito limodzi mu chirengedwe, kwa zinthu zonse? ["Ameni."]

<sup>334</sup> Iye, penyani, Iye anachita dziko. Iye akuwombola dziko monga momwe Iye akumuwombolera munthu. Kodi munthu amakhulupirira chiyani? Iye amakhulupirira, kenako amabatizidwa; kenako iye amayeretsedwa ndi magazi, kuyeretsedwa, umene unali uthenga wa Wesley; kenako iye amadzazidwa ndi Moto wa Mzimu Woyera, umachotsa dziko mwa iye, ndipo iye amadzazidwa ndi Mzimu, amene ali Mawu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Tsopano penyani chiyani. Mulungu adzawombola dziko Lake mwanjira yomweyo.

<sup>335</sup> Ndi angati amene ali ndi—a—*Kwawo Kwamtsogolo Kwa Mkwatibwi Ndi Mkwati*, pa tepi? Mwaona, ine ndinazibweretsa izo mmenemo. Ambuye anapereka izo kwa ine. Ine ndimawupereka iwo kwa inu monga momwe Iye akundipatsira ine.

<sup>336</sup> Penyani, chinthu choyamba, dziko linatsutsidwa, pansu pa kugwa kwa Adamu ku Mawu. Kulalikira kwa Nowa kunabweretsa kulungamitsidwa, ndipo Mulungu analibatiza dziko lapansi ndi madzi; kenako motsatira panadzabwera Mwana ndipo anagwetsera Mwazi Wake pa iwo, kuti ayeretse iwo, kuti adzitengere iwo kwa Ake Omwe; ndiye potsirizira pake, kukonzanso, udzakhala moto umene udzapsereze kachiroambo kalikonse, china chirichonse, iwo udzapita kwa mailosi masauzande mmwamba, mu mlengalenga.

<sup>337</sup> Ndipo kenako chiyani? "Ine ndinawona Kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano, kumwamba koyamba ndi dziko lapansi zinali zitapita. Ndipo ndinawona Mzinda Woyera, Yerusalemu Watsopano ukutsika kuchokera kwa Mulungu, kuchokera Kumwamba, wokongoletsedwa ngati mkwatibwi kwa iye. . . wokongoletsedwa ngati mkwatibwi kwa

mwamuna wake, mwaona, ukubwera pansi pa dziko lapansi.” Kenako Mulungu ndi munthu. . .

<sup>338</sup> Chinthu chomwecho ndi Yesu, penyani, pamene Iye ankabatizidwa mmadzi, ndipo anapanga kukonzekera Kwake. Iye anayeretsedwa, kuyamba ndi kuyamba, ndi Atate; kenako Iye anakweza mmwamba manja Ake, ndipo apa panabwera Nkhunda pa Mwanawankhosa. Kodi Mulungu anali akuchita chiyani pamene Iye anayika Nkhunda Pamenepo? Iye ankadzitengera gawo limenelo la moyo; ilo—ilo linali gawo la dziko lapansi, Yesu kuti azidya chakudya monga ife timachitira, mkate wachibadwa. Koma tsopano Mulungu akulitenga ilo, palibe chirichonse chimene chiti chiletse izo. Imfa siyingaletse izo. Anati, “Phwasulani Kachisi uyu, Ine ndidzamuwukitsanso Iye.”

<sup>339</sup> Ndipo pamene mwamuna ndi mkazi alowa mwa Mulungu, athunthu tsopano, osati pansi pa kuwombeza kwina, osati pansi pa kutengeka kwina, koma kwenikweni pamene Mawu ndi Iye akhala mmodzi; Mulungu wamupulumutsa munthu ameneyo, amuyeretsa iye ku zinthu za dziko lapansi, kukonzanso chirichonse cha mdziko chitalikirane ndi iye, ndi Moto wa Mzimu Woyera, ndi kumakhala mwa munthu ameneyo, kumadzinyezimiritsa Yekha, mwamuna wangwiro uja kapena mkazi akukhala moyo mwa Mawu. Mwaona, limenero ndi dziko lapansi limene layeretsedwa. Iye adzagwiritsa ntchito dziko lapansi mwanjira yomweyo, Iye akuliwombola ilo.

<sup>340</sup> Tsopano penyani, njere ya tirigu imagwera mu nthaka. Tsopano, Yesu anali njere ya tirigu imeneyo imene inagwera mu nthaka, imene itatha kupangidwa kukhala yangwiro, Iyo inali ndi Moyo mwa Iyo. Mose sanawuke. Adamu sanawuke. Palibe aliyense wa iwo amene anawuka. Koma Mmodzi wangwiro uyu amene ankanyezimiritsa Mawu mwa njira iliyonse, Mawu aliwonse amene Iye ankakhala nawo moyo! Ndi angati angati “ameni” pa zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Mawu aliwonse amene Iye ankakhala nawo moyo. Chinachitika ndi chiyani? Iwo anamuika Iye mmanda. Koma, masiku atatu, Iye anawatsegula iwo ndipo anatulukamonso. Mukuona?

<sup>341</sup> Tsopano apa pakubwera mpingo kachiwiri, mwaona, ukubwera kwa Mmodzi wangwiroyo, ku Mkwatulo kachiwiri. Tsopano chinachitika ndi chiyani mpingo utagwera mu nthaka ku Nicaea, Roma, kwa bungwe loyamba? Kodi winawake angati “ameni,” kuti uko nkulondola? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Kodi iye anachita chiyani? Iye anatuluka kachiwiri mu chiwukitsiro chakanthawi, Iye anayesera kudzera mwa Luther mofanana monga Iye anachitira kudzera mwa Nowa. Koma kodi iye anachita chiyani? Iye anawalephera Mawu, iye anapanga bungwe. Kodi izo zinachita chiyani?

<sup>342</sup> Ziri ngati njere ya tirigu ikuphuka. Pamene njere ikuphuka,

chinthu choyamba chimene chimabwera ndi chiyani? Mphukira ziwiri zazing'ono. Tsopano mvetserani mwatcheru kwenikweni. Chimabwera ndi chiyani, mwachibadwa tsopano? Ife titsatira zachirengedwe ndi zauzimu, mkate wachirengedwe ndi mkate wauzimu. Chimachitika ndi chiyani? “Zingatheke bwanji kuti Munthu yuyu akhale Mkate?” Penyani.

<sup>343</sup> Pamene mpingo unadza, iwo unali tsamba limodzi laling'ono. Tsopano izo sizinawoneke ngati njere imene inalowa mu nthaka, nkomwe, koma ndi chonyamulira cha moyo. Mukuona? Tsopano chimachitika ndi chiyani? Tsopano munthuyo amati, “Oh, ine ndiri ndi munda wabwino wa tirigu.” Osati panobe. Mwakuyankhula kwina iye ali nawo. Chinachitika ndi chiyani? Wotsatira amene anabwerapo anali Zwingli, uko kunali kusuntha kwina kumene kunabwera pambuyo pa Luther. Komabe izo sizinali zimenezo. Ndi tsamba. Kenako phesi linatulutsa masamba ambiri, monga ngati Kalvini, ndi ena otero, anatulukira. Potsiriza mpingo wa Anglican unawuka, masamba onse. Mwaona, onse a iwo ofanana chimodzimodzi basi, chinthu chomwecho.

<sup>344</sup> Kenako chinachitika ndi chiyani? Tirigu amasintha, ndipo chimanga chimasintha, ndipo chirichonse chimasintha. Chimene chinabwera chinali ngayaye. Inu mukhoza kuchiticha icho ngayaye. Chabwino, pamene icho chinatero, yang'anani chimene chapachikidwa pa icho, mungu waung'ono. Tsopano izo zimawoneka mochuluka pang'ono monga njere yapachiyambi imene inalowa pansu, kuposa momwe tsamba linachitira. Nkulondola uko? Chabwino, uthenga wa Wesley unali pafupi kwambiri ndi Baibulo kuposa wa Luther. Inu mukudziwa zimenezo. Nkulondola uko? Kodi ngayaye zazing'ono zonsezo ndi chiyani tsopano? Apo panali Amethodisti Achiwesley, Anazarene, Pilgrim Holiness, United Brethren, onsewo pansu pa kuyeretsedwa. Ndipo chinabwera kuchokera pamenepo ndi chiyani? Ichu, potsiriza, chinachita chiyani? Kupanga bungwe, kufa!

<sup>345</sup> Chimene chinatuluka mmenemo chinali Apentekoste. Inu mukuti, “Oh, m'bale!”

<sup>346</sup> Tsopano molemekeza, ndipo ine ndikunena ichi ndi chikondi chaumulungu. Ndipo mulole Atate Wamkulu Amene ine ndangokuuzani inu kumene, pachiyambi, analipo pano, wopezeka ponseponse. Ngati ine ndinganene izi mwa tsankho, ndiye Iye adzandiweruza ine. Ngati ine ndinganene izi mu Choonadi, Iye adzandidalitsa ine. Iye adzakulolani inu kuti muwone Ichu, ngati inu munadzozedwera ku Moyo.

<sup>347</sup> Pamene njere yaing'ono yoyamba ya tirigu itulukira pa phesi la tirigu, iyo mwamtheradi imawoneka ngati njere. Nkulondola uko? Koma iyo ndi chiyani? Iyo si njereyo. Ameneyo ndi Mateyu 24:24, “zoyandikana kwambiri mwakuti izo zikananyenga

osankhidwa omwe ngati kukanakhala kotheka.” Zindikirani, izo zimawoneka ngati njere. Koma inu mukakoka icho ndi kukhala pansu, ndi kutenga galasi loyang’anira ndi kuyamba kukokera mmbuyo. Ndi mankhusu chabe pa chimanga, kapena mankhusu pa tirigu. Iwo anangotero kuti ayiteteze iyo, koma izo zimangawoneka mofanana basi ngati njere. Tsopano ndi angati amadziwa kuti izo ndi zoonza, kwezani manja anu? Ndithudi. Koma ndi mankhusu.

<sup>348</sup> Tsopano, abale Achipentekoste, musandimve ine molakwika, koma ichi ndi Choonadi. Simungathe kunyoza chirengedwe. Ndipo chirengedwe chimamulengeza Mulungu mu chirichonse, Mlengi wake.

<sup>349</sup> Tsopano tayang’anani pa mankhusu amenewo. Iwo akuwoneka...Kodi iwo anachita chiyani? Iwo anayankhula mmalirime. Iwo amachita chimodzimodzi basi monga iwo anachitira pa Pentekoste. Koma ngati inu mungaidule iyo, kutenga kanthu kakang’ono kameneko ndi kukakokera mmbuyo, iyo ili ndi mankhusu aang’ono ambiri mwa iyo. Ndipo pamene inu muyikokera iyo mmbuyo, inu mumaona mmbuyo kumbuyo kutali, inu mukuyenera kukhala ndi galasi labwino, loyang’anira mmbuyo uko. Pali kamphukira kakang’ono ka njere kakubwera, apo pali chinthu chenicheni. Ichi nehonyamulira. Chifukwa chiyani? Iwo akuyenera kukhala pamenepo kuti ateteze njere imeneyo. Izo zikugwira ntchito mogwirizana, koma ndizoti ziteteze njereyo. Tsopano pamene njere inabwera kuchokera mu nthaka, kudutsa mwa Achilutera, kudutsa mmipingo imeneyo, kudutsa mwa Wesley ndi kudutsa uko, kudutsa mu ngayaye, ndipo tsopano kutsika mpaka mmankhusu. Tsopano zikungowoneka mwangwiro basi. Nzosadabwitsa Yesu anati, “Izo zikanadzanyenga osankhidwa omwe ngati kukanakhala kotheka.” Amawoneka ngati njere basi, pamalo kumene amene njere ikuyenera kukhalapo, koma chinachitika ndi chiyani? Iwo anachita chinthu chomwecho chimene ena anachita izo zisanachitike, anapanga bungwe! Kodi iwo anakhala chiyani? Chonyamulira.

<sup>350</sup> Tsopano mmasiku amene ife tikukhalamo, wazambiriyakale aliyense pano akudziwa kuti chitsitsimutso chirichonse chimangokhala pafupifupi zaka zitatu, ndipo kenako kuchoka mu chitsitsimutso chimenecho pamabwera bungwe. M’bale, mlongo, mu chitsitsimutso chachikulu ichi cha zaka fiftini chimene ine ndakhalamo, ndakhala ndi mwayi kukhala nacho ndi inu, sipanakhale bungwe lochoka mu icho. Palibenso mabungwe. Sadzakhalaponso. Apo pali wotsiriza. Tsopano, Chipentekoste chinkayenera kukhala pamenepo kuti chitetezere ichi. Kodi ife tikanapita kuti ndi Uthenga wonga uwu ngati pakanati pasakhale wa Chipentekoste kuti awukhulupirire iwo? Tsopano bwererani ku Mtsinje wa Ohio, mu 1933. Mukuona?

<sup>351</sup> Mukhululukire ichi, koma ine ndikufuna kuti inu mudziwe

Choonadi. Ndipo ine ndiribe nthawi yochuluka imene yatsala, inu mukudziwa izo, ine ndiri fifite-faivi. Koma matepi awa adzakhallabe moyo pamene ine ndapita, ndipo inu mudzawona ngati ziri zolondola, kapena ayi, ngati ine ndiri wantchito woona kapena mneneri wabodza. Ine sindinakuuzenipo inu kalikonse koma chimene chinachitika, chomwechonso izi zidzachitika.

<sup>352</sup> Ndi chonyamulira. Izo zinkayenera kutero. Koma pamene tirigu uja ayamba kukula, monga mpingo poyamba unali chonyamulira kwa Yesu, koma pamene Iye anayamba kuwauza iwo Choonadi cha Mulungu, iwo analekana ndi Iye. Tsopano chikuchitika ndi chiyani? Palibe mgwirizano. Chifukwa chiyani? Izo zikuyenera kukhala mwanjira imeneyo, kuti tirigu athe kukhala pamaso pa dzuwa, d-z-u-w-a, ndipo chotero tirigu wauzimu akhoza kugona pamaso pa M-w-a-n-a, kuti akhale njere ya golide ya Mawu, mwaona, kupangidwa Mawu, Mulungu atсандulika thupi, wotsimikiziridwa. A... “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuchita iyenso adzazichita.” Mpingo umene umakhala moyo mwa Mawu amenewo, kolondola, osati kupyolera mu bungwe, koma mu Kukhalapo kwa Mawu, Mwana, iwo umakhala (chiyani?) Mawu omwewo amene anapita pansu pa Tsiku la Pentekoste.

<sup>353</sup> Tsopano, kodi Malaki 4 samatiphunzitsa ife, kuti tsiku lalikulu ndi lowopsya la Ambuye lisanadze, kuti izi zidzachitika? Ndi angati akudziwa zimenezo? “Ndipo Iye adzabwezeretsa mitima ya ana kwa atate,” nkulondola uko, “Chikhulupiriro cha makolo achipentekoste apachiyambi.”

<sup>354</sup> “Ndipo mu tsiku limenero,” Luka 17:20, ine ndikukhulupirira ndi choncho, Yesu anati, “pamene Mwana wa munthu adzawululidwa,” osati amuna. “Mwana wa munthu,” osati bungwe. “Mwana wa munthu,” Mawu akudzikhala moyo Okha kachiwiri pakati pa anthu! Mukuona?

<sup>355</sup> Mawu, Iwoeni, atсандulika thupi mwa inu, inu ndi chinyezimiro cha ora lino, Uthenga, chinyezimiro cha iwo. Mwaona, inu mukukhala moyo kachiwiri, khalani Moyo umene unali mwa Yesu Khristu. Inu muli mu Kukhalapo kwa Mwana. Kenako kwa . . .

<sup>356</sup> Kodi chimachitika ndi chiyani kwa iwo? Chimachitika ndi chiyani kwa Mpingo umenewo? Potsiriza, mvetserani, mankhusu amenewo amachoka kwa tirigu ameneyo, pamene iye akuyamba kuwonetseredwa. Chinachitika ndi chiyani? Moyo umene unali mu mankhusu, unapitirira kutuluka kukalowa mu tirigu. Moyowo siwusinthu. Zonyamulira zimasinthu, iwo amapanga chipembedzo; mwaona, masamba, ngayaye, mankhusu. Koma tirigu sangasinthu. Iye akuyenera kukhala utumiki ndendende basi pa Mawu monga Iye anali pa Mawu, ndipo monga Mpingo woyamba unali pa Mawu, wodzazidwa ndi Mzimu, wodyetsedwa Mawu; osati wodyetsedwa chipembedzo. Odyetsedwa Mawu!



357 Tsopano pali chirengedwe, ndi Mawu a Mulungu. Iye ndi Mkate umenewo. “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.”

358 Ndikutseka tsopano, tisanati tipemphere. Zindikirani apa, apa pakubwera chinthu chimene ine ndikufuna kuchinena.

359 Tsopano mankhusu amenewo akuyenera kuchokapo kwa tirigu ameneyo, amene ali mu chisamaliro cha Mulungu. Ndi angati akuti “ameni”? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Mankhusu akuyenera kuchoka kwa tirigu, chifukwa iye akukhwima tsopano. Iye wayima. Tsopano, mankhusu amenewo sanali pamenepo, iwo anali othandizira, iwo anali chonyamulira cha Moyo, kenako Moyo kuchokera mmenemo unatuluka kukalowa mu tirigu. Tsopano, ndicho chifukwa chake.

360 Mvetserani, abwenzi, ndi tsiku lanji limene ife tikukhalamo? Ife takhalapo nacho chitsitsimutso cha zaka fifitini. Ndi angati angati “ameni” kwa izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ndi bungwe liti limene linawukapo? Palibe. Iwo anayetsa kuti andipangitse ine ndipange bungwe, anati, “Kodi inu mungapange bungwe, M’bale Branham, pa utumiki wanu? Ilo lidzakhala. . .” Tsopano, osati ine, ine sindikukamba za ine. Ine ndikukamba za Uthenga wa ora, wa tsikuli.

361 Ndipo iwo anapita uko mu Canada ndipo anakapeza abale angapo a mvula ya masika. Ilo linafera pomwepo. Mukukumbukira mvula ya masika, abale inu? Kodi izo zinapita kuti? Kodi chirichonse chinapita kuti? Koma kodi bungwe linapeza chiyani kuchokera mwa izo? Mamiilioni a otembenuka, ndipo anapanga akapolo kuchokera mwa iwo, kupita ku tizikhulupiriro tawo, anadzakhala olemera, ndi kumanga mamillioni ndi mabillioni a madola mu nyumba ndi zinthu monga choncho, ndi kumati “Ambuye akubwera,” kumatumiza alaliki ku maseminare ndi zinthu, ndi kumawaphunzitsa iwo pa zaumulungu zopangidwa ndi anthu, monga Luther, Wesley, ndi nonse a inu. Iwo anadzakhala mankhusu.

362 Koma, zikomo Mulungu, njereyo ikupitirirabe. Ndiye ngati izo ziri zoonza mwa Mawu, kumene ife tikukhalako, izo nzoona mwachirengedwe, izo zatsimikiziridwa, njere ya tirigu, njira iliyonse, kodi ife tikhala motalika bwanji? Inu mukudziwa chiyani? Ine ndikumva kubwera kwa chokololera, World Council, icho chidzalekanitsa izo. Kodi iye akutani? Kumusenga iye kuyambira pa phesi lake. Koma Iye ali ndi chonyamulira chikumuyembekezera Iye. Iye adzapita Kwawo, umodzi wa mmawa uwu. Oh, inde. Inu mukumvetsa, nenani “ameni”? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi].

363 Ine ndikudziwa kuti dziko silimakhulupirira zimenezo. Iwo sangakhulupirire izo. Sikuti. . . Ndikungowamvera chisoni iwo,

chifukwa, “Palibe munthu angadze pokhapokha Atate Anga atamukoka iye; ndipo onse amene Atate Anga andipatsa Ine adzadza.” Ngati dzina lake liri pa Bukhu la Moyo, iye ndithudi adzawazindikira Mawu. Iye akuyenera kutero, izo zachitika motalika kwambiri. Izo zatsimikiziridwa mwangwiro kwambiri, mpaka izo ndi motsimikizika Choonadi.

<sup>364</sup> Ife sitidzakhalanso ndi mabungwe enanso, koma mabungwe onse adzalowa mu limodzi. Kodi iye ndi wabwino kwa chiyani? Kupita... Pakuti kodi iwo amachita chiyani ndi udzu? Amawuwotcha iwo. Yesu anati, “Angelo adzabwera kudzasonkhanitsa tirigu mu nkhekwe.” Ndipo chidzachitike ndi chiyani? “Mapesi, ndi ziputu, ndi zisoso, zidzathedwa ndi moto wozazimitsika.” Inu mukuona? Ndipo chimene chikuyenera kuchitika koyamba ndi chiyani? Angelo anapita ndipo anakamanga namsongole poyamba. Nkulondola uko? Mwaona, iwo akudzimanga okha pamodzi mu bungwe limodzi lalikulu kwambiri, palibenso mabungwe.

<sup>365</sup> Tirigu ali pano. Matamando akhale kwa Mulungu, tirigu ali pano. Khristu ali pano. Iye akutsimikizira Mawu Ake, Iwo ndi Choonadi. Tirigu ali pano, akukhwima tsopano, akugona mu Kukhalapo kwa Mwana.

<sup>366</sup> Sikuti munthu aliyense angawagwire Iwo, iwo onse akuchokapo, “Ife sitidzakhala ndi chochita ndi Iwo.” Inu mukuyenera kuchita zimenezo.

<sup>367</sup> Oh, m’bale, lowani mu tirigu, mulole Moyo wanu umene uli mwa inu utulukire mu tirigu. Kodi mutero? Khulupirirani Mulungu. Musati... Mungokhala ndi Mulungu. Kodi mukutsimikiza kuti mukwanitsa izo? Bwanji ngati winawake akanati. . . Ine sindikusamala.

<sup>368</sup> Monga nkhani imene ndinawerenga, nthawi yina. Panali dokotala, iye anali munthu wabwino, ndipo iye anakonda anthu osauka. Ndipo nthawi iliyonse imene osauka samatha kulipira ngongole zawo, inu mukudziwa chimene iye anakachita? Iye amangosayina mu inki yofiira, kuti, “Iwe wakhululukidwa.” Potsiriza, dokotalayo anamwalira. Ndipo pamene dokotalayo anamwalira, mkazi wake anali wamwano. Iye anali wosiyana, monga mpingo lero. Iye anapita ndipo anakawapera onse pamodzi. Iye anabweretsa mlandu, ndipo anawaponyera onse mu khoti, “Inu mulipira ngongole izi, mulimonse!”

<sup>369</sup> Koma woweruzayo anatengapo zikalata zina, anati, “Bwerani kuno, amayi.” Iye anati, “Kodi inki yofiira iyi ndi siginecha ya mwamuna wanu?”

Iye anati, “Inde, bwana, ndi imeneyo.”

<sup>370</sup> Anati, “Palibe khoti mu dziko limene lingawasumire iwo. Iwo ndi mfulu.”

371 Aloleni iwo anene chimene akufuna. Iye anasaina Mawu Ake ndi Magazi Ake Omwe. Palibe chimene chingachotse icho kwa ife, m'bale. Ndife mfulu.

372 Tiyeni tipemphere. Ndithudi inu. . .

[M'bale mwa osonkhana akupereka chilimbikitso. Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. Amen.

373 Tsopano ndi mitu yanu yoweramitsidwa. Ngati ndikumvetsa, wina anauka pakati pa iwo, mmasiku a mfumu, ndipo anapereka ulosi, kumene iwo akanati adzakumane ndi mdani ndi kuwawononga iwo. Tsopano, ngati ine ndingamvetse zimenezo molondola, alipo malo amodzi oti mukumane ndi mdani wanu, ndiwo pa Mawu. Ndi kumene iye akuyesera kuti akumane nanu inu. Inu mukakumana naye kumeneko ndi PAKUTI ATERO AMBUYE.

374 Ndi angati muno, ndi mitu yanu yoweramitsidwa, (yayandikira kwambiri pakati pa masana, ndiribe nthawi yoitanira kuguwa koma ichi basi) mungakweze manja anu, ndi mitu yanu yoweramitsidwa, maso anu ali otsekedwa, "Ine ndikufuna kuti ndikhale gawo la Iye. Ine ndikufuna kuti ndidzilumikizitse ndekha ndi Iye ndi Mawu Ake. Ziribe kanthu chimene chiti chibwere kapena kupita, chimene dziko likunena, ine ndikufuna kukhala gawo la Iye," kwezani dzanja lanu ndi kunena, "Ine ndikutero"? Mulungu akudalitseni inu. Handirede peresenti, ine ndikuhulupirira.

375 Ndi mitu yathu yoweramitsidwa, pamene ife tikulingalira, tiyeni ting'ung'udze mwakachetechete nyimbo yang'ono iyi tsopano. Aliyene akupemphera.

Chodala chikhale Chimango chimene  
chimamanga (Amenewo ndi Mawu.)  
Mitima yathu mu chikondi cha Chikhristu;  
Chiyanjano cha malingaliro achibale  
Chiri chonga chija Chakumwamba.

"Monga Ine ndi Atate Anga tiri mmodzi, inu ndi mmodzi ndi Iye, nanunso."

Pamene ife tisiyana,  
Zimatipatsa ife ululu wamkati;  
Koma tidzalumikizanabe mu mtima,  
Ndi kuyembekeza kudzakomananso.

376 Loweruka lotsatira mmawa ku Flagstaff, Arizona, Ambuye akalola, ine ndikuyembekeza kudzakumana nanu kachiwiri. Kodi mukumukonda Iye?

377 Tsopano ine ndingozisiya izo monga choncho, mwaona. Baibulo linati, "Ochuluka amene anamukhulupirira Iye, ndi ochuluka amene analandira Mawu." Mukuona? Sindinganene kuti ndi ndani kapena si ndani, izo ziri ndi inu. Koma ngati inu mukugwiritsitsa ku kachikhulupiriro kena kakang'ono, ena

a inu Amethodisti, Abaptisti, kapena Apentekoste, kapena aliynse amene inu mungakhale, amene mwagwiritsitsa ku chinachake chosiyana ndi Mawu amenewo, chonde, anthu anga okonedwa, chokani kwa zimenezo, lero. Sichoncho inu? Chokani kwa izo, ndipo mutembenukire kwa Iye. Musalole kuti Mawu amodzi akuchotseni inu ku chiyanjano cha Khristu. Mulole Mzimu Wake upereke izi.

<sup>378</sup> Atate Mulungu, anthu awa akhala pano kwa nthawi yaitali. Izo zikundikumbutsa ine za nthawi ina imene Paulo, akulalikira pa mzere womwewu, iwo unali Uthenga, iwo anakhala usiku wonse ndipo anamvetsera kwa iye, mnyamata anagwa kuchokera pa zenera ndipo anafa. Paulo anapita ndipo anakayika thupi lake pamwamba pa mnyamatayo, ndipo anati, “Moyo wabwerera kwa iye.” Tsopano, Atate, pali odwala ndi osautsika pano, pali iwo amene akusowa mapemphero a matupi awo. Ine ndikupemphera, Wokonedwa Mulungu, kuti musadikire mpaka msonkhano. Iwo sakuyenera kudikirira msonkhano uliwonse. Mawu nthawizonse ali pano, ndiwo Khristu. Ine ndikupemphera kuti Inu muchize aliyense wa iwo. Mulole aliyense wa iwo akhale wamphumphu kwathunthu, Mulungu. Perekani izi. Adalitseni iwo, kuyesetsa kwawo. Iwo sibwenzi atakhala pano, Ambuye, iwo sibwenzi akumvetsera kwa Iwo, ngati iwo akanati asakhulupirire Iwo. Tsopano, Ambuye, iwo akweza manja awo, iwo akuwakhulupirira Iwo, tsopano mulole Iwo alandire mmitima yawo, mtumiki aliyense, aliyense wa anthu. Wochimwa, mulole iye amulandire Khristu; wobwerera mmbuyo abwerere. Perekani izi, Atate. Madalitsa awa ife tikupempha mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye,

Iye anayika dzina langa mmenemo, zaka zambiri zapitazo.

. . . anayamba kundikonda ine

Nandigulira chipulumutso changa

Pa mtengo wa Kalvare.

<sup>379</sup> Inu mumamukonda Iye? Tsopano pamene tikuyimba iyo kenanso, ingofikirani pa tebulo ndi kugwirana chanza ndi winawake, mukuti, “Wokonedwa mwendamnjira, ndine wokondwa kukhala pano mmawa uno. Ine ndimakhulupirira Khristu. Sichoncho iwe?” Chinachake chonga icho, pamene tiziyimba kenanso.

Ine . . . ( . . . ? . . . )

. . . gulira chipulumutso changa


Pa mtengo wa Kalvare.

<sup>380</sup> Tsopano, kuyambira pano, kodi ife tathana ndi dziko? Kodi ife tathana ndi mafashoni a mdziko? Ndipo a . . . zonse zamkutu, ndi zonse izi apa zokongola, ndi kutenga Uthenga ndi kuwupanga chinthu chamalonda kuchokera mwa iwo, ndipo—ndipo ife tathana nazo? Sichoncho ife? Mungondipatsa

ine Yesu, ndizo zonse zimene ndikufuna. “Kumudziwa Iye ndi Moyo, kumudziwa Iye.” Ine ndimamukonda Iye. Kodi inu simukumukonda Iye? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Oh, momwe ife timamukondera Iye!

<sup>381</sup> Tsopano ine nditembenuzira msonkhanowu kwa M’bale Carl, ine sindikudziwa china chimene iye ati achite.

<sup>382</sup> Mulungu akudalitseni inu. Ndipo ine ndikuyembekeza kudzakuwonani inu kenanso Lamlungu likudzali, ndipo ngati ine sindingakuoneni inu . . . kapena Loweruka lotsatira. Ngati ine sindidzakuonani inu pamenepo, ndidzakuonani inu uko ku Tucson. Ngati sichoncho, ine ndidzakuonani inu kuno pa seventini. Ngati sichoncho, ine ndidzakuonani inu mu Ulemelero. Ameni.

<sup>383</sup> M’bale Carl tsopano, ine sindikudziwa chimene iye akufuna kuchita pa nthawi ino, M’bale Williams. 

64-1212 Nthawi Yokolola  
Ramada Inn  
Phoenix, Arizona U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)